

MAFUNSO NDI MAYANKHO



Tiyeni ife titsale chiimire kwa mphindi chabe kwa pemphero.

Wokonedwa Mulungu, ife tikukuthokozani Inu usikuuno, poyamba, chifukwa cha Yesu Khristu, Mpulumutsi wathu. Ife tikukuthokozani Inu chifukwa chakuti Iye ali chimodzimodzi dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha anthu amene amakhulupirira zimenezo. Ndife okondwa kwambiri kuti ife tiri naye Mulungu, osati kungokhala Mulungu womulingalira, fano lolingalira, mzimu woulingalira; palibe chimene chiri cholingalira pa izo—Mulungu woona ndi wamoyo amene akukhala nafe ndi mkati mwathu ndipo akugwira ntchito kudzera mwa ife. Si kupangira chosemedwa kwa Mulungu, koma ife kukhala mafano a moyo a Mulungu...Mzimu Woyera, osati kumayankhula kupyolera mu chosemedwa, koma kuyankhula kupyolera mu chipangizo chowomboledwa—Mulungu akuwonetseredwa mu thupi. Momwe ife tikukuthokozerani Inu chifukwa cha izi, Lawi la Moto lalikulu likutitsatira ife, kapena ife tikulitsatira Ilo, maka, ndi chifukwa cha mawonetseredwe onse aakulu a Mzimu womwewo ukuchita ntchito yomweyo imene Iwo nthawizonse wakhala ukuchita pamene Iwo ubwera pa dziko lapansi. Chitonthozo chake chomwe izo zimatipatsa ife.

² Ife tasonkhana usikuuno, Ambuye, osati kwa cholinga china koma kuti tidzadziwe ndi kuti tidzaphunzire, mwa thandizo Lanu, momwe tingakhalire Akhristu abwinoko ndi omvera oyenera kwa ora lino limene ife tikuliyandikira. Kodi inu simutithandiza ife, Ambuye; ife tikukusowani Inu. Mu Dzina la Yesu. Amen. (Inu mukhoza kukhala.)

³ Ndi pafupi mafunso ena sate kapena forte, i—ine sindikudziwa momwe ine ndingafikire konse kwa iwo. Ine ndinayesera molimba madzulo ano kuti ndiwone ngati ine ndingawafikitse iwo pabwinobwino, koma ine sindinathe kuti ndichite zimenezo. Koma ine ndikufuna kunena kuti ine ndichita mopambana kwambiri momwe ine ndingathere k—kuti ndiwayankhe mafunso awa, chifukwa iwo ndi mafunso abwino, akuchokera mu mitima ya Akhristu. Ndipo i—ine ndithudi ndikufuna kuti ndichite chirichonse chimene ine ndikuchidziwa momwe ndingawayankhire iwo mwanzere basi monga momwe ine ndikudziwira kuti ine ndiwayankhe iwo. Ndipo i—ine ndikufuna kuti ndiwathokoze Ambuye chifukwa cha momwe Iye anatithandizira ife mmawa uja potithandizira ife k—kuti tiwatenge mafunso awa n—ndi ku—mayankho amene Iye anatipatsa ife.

⁴ Tsopano, ine ndangowasakaniza iwo onse apa, ine ndikuganiza 150 ena. Ndipo ife tinafika kwa pafupi twente, ine ndikuganiza, mmawa uja. N—ndipo kotero tsopano, ife tisanayambe, ine ndimangofuna kunena kuti ngati aliyense akufuna kuti awone nkhani iyi ya *Mpingo Kugwedemuka pamene Ng’oma Zikulindima*, mtumiki wa Chipresbateria kuno akutsogolera osonkhana ake mu gwedemula, dongosolo la—sakaramenti. . . Ndiroleni ine ndingowona miniti yokha.

⁵ “Mamembala achinyamata avina kwa jazi—jazi. Sewero lakutengeka lifotokoza za m-p-h-i-p-h-i-r-i-t-s-o wamakono, roko andi rolo.” Abusa apa akuwatsogolera onse ausinkhu wa mmateni kumeneko ndi kudutsa mu kutengeka naye Khristu, kupachikidwa kukuseweredwa mwa roko andi rolo ndi jazi. Chabwino. . . Zimenezo ziri ku Maryland. Tsopano, kodi zimenezo si chinachake?

⁶ Ndiyeno, apa pali chithunzi cha ajawa. . . Ine ndimakuuzani inu mmawa uja za Mabitoloji, *Kubwerera kwa Mabitoloji*, ndipo apa pali zolembedwa; inu mungathe kuziwerenga izo kuchokera mu magazini ndi zinthu zonse zosiyana. “. . . monga izo zinaliri, ayambitsa chipembedzo chatsopano.” Tsopano, manenjala wawo. . . Ine ndiri ndi cholemba kuchokera mu pepala apa. Inu mulibe nthawi. . . Ngati aliyense akufuna kuti awerenge izi—kapena ine ndikhoza kuziyika izo pa bolodi la zolengeza, ndiye inu mukhoza kuziwerenga izo. Ndipo ine ndikungofuna kuti ndikusonyezeni inu ora limene ife tiri kukhalamo ndi zodabwitsa. Inu mwina mukhoza kusazimvetisa izo, koma, anthu, yeserani kuti muzimvetse izo, kuti—chomwe zinthu izi ziri! Ine ndamufunsa M’bale Capps—iye ali ndi maphunziro abwino ndipo iye akhoza kuwerenga bwino kuposa ine—ine ndamufunsa iye kuti awerenge nkhani iyi yochokera kwa manenjala wa Mabitoloji. Kodi inu mungathe kuchita izo, M’bale Capps, pa nthawi ino?

⁷ [M’bale Capps awerenga nkhani ya Mabitoloji—Mkonzi.] Akunena kuti:

Mabitoloji akuzidabwa okha ndipo sakupezapo mayankho. “Ndi zosaneneka, mwamtheradi ndi zosaneneka!” akutero Derek Taylor, wolengeza nkhani za Mabitoloji, “Apa pali anyamata anai ochokera ku Liverpool. Iwo ndi amwano; iwo ndi otukwana; iwo ndi olaula; ndipo iwo alilanda dziko. Izo ziri ngati kuti iwo ayambitsa chipembedzo chatsopano. Iwo ali kwathunthu otsutsakhristu. Ine ndikutanthauza, ine ndine wotsutsakhristu nanenso; koma iwo ali otsutsakhristu kwambiri mpaka iwo akundidabwitsa ine, chimene sichiri chinthu chophweka. Koma ine ndatengedwa nawo iwo. Kodi aliyense sali? Ine ndikutengedwa ndi kuonamtima kwawo, ndipo anthu

amene akuwakonda iwo kwambiri ndi anthu amene akanayenera kumakhala akukwiya nazo kwambiri.”

“Mu Australia, mwa chitsanzo, nthawi iliyonse ife timafika pa bwalo la ndege, izo zimakhala ngati deGaulle wafika, kapena bwinoko, apobe Mesiya. Misewu inali itandandidwa molimba. Olumala amatayira kwina ndodo zawo. Anthu odwala amathamangira mpaka ku galimotoyo, ngati kuti kugwira kochokera kwa mmodzi wa anyamatawo kukanawapangitsa iwo kukhala bwino kachiwiri. Azimayi okalamba amaima akuyang’ana ndi zidzukululu zawo pamene ife timadutsa apo. Ine ndimakhoza kuwona mawonekedwe pa nkhope zawo. Izo zimakhala ngati kuti mpulumutsi wina anali atafika ndipo anthu onse awa anali okondwa ndipo atamasulidwa, ngati kuti zinthu mwanjira inayake zikanati zikhale bwinoko tsopano.” Taylor anaimikira ndipo anasomeka ndudu mkamwa mwake, “Chinthu chokha chimene chatsalira kwa Mabitoloji,” iye anati, “ndi kupita pa ulendo wa machiritso.”

8 Kodi izo si zimene Iye ananena? “Ambiri adzadzwa kwa Ine mu tsiku limenelo ndi kuti, ‘Ambuye kodi ine. . .’” Mukuona? Tsopano, kodi inu simukuwona kuti inu simungaike chidaliro chanu mu misonkhano yokopa ya machiritso? Inu simungati muike chidaliro chanu mu mtundu uliwonse wa chizindikiro ngati chimecho. Chinthu chokha chimene inu mungaike chidaliro chanu ndicho PAKUTI ATERO AMBUYE wochokera mu Baibulo. Tsopano, Mpingo, apo ndi ndendende pamene ine ndayesera kuti ndikusungenipo inu, ana anga. Ndipo ngati chinachake chichitika kwa ine ndipo Mulungu nkundichotsapo ine pa dziko lapansi lino, musati inu mudzalephere konse. Muzikumbukira izi ndi mtima wanu wonse: khalani ndi Mawu amenewo! Inu musati muwasiye Mawu amenewo! Chirichonse chosiyana kwa Iwo, zisiyeni izo zokha, ziribe kanthu chimene izo ziri. Ndiye inu mudziwa kuti Iwo ndi olondola. Mukuona?

9 Msonkhano wokopa wa machiritso tsopano! Anthu ochimwa kwambiri amene akuwadabwitsa mamananjala awo omwe ndi zolaula zawo, ndi uve, ndi nyansi; ndipo anthu akumatayira kwina ndodo zawo ndi kumachiritsidwa pa kuyang’ana pa anyamata awa. Izo ndi zonyansa kwambiri, ndi zauve, ndi zotsutsakhristu! Inu mukuona, ndi Satana ali pa msonkhano wokopa anthu wotanza. Mukuona? Iye akuchita chirichonse chimene Khristu akhoza kuchichita, koma iye sangathe kuwatsimikizira Mawu. Mukuona? Iye angatenge gawo la Iwo apa ndi gawo la Iwo apa, koma iye sangathe kuwatenga Iwo onse palimodzi. Mukuona? Iye sangathe kuwatenga Iwo palimodzi. Kotero inu mukuona, palibe zodabwitsa kuti Baibulo

linanena kuti zikanadzapusitsa pafupi Osankhidwa omwe ngati zikanakhala zotheka—mzimu wotsutsakhristu.

¹⁰ Tsopano, ngakhale manenjala wawo yemwe wolengeza nkhani apa, utola nkhani, iye ndi wa iwo, akukhulupiririra mwa iwo, ndipo akuti iyeyo ali wogwidwa ndi chinthu chomwecho, chifukwa iwo amupindula iye.

¹¹ Zinthu zoipa zimenezo, izo...Tsopano, kodi inu simukuwona, akazi, chifukwa chimene ine ndikuyesera kumakuuzani inu za kuvala-zazifupi uku, kumeta, kudula tsitsi, ndi zinthu. Uwo ndi mzimu. Iwowo ndi mzimu! Ndi izi pano ziri mu magazini athu omwe otchuka ndi chirichonse cha zomwe zikuwonetsedwa uko—roko andi rolo ndi zinthu mu mpingo. Bwanji, ndi khwekhwe ndendende la Satana, ndipo iwo akadali mipingo ndi zipembedzo.

¹² Bwererani ku Mawu, ana, mofulumira momwe inu mukudziwira; ndipo inu musayerekeze kuti muwasiye Iwo! Inu mukhalabe muli ndi Mawu amenewo.

Onani, momwe mzimu wotsutsakhristu uwo, iwo ukhoza kuyankhula mu malirime, ukhoza kuwonetsa zizindikiro ndi zodabwitsa; iwo ukhoza kuchiza odwala; iwo ukhoza kuchita zinthu zonse izi. Mukuona? Anthu amenewo akuganiza kuti iwo akumufikira Mulungu, kuti anyamata amenewo ali otumizidwa ndi Mulungu, chifukwa mpingo walekerera pa Mawu.

¹³ Anyamata amenewo ndi a mu mpingo. Elvis Presley ndi wa Chipentekoste. Pat Boone ndi wa Mpingo wa Khristu. Tayang'anani pa anyamata amenewo, Achipentekoste, Mpingo wa Khristu, ndi onse amenewo monga choncho ali ndi mizimu yoipa imeneyo pa iwo. Red Foley, liwu lagolide, Mpingo wa Khristu, kumaimba nyimbo zachipembedzo momwe palibe wina amene angathe kuziimba izo ndi roko andi rolo mu liwu lotsatira. Ndi zipatso zawo inu mumawadziwa iwo. Taonani mipingo yomwe iwo ali a iyo. Elvis Presley ndi mamembala a Assemblies of God. Ndi zimenezotu, aliyense wa iwo ankafuna zimenezo, ndipo Satana anazipereka izo kwa iwo.

¹⁴ Kodi inu simukuwona, amzanga, momwe...Musati mulole akupulumukeni Mawu amenewo. Onani, ndi mzimu umene umafika pa iwe.

¹⁵ Ndipo ine ndimawauza akazi awa, pamene iwo amadzipanga iwo okha kumawoneka mwachigololo mu madiresi awa, kuti Mulungu adzakupangani inu kuti mudzayankhire chifukwa chochita chigololo. Ngati inu mukundikhulupirira ine kuti ndine chimene inu mumanena, wantchito wa Mulungu, mneneri, mverani kwa zimene ine ndikukuuzani inu. Mukuona? Inu mukhoza kusintha kuzimvetsa izi, ndipo ngati inu simungathe, ndiye inu muzingochita zimene ine ndikukuuzani inu kuti muzichita. Mulungu adzandigwira ine kuti ndiyankhire pa zimene ine ndikukuuzani inu. Mukuona? Inu zimvetserani

mwatcheru kwenikweni, ndipo zikumbukirani kuti zinthu zimenezo ndi mzimu.

¹⁶ Mwawamba, mwinamwake munthuyo Sali...Inu kumbukirani, *Mulungu ataphimbidwa ndi khungu*, ine ndinalalikira pa izo si kale litali (mwaona, mukuona?)—Mulungu ali ndi khungu pa iye? Tsopano, ingokumbukirani, ena a ife tinatumizidwa ku dziko lino kuti tizitulukira mu madera amenewa kuti azitiuza ife zinthu zimenezi. Mukuona? Ndi kudziwiratu; ndi Mulungu akuyankhula, akutisonyeza. Pamene inu muchiweruza chirichonse mwa mnofu, bwanji, iwo ndi osalakwa (taonani apa), anthu abwino, owona mtima, sangakuuzeni inu bodza kapena kanthu kosakhalapo. Ndipo chinthu chonsecho chiri mdierekezi. Achipembedzo, ngakhale kuyambitsa msonkhano wokopa anthu wamachiritso. Mukuona? Ndendende basi wotsutsakhristu. Mukuona? Ndipo apo pali Achipresbateria ndi onse awo. Inu mukuziona zipembedzo izo, momwe iwo akuchitira—kumene mu chinthu chomwecho?

¹⁷ Bwanji, kuno ku London, England, posachedwa pomwepa iwo anali ndi gulu la roko andi rolo kuti izimusanzira Khristu, ndi Yudasi, ndi zonse izo, ndi...Iwo amamutcha Khristu “Dadi-o” ndi kuyankhula kwa mawu onse awo amene ana openga aja amawayankhula. Mukuona? Ana ausinkhu wa mmateni alilanda dziko. Tsopano, inu mukudziwa kuti Baibulo limaneneratu zimenezo: Osathokoza, osayera, opanda chikondi chachibadwidwe, osayanjanitsika, onenera zobodza, osamvera kwa makolo (mukuona?), ausinkhu wa mmateni akulilanda dzikoli, ndipo izo zachita izo.

¹⁸ Ine ndinapita mu malo tsiku lina; iwo anali akusewera ichi—chimodzi cha zimajubokosi zakale izi, zonyansa, zinthu zonse izo. Ine sindinkafuna ngakhale kuti ndilitengeremo banja langa. Ine ndinati kwa dona ameneyo, “Kodi marekodi amenewo mumagula ndalama zingati?”

“Masenti khumi iliyonse.”

“Ndi zingati zomwe iyo ingasewere pa ora?” Iye anandiuza ine. Ine ndinati, “Nazi ndalama zake; chizimitseni icho!”

“Chabwino,” iye anati, “ine sindingati ndichite zimenezo. Ana amenewo amabwera kuno kuti azidzasewera zimenezo.”

¹⁹ Ndiye ine sindikanati ndiwononge ndalama kumeneko; ine ndinapita kwinakwakenso. Mukuona? Chabwino, chinthu chimenecho chingakupange iwe kukhala wamanjenje; iwe ungachite kusowa kuti upite kwina ndi kukatenga mulu wa zotontholetsa misempha kuti umwe utatha kumvera chinthu chopengetsacho. Izo zimamuyipira Mkristu. Ngati iwe umazikonda zinthu za mtundu umenewo, iwe ukudziwa chimene chiri cholakwika ndi iwe? Iwe ukusowa kuti ufike populumutsidwa, chifukwa chimene chiri mwa iwe chikudyerera pa chinachake pambali pa Mawu. Icho chikudyerera pa . . .

²⁰ Inu simukanati mulingalire Yesu akuchita chinthu ngati chimenecho mungatero inu? Kodi inu mungalingalire mmodzi wa aneneri akuchita chinthu choterocho? Kodi inu simukuwona, amzanga, chinthu chonsecho kulikonseko ndi mdierekezi. Ndipo Baibulo linanena momwe iye ati adzabwerere mu mawonekedwe a chipembedzo ndi kumangodzachita ndendende basi monga Khristu. Mukuona? Koma njira yokha imene inu muti mudzathere kudziwira izo, si ku jowina mpingo *uwo*, kapena kujowina mpingo *uwo*, ndi kukhala ndi Mawu; Iye ndi Mawu.

²¹ Tsopano, Ambuye akudalitseni inu aliyense. Ife tikupita molunjika kumene ku mafunso. Ndipo tsopano, kwa pafupi—mpaka pafupi ora ndi maminiti fifitini... Ine sinditha kudutsa mu mafunso onse awa. Pangokhala mulu wa iwo. Ine ndikuganiza iwo ndi mafunso abwino. Iwo ndi abwino kwambiri. Ine ndizingofikira pansipa ndi kutolapo limodzi apa ndi apo pamene ine ndizipitirira nazo. Ndipo tsopano... kuyankha iwo...

Ine ndimati... ine ndimaganiza usikuuno ine ndingobwera kuno, nkumusiya wina aziwerenga iwo, nkuti, “inde” kapena “ayi,” “inde” kapena “ayi,” mpaka... Kumeneko si kuwachitira anthu chilungamo. Iwo anafunsa mafunso amenewo kuti apeze yankho. Ndipo i—ine sindingati ndichite zimenezo, chifukwa ine nditenga amene ine ndingathe; ndipo amene ine sindingathe, ine ndidzawatenga iwo nthawi yotsatira pamenepa.

²² Ndipo tsopano, i—ine... Pafupi Lamlungu likudzali, ine sindikudziwa. Ine ndikukuuzani inu; ngati inu mungakomane naye Billy nthawiina pakati pa lero ndi Lachitatu... Ife mwina tingati tichokepo.

²³ Tsopano, kuno kuli chinthu chimodzi. Ine ndatsalira mmbuyo kwambiri mu zoyankhulana. Billy amandisonyeza ine mulu wa zoyankhula zapadera wautali *choncho*, amene akhala akudikirira, ena a iwo, kwa miyezi. Chabwino, pamene ine ndiri muno, ine ndiyenera kuti ndigwirepo ena a iwo, kugwirapo kukomana kwina, kuchita chirichonse chimene ine ndingathe kuti ndikhale ngati ndiziyanjanitsa. Ine ndipita ndikapemphere sabata ino pamene ine ndikhala nditapita ndi kuwapempha Ambuye, “Kodi Inu mukufuna kuti ine ndichite chiyani, kuwatsirizapo awa ka—kapena kutenga zoyankhulanazo?” Ngati ine nditenga zoyankhulanazo, ndiye ine ndidzangothamanga—ndidzabwera kunyumba Lamlungu ndi kudzathamangitsa kuyankhulana uku modutsa kumene kwinawake, ndi kupitirira nao kumene tsiku lonse ndi kuyankhulanako. Ndipo ngati ine sindidzatero, bwanji, ine ndidzasowa kuti ndidzaimitse kuyankhulanako mpaka ine ndidzabwererense kachiwiri. Ngati ine sinditero, ndiye ine ndidzayankha... ine ndidza... Billy adzakutumizirani inu khadi.

²⁴ Ndipo ine ndikukuuzani inu; ndi zabwino, ana abwino awa, kuti ndikuuzeni inu momwe iwo amakonderana wina ndi mzake, chikondi chimene iwo ali nacho kwa wina ndi mzake. Wina akhoza kumuuza wina ndipo winayo amamuuza... Billy amangoimbira mmodzi mu chigawo, pafupi mailosi handiredi ndi fifite, ndipo ena onsewo amawauza ena onse. Iwo amakondana wina ndi mzake. Iwo samafuna kuti aphonye chirichonse. Iwo ali—amafuna kuti azikhala ali kuno pa miniti iliyonse kuti aziwona zimene zikuchitika; pakuti ngati Ambuye angapereke chinachake, iwo akufuna kuti azikhala ali kuno kuti achilandire icho. Ndipo ine ndikuwayamikira iwo.

²⁵ Tsopano kumbukirani, amzanga okonededwa, mmawa uno ine ndinapanga neno pa ena a mafunso. Ndipo ine ndikuzindikira ena a awa (eya!) komabe—amene ndiri nawo mmawa uno, ali ochuluka okhudza anthu kusamukira ku Arizona. Mukuona? Ine ndimaganiza ine—kulibwino ndizifotokoze zimenezo momveka, kuti inu mumvetse.

²⁶ Tsopano, mu—musati muziganiza kuti ine ndikuyesera kumawauza anthu kumene iwo angati azikakhala, ndi zimene iwo angati azichita, ndi...Tsopano, ine sindiri kunena zimenezo, m'bale wanga wokonededwa. Pali anthu owona mtima amene akufuna kuti asamukire ku...Chabwino, aliynese amene akufuna kuti asamuke, ine zedi—ndingakhale ndiri wokondwa, utali wonse umene ine ndiri kumeneko chimene—kuchuluka kwa momwe ine ndiri kumeneko...Ine ndiri kuno pafupi kakhumi kuposa momwe ine ndiri kumeneko. Ine ndiri nazo...Pakati pa pano ndi Khristmasi, ine ndiri ndi pafupi masiku anai oti ndikhale ndiri kumeneko. Ndiye mwamsanga zikakatha zimenezo, ine ndichoka kupita kutsidya kwa nyanja. Ine ndidzakhala ndiri kuno ku kachisi mwinamwake masabata awiri kapena atatu ine ndisanapite kutsidya kwa nyanja mu—chitsitsimutso, monga kawirikawiri ine ndimachitira mu kuphukira masamba uku. Ndiyeno kuchokera kumeneko, ine ndangokhala ndi msonkhano umodzi wokha ku Arizona yense, ndipo umenewo ukufika podzachitika mu Januwale ku Phoenix, mausiku awiri ndi Amuna Amalonda Achikhristu. Mukuona? Ine sindiri...Ngati anthu kumeneko...Kodi inu mungaimitse tepi imeneyo? [M'bale Branham apempha kuti tepi rekoda iyimitsidwe ndipo ayankhula kwa osonkhana—Mkonzi.]

²⁷ Tsopano, pamene ife tikuyamba pa mafunso awa usikuuno, ine ndatola limodzi apa ndipo...Kodi inu mukukomedwa nawo iwo? Nenani, "Ameni!" [Osonkhana ayankha, "Ameni!"—Mkonzi.] Ine ndikuganiza ndi zopindulitsa kwa ife pa nthawi ino. Ndipo o, ine ndikukhulupirira posachedwapa ku...Poyang'ana mmawa uno ndisanabwere kuno pa n—nkhani zina ndi malo ena mu Baibulo, ine ndimaganiza, "O, chinthu chodabwitsa chake chomwe icho chiti chikhale chiri...Pamene ife tikuyembekezera kudza

kwa Ambuye, chinthu chodabwitsa chake chikanati chikhale kuti titenge mobwera mmbuyo kudutsa pa ochitapo onse a Chipangano Chakale aja, kudutsa mu Yobu ndi kudutsa mmenemo, ndi kuyendetsa mndandanda wa misonkhano pa iwo (kodi izo sizikanati zidzakhale zodabwitsa?), kungokusonyezani inu momwe zikufanizitsira kumene mu tsikuli (Mawu onsewo kumangirizana palimodzi), ndi zonse zokhudza ziwonongeko za—ndi nthawi zamakedzana ndi momwe zikufanizira ndi lero; momwe chirichonse mu Chipangano Chakale chikuyankhula za kudza kwa Ambuye Yesu.”

279. Tsopano, funso loyamba ine ndinalisolola kuchokera apa: **M'bale Branham, kodi ndi zolakwika kuti Mkristu aziyika—aziyika tsitsi lake mu mapini okulunga? Ndiponso, izitalika bwanji mikono ya zovala zake? Zikomo inu. Mlongo.**

²⁸ Tsopano, izo—zikutanthauza mochuluka kwambiri kwa mkazi ameneyo. Tsopano, kwa ena a ife abale ife tikhoza kuganiza, “O, mkazi wopusayo.” K—koma izo si zopusa kwa iye; iye akufuna kuti adziwe.

Tsopano, za kuika tsitsi mu kodi zinali chiani izo, michira ya nkhumba kapena chinachake chimzake? Ine ndikupepesa. I—ine sindimati. . . Izo. . . Ine ndikupepesa. Mapini okulunga. Ndikhululukireni ine. Mapini—michira ya nkhumba! Ndi zimene asungwana anakonda kuvala zaka zapitazo. Inu mukukumbukira, zokhala ngati. . . Kodi uko sikunali kulondola? Iwo ankazitcha izo michira ya nkhumba, basi kungokhala ngati lopiringizika likulendewera pansu? Ayi, pini yokulunga, ndikhululukireni ine, amzanga.

²⁹ “Utali wake wa manja azovala zoti azivala?” I—ine sindikuganiza kuti izo ndi chirichonse pa izo. Ine sindikudziwa. Mukuona? Zimene ine sindingathe kuziikira kumbuyo ndi Baibulo, i—ine sindikufuna kuti ndizinena zochuluka pa izo.

³⁰ Tsopano, ine ndikungokuuzani inu izi kwa ine, chifukwa ine ndiribe Lemba loti ndiziyikire kumbuyo izi. Chinthu chokha chimene ine ndiri nacho kwa madona cha tsitsi lawo ndi kuti asalidule ilo. Momwe iwo akufuna kuti azivalira ilo, zimenezo ziri kwa iwo. Ndipo za mapini okulunga, kwenikweni, ine sindikudziwa chomwe iwo ali, kupatula ngati ziri zinthu izi zimene zimawoneka ngati zopanira zovala zimene iwo amaika mu tsitsi lawo, ndi za—chinthu chokha chimene ine ndikuchidziwa. . .

³¹ Ndipo utali wa manja a zovala, ine ndikuganiza, pokhala Mkristu, Mulungu azikuuzani inu zoti muzichita pa zinthu zimenezo. Inu mukuona? Ine ndikukhulupirira monga munthu wa Chikristu inu mungati—inu mungati muzidziwa momwe mungamachitire izo. Ine sindikuganiza kuti Mulungu amadula utali uliwonse kapena chirichonse chimene icho chiri. Bola ngati

inu mukuwoneka bwino ndipo mukuwoneka molemekezeka ndi mwawukhondo, i—ine ndikuganiza zimenezo ziri bwino bwino. Sichoncho inu? Mukuona? Tsopano, kumeneko ndi kulingalira kwanga basi. Tsopano, uyu ndi ine, mwaona, chifukwa ine sindingaikire kumbuyo chinthu chinachake ndi Lemba.

³² Ine ndikukhulupirira mmawawu funso linabwera apo la kulocha tsitsi, inu mukudziwa, ndi—mangamanga. Tsopano, i—i—izo—i—ine sindingathe kunenapo kanthu pa izo. Ine sindikudziwa, koma i—i—i—ine ndiribe Lemba kuti ndinene kuti ayi ku—kulocha tsitsi lanu. Tsopano, izo ziri—izo ziri . . .

Inu akazi, inu mumafuna kuti muziwoneka bwino, ndipo inu muyenera kumawoneka bwino. Ndipo M'bale Branham sakutsutsana ndi ana inu. Inu ndi ana anga; i—i—ine ndimakukondani inu, ndipo i—ine sindikufuna kuti ndizipitirira kukulalatrani inu. I—ine sindingati ndizichita zimenezo popanda chifukwa; ine ndikungoyesera kuti ndikuthandizeni inu.

³³ Koma tsopano, taonani, ingondilolani ine basi ndikufunsemi . . . Ndiroleni ine ndinene izi monga yankho kwa funso limenelo. Tsopano, kodi inu mwakonzeka? Ndipo kwa inu amene muli pa tepi, ndi izi apa, alongo: Ngati pali funso mu zimenezo, inu musamazichite izo. Koma ngati inu—ngati inu muli odzazidwa ndi Mzimu wa Mulungu ndipo mukutsogozedwa kuti muchite zimenezo, bola ngati izo sizikusokonezana ndi Lemba ndipo sizikusokonezana ndi funso, inu muli okhutsidwa mwangwiro kuti icho ndi chifuniro cha Ambuye, ndiye pitirirani nazo ndi kumachita izo (mukuona?), chifukwa palibe Lemba loti linene ayi (mukuona?) pa izo. Ine sindiri . . . Sali kunena kanthu kongga izo mu Baibulo.

³⁴ Ine ndikudziwa Yesaya 5, ine ndikukhulupirira ndi pamenepo, amakamba za akazi, momwe iwo azidzavalira zovala zosintha ndi chirichonse monga izo; koma uko kunali kunyada ndi zinthu, kukuidwapo. Ngati inu muzichita izo chifukwa cha kunyada, ndiye ndi zolakwika. Mukuona? Fufuzani mtima wanu pamaso pa Mulungu. Ngati palibe Lemba la izo, ndi momwe Mzimu ukukutsogolerani inu, inu pitirirani nazo kumachita zimenezo. Koma tsopano, pamene izo zifika pakuti ngati inu mukuyenera kukhala ndi tsitsi lalitali kapena lalifupi, inu muzikhala ndi tsitsi lalitali; limenelo ndi Baibulo.

³⁵ Pali funso apa; i—ine ndikhoza kuliyanika ilo pakali pano. Ilo liri apa; ine ndinaliwona ili mmawa uja kapena nthawiina. Anati, “Inu nthawizonse mumakamba za akazi, momwe iwo sayenera kuti azivalira tsitsi lawo, koma inu simumanena kanthu za amuna.”

³⁶ Ngati ine nditamuwona mwamuna akubwera muno ndi tsitsi lalitali likulendewera kumbuyo kwake ngati mkazi, ine ndinganene, “Bambo, bwanji inu osapita ku nyumba yometera?”

Inu mukuwoneka ngati mkazi.” Mukuona? Koma amuna kawirikawiri samachita zimenezo. Mukuona? Osati momwe mwamuna. . . Tsopano, si mwa kusalephera kwa mwamuna, iwo ali ochimwa basi monga mkazi.

Ndipo tiri chiyankhulire, mwamuna amene angamamulole mkazi wake kuti azichita zimenezo, iye akhala ali wochimwa pawiri pa zimenezo, chifukwa iye akuyenera kukhala amene ali ndi chonena mu nyumbayo. Ndipo mwamuna amene akulephera ngakhale kuti azilamulira nyumba yake yomwe; iye angathe bwanji kuchita izo mu nyumba ya Mulungu? Mukuona?

³⁷ Ine ndiri wothokoza kwambiri chifukwa cha gulu lathu la akazi amene ife tiri nawo amabwera kunowa. Ine ndikunena izi ndi kulemekeza ndi chikondi, ndipo tsopano, Mulungu akudziwa kuti izi ndi zooni. I—ine ndinali naye mzanga wolalikira Kummwera uko amene anali ndi chimodzi cha mipingo yowoneka mwaukhondo yomwe ine ndinayamba ndaiwonapo. Pamene zifika pa akazi, akazi okongola kwambiri amene ine ndinayamba ndawawonapo amakhala pamenepo mwachiyero, mwaumulungu, ali ndi tsitsi lalitali. Ndipo ine nthawizonse ndinkayamikira kupita ku mpingo umenewo. Ndipo Ambuye Yesu wandipatsa ine mpingo lero umene ukuwala kuuposa umenewo mailosi zana limodzi—azimayi anga.

³⁸ Ine sindimakuzazirani inu kuti ndikhale wankhanza; ine ndingokhala wokondwa kwambiri chifukwa cha inu. Ine sindikufuna basi kuti Satana apondetse phazi paliponse. Mukuona? Ine ndikufuna inu kuti muzisunthira mmwamba, osati chammbuyo. Musati muzilola konse munthu wina kuti akunyangani inu ndi matsenga ena, kapena chinachake chimzake monga icho, kapena chinachake kumati, “O chabwino, izo sizi. . .” Mukuona? Umo ndi momwe Satana anatanthauzira Mawu kwa Eva. Mukuona? Inu muzikhulupirira basi zimene Mawu akunena. Chabwino.

280. Zachangu kwambiri. M’bale Branham, podziwa kuti nthawi ikutha ndipo umuyaya ukulowamo, kodi langizo lanu lingakhale lotani kwa anthu amene akukonzekera chikwati?

³⁹ Pitirirani nazo kumene ndi kukwatirana. Mukuona? Zipitirirani nazo ngati kuti inu mukhala moyo kwa zaka zana zina kuno pa dziko lapansi. Zingopitirirani nazo kumene; sungani mtima wanu utakhazikika pa Khristu, osati mitima yanu pa zinthu izi za mdziko, koma pa Khristu. Mukuona? Zipitirirani nazo kumene; zikwatiranani, ananu. Mulungu akudalitseni inu mu chikwati chanu.

281. Wokonedwa M’bale Branham, ine ndinabatizidwa mu Dzina la Yesu. Mawu amanena kuti inu mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera. Kodi izi—kodi izi zikutanthauza ubatizo, Mzimu Woyera,

kapena kodi izi zikutanthauza kuti ine ndilandire mphatso—yotsimikizika—ine ndilandire chondichitikira chotsimikizika limodzi ndi ubatizowo? Ine ndikufunitsitsa kuti ndikhale—kuti ndikhale wodzazidwa ndi—Mzimu. Chonde ndikhululukireni chifukwa cha cholembedwa chachitalichi pakuti ine ndakhala ndikufuna kuti ndikufunsi inu funso ili kwa nthawi yaitali. Zikomo inu. Ndipo munthuyo walembo dzina lake. Awo ndi anthu akunja kwa mzindawu.

⁴⁰ Tsopano, apo pali funso labwino. Tsopano, ubatizo ndi Mzimu Woyera ndi chokuchitikirani chenicheni chimene munthu amayenera kuchilandira. Tsopano ndiroleni ine ndikhale ngati ndachikonza apo icho kwa miniti chabe. Mukuona? Tsopano, anthu ambiri ali nalo—lingaliro... Ine ndikuhulupirira izo zapotozedwa. Ndipo mwinamwake apa pomwe kwa mpingo ndi kwa mpingo umene ukumvetsera, uko kukhoza kukhala kuli funso. Tsopano, pamene ine ndikunena za kusakhulupirira umboni woyambirira wa Mzimu Woyera kuti ndi kuyankhula ndi malirime (i—ine sindimavomereza zimenezo) ine ndikuhulupirira ndi kuthandizira kwa Mulungu ine ndikhoza kutsimikizira izo mu Baibulo kuti uko ndi kulakwitsa (mwaona?), chifukwa kuyankhula mu malirime ndi mphatso ya Mzimu Woyera. Ndi angati akudziwa zimenezo? Machiritso Auzimu ndi mphatso ya Mzimu Woyera, ndipo apa Mabitoloji akuchita zimenezo. Mukuona?

⁴¹ Satana akhoza kusanzira iliyonse ya mphatso zimenezo. Afiti aakazi, afiti aamuna akhoza kuyankhula mu malirime ndi kuwatanthauzira iwo. Ku maiko akunkhalango, nthawi zambiri mfiti imayankhula mu malirime, kumwa magari kuchokera mu chigaza cha munthu, ndi kumatanthauzira malirime osadziwika.

⁴² Uko mu Arizona pamene iwo akhala ndi chisangalalo chachikale cha kuvina kwa chimanga, Amwenye amakulunga ndi njoka za mbobo izi pa iwo pamene iwo akuyesera kuti apemphere kwa Mulungu kuti awatumizire iwo mvula pofuna chimanga chawo. Iwo amakutcha uko kuvina kwa chimanga. Iwo amatenga ngayaye za chimanga, nkuziika izo mozunguliza pa iwo, ndi kupanga kamtambo kakang'ono, ndipo iwo amavina. Ndipo sing'anga amatulukira apo ali ndi nyanga pa mutu wake, nyanga za njati. Ndipo iwo amavina ali ndi njoka za mbobo izi modzikulunguza nazo, ndipo afiti ndi ambiri a osuta akaliwo ndi zinthu atazungulira pa malopo... Iwo samamulola mzungu pozungulirapo pa nthawi imeneyo, koma ine ndinkawayang'ana iwo kudzera mu zoyang'anira, ndipo ndiri nawo amzanga Achimwenye amene anapita ku zovina zawozo; amenewo ndi amene sali Akhristu, ndithudi. Ndipo iwo amavina kuvina kwa chimanga uku atazigwira njoka izi. Ndipo mfiti imabwera apo, ndi kudzicheka yokha ndi mipeni, ndi china chirichonse, ndipo

potsiriza iwo amalowa mu mzimu, ndi kuyankhula mu malirime ndi kuwatanthauzira iwo.

⁴³ Ine ndiri—ndikhoza kukutengerani inu kumene mkati mwa maora atatu kapena anai kuchokera pano, kumene wamaula akhoza kuika pensulo pa tebulo, ndi kulowa mu chizimbwizimbwi ndi mitundu yonse ya zinthu, ndi kumagwedeza manja awo; ndipo pensulo imeneyo nkuwuka apo ndi kumalemba mu malirime osadziwika, ndipo mfitiyo imaimirira ndi kukuuzani inu chimene iwo akunena.

⁴⁴ Tsopano, umenewo si umboni wa Mzimu Woyera. Mukuona? Inu simungati muzidalira pa zimenezo. Inu simungati muzidalira pa chipatso cha Mzimu, chifukwa chipatso choyamba cha Mzimu ndi chikondi. Ndipo a Chikristu cha Sayansi amachita chikondi chochuluka kuposa aliyense amene ine ndikumudziwa, ndipo iwo ngakhale amamukana Yesu Khristu kuti ndi Waumulungu. Mukuona? Pali umboni umodzi wokha wa Mzimu Woyera umene ine ndikuwudziwa, ndipo umenewo ndiwo chikhulupiro chencheni mu Mawu olonjezedwa a oralo!

⁴⁵ Tsopano, Ayuda aja ankabwera; iwo anali nacho chipembedzo chochuluka kuposa chimene ophunzira anali nacho. Iwo anali ophunzitsidwa bwinoko mu Malemba kuposa momwe ophunzira analiri, chifukwa iwo anali asodzi, okhometsa misonkho, ndi zina zotero. Ndipo iwo anali nacho chikhulupiro chencheni ndi chikhulupiro choona mu zimene iwo anali kuzichita. Tsopano, mvetserani mwatcheru tsopano; musati muphonye izi! Mukuona? Pamene zinafika pokhala zipatso za Mzimu, wachifundo ndi wofatsa, ine ndikulingalira apo panalibe mmodzi wa ansembe amenewo koma amene sakanamuposa Yesu Khristu mu zimenezo. Iye anapita ku kachisi, anapota zingwe, anayang'ana pa iwo ndi mkwiyo, ndipo anagudubuza magome awo, ndi kuwathamangitsa iwo pamalopo. Ndi kulondola uko? Baibulo limati Iye anayang'ana pa iwo ndi mkwiyo. Baibulo limanena zimenezo. Ndizo ndendende kulondola.

⁴⁶ Koteru mukuona, ansembe amenewo anali odekha, ofatsa, anthu omvetsa. Pamene izo zifika pa zipatso za Mzimu, iwo akanakhoza kuwonetsera zipatso zochuluka za Mzimu kuposa zimene Yesu akanachita konse. Pamene izo zifikaku za fioloje, iwo sankadziwa—sukulu imene Iye anachokerako. “Kodi munthu uyu anachokera kuti? Kodi iye anachokera kuti? Kodi iye ali ndi khadi la chiyanjano chiti? Kodi iye ndi wa bungwe liti? Iye sitikudziwa kumene iye akuchokera. Iye anali basi mwamtheradi munthu wakunja amene anabadwa mwathengo. Bwanji, ife tikhoza kumumiza iye apa mu maminiti pang'ono ndi kukuwonetsani inu mwa malamulo...” Iwo anali nawo ufulu woti achite zimene iwo anachita pamene izo zifika ku zimenezo. Bwanji? Chifukwa iwo ankalephera kuti awone kuti Iye anali Mawu olonjezedwa a ora aja. Njira yokha imene

iwo anazindikirira izo, pamene Yesu anachita Mawu pokhoza kuwauza iwo zimene iwo anali nazo mu mitima yawo, zimene iwo anakhala akuchita...Iye anali Mneneri molingana ndi Mawu a Mulungu. Zimene Iye ankanena zinkafika podzachitika, mawu aliwonse, liwu ndi liwu.

⁴⁷ Iye anali Mneneri wa Mulungu, Wantchito, Mulungu Mneneri. Osati...Izo zinali—a—anali pamenepo, mneneri wa Mulungu, ndipo uyu ndi Mulungu Mneneri, osati mneneri wa Mulungu. Ameneyo anali Malaki, Yeremiya, ndi Yesaya, ndi Eliya, ndi ena otero, koma uyu anali Mulungu Mneneri, osati mneneri wa Mulungu. Inu mukumvetsa zimenezo tsopano?

Aneneri onse amene ankawonetsera moyo Wake mu zigawo, ankasewera gawo lawo, koma mwa Iye munali Chidzalo cha aneneri onse. Aneneri, Mawu a Ambuye ankabwera kwa iwo, aneneri, koma Awa anali Mawu ndi Mneneri, Munthu yemweyo. Mukuona?

⁴⁸ Tsopano, tsopano, pamene munthu alandira Khristu mwa khalidwe limene Iye alirimo, inu simungati mulandire izo pokhala...Mukuona? Tsopano, ena a iwo amati, “Chabwino, ine ndine Wachilutera.” Chabwino, ndiribe kanthu kotsutsa zimenezo, koma Mphungu sizimadya pa zimenezo. Mukuona? Izo zinali monga momwe izo zinaliri; icho chinali chakudya chatsopano cha tsiku limenelo.

“Ndine wa Chiwesile.” Izo zonse ndi zabwino, koma inu mukukhala mu zakale. Mukuona?

Tsopano, anthu amenewo ankati, “Pakuti, ife tiri naye Abrahamu kukhala atate athu.”

Mneneri ameneyo anati, “Mulungu ndi wokhoza mwa miyala iyi kudzutsira ana kwa Abrahamu.” Mukuona?

“Ife ndi a *ichi*. Ife ndi a *icho*.”

Izo zinalibe kanthu...Iye anati, “Inu kam’badwo ka njoka, ndani wakuchenjezani inu kuti muthawe mkwiyo? Musati muyambe kumanena, ‘Ife tiri naye Abrahamu atate wathu,’ chifukwa Mulungu ndi wokhoza mwa miyala iyi kudzutsira ana kwa Abrahamu.” Mukuona?

⁴⁹ Kotero kukhala wafioloje wophunzitsidwa bwino zinalibe kanthu kochita ndi izo. Kukhala wofatsa ndi wodekha zinalibe kanthu kochita ndi izo. Nchiani chinkamupangitsa Iye kukhala wosiyana? Iye anali Mawu atapangidwa thupi, osati Mawu a tsiku la Mose, Mose anali tsiku limenelo—Mawu; osati Mawu a masiku a Nowa, Nowa anali Mawu a tsiku limenelo; osati tsiku—Mawu a tsiku la Eliya, Eliya anali Mawu amenewo a tsiku limenelo; koma Iye anali Mawu a pakali pano, ndipo iwo ankakhala moyo mu za mmbuyo.

⁵⁰ Chinthu chomwecho chikubwereza! Umenewo ndiwo umboni wa Mzimu Woyera, pamene Mulungu awululira kwa

inu ndipo inu nkuziwona izo, PAKUTI ATERO AMBUYE ndi kuzivomereza izo. Osati zimene inu muli, zimene inu munali, kapena kalikonse ka izo, ndi zimene Mulungu wakuchitirani inu tsopano. Umenewo ndiwo umboni.

⁵¹ Yesu anati . . . Iye anatipatsa ife umboni wa Mzimu Woyera, Yohane 14. Iye anati, “Ine ndiri nazo zinthu zambiri zoti ndikuuzeni inu. Ine ndiribe nthawi yoti ndichitire izo, koma pamene Mzimu Woyera adza, Iye adzakuuuzani inu, adzabweretsa ku kukumbukira kwanu zinthu zimene ine ndinkakuuzani inu, ndipo adzakusonyezani inu aponso zinthu zimene ziri nkudza.” Kodi inu simukuwona? Umenewo ndiwo umboni. Kumeneko ndi kuneneratu ndi k—kukhala ndi kutanthauzira Kwaumulungu kwa Mawu olembedwa. Tsopano, kodi umenewo sindiwo umboni wa mneneri?

⁵² Mpenyi mu Baibulo anali mwamuna amene ankakhoza kuneneratu ndipo izo nkukhala mwangwirowi, ndendende, osati winawake kuika manja pa iye, imeneyo ndiyo mphatso. Mneneri ali wokonzedweratu ndipo amabadwa kuti adzakhale ali mneneri. Mukuona? Moyo wonse wamphumphu amakhala uli mneneri, umenewo ndi udindo. Apo ndi pamene anthu . . .

⁵³ Ambiri a mafunso apa pa: “Chabwino, kodi Mkwatibwi . . .?” “Kodi *ichi* . . .?” “Mpingo n . . .” Mukuona? I—inu simungathe kugawaniza chomwe iwo ali. Mkwatibwi ndiye Wosankhidwa wa Mulungu. Mpingo udzadutsa . . . Awo ndi amene Ilo limawanena, “Aliyense amene afuna, msiyeni iye abwere.” Koma Mkwatibwi ndiye Wosankhidwa wa Mulungu.

⁵⁴ Pali maudindo asanu osankhidwa a Mulungu. “Pakuti Mulungu waika mu Mpingo atumwi, aneneri, aphunzitsi, abusa, alaliki.” Mulungu anachita zimenezo. Anthu amakhala ndi madikoni ndi zina zotero, ndi chinthu china chirichonse, koma inu mukuona, koma Mulungu anaika mu Mpingo kwa ungwiro wa Mpingo—simungathe kugawanitsa zimenezo.

⁵⁵ Tsopano, Mzimu Woyera, pamene Iwo ubwera, Iwo umakhala umboni kwa inu (mukuona?) kuti Mawu awa ali olondola, Mawu a lero, osati Mawu a Lutera, Mawu, osati a Mose. Iye timachitira umboni kuti Iwo ndi Choonadi, koma ilo ndi tsiku lina.

⁵⁶ Tsopano, nanga bwanji ngati Yesu akanabwera nkuti, “Tsopano, monga Mose anabwera kudzakutulutsani inu nonse ku Igupto, ine ndabwera kuti ndidzakutengereni inu kwinakwakenso”? Nanga bwanji ngati Iye akanati, “Tiyeni tipite tikagwire ntchito ndi kumanga chombo. I—ndine Ambuye Mulungu, i—ine ndiliyandamitsa dzikoli tsopano. Ine ndikuti ndilimize dzikoli, onse a iwo”? Bwanji, Iye akanakhala kuti ali kunja kwa . . . Mwaona, Lemba silinanene konse kuti Iye akanati abwere monga choncho. Mukuona? Iye sakanati akhale ali Mesiya. Ziribe kanthu momwe Iye akanamangira chombo

chachikulu, kapena chirichonse chimene Iye akanati achite. Iye apabe sali—Iye akanakhala kuti sakukwanira kuti akhale Mesiya. Aleluya! Ndi zimenezotu! Ndi kuyenerako! Inde, bwana!

⁵⁷ 1 Akorinto 13 amanena izi: “Pamene icho chimene chiri changwirowo chibwera, icho chimene chiri cha mderamdera chidzachotsedwapo.” Koteru zinthu zazing’ono zonse izi za kulumpha mmwamba-ndi-pansi ngati mwana, akuyesera kuti ayankhule mu malirime, ndi zinthu zina zonse izi, pamene icho chimene chiri changwirowo... Ndipo ife tiri nako lero, mwa kuthandizidwa ndi Mulungu, kutanthauzira kwangwirowo kwa Mawu ndi kutsimikizidwa Kwaumulungu! Ndiye icho chimene chiri chamderamdera chathetsedwapo. “Pamene ine ndinali mwana, ine ndinkayankhula ngati mwana, ine ndinkamvetisa ngati mwana; koma pamene ine ndinakhala wamkulu, ine ndinasiya zinthu zachibwana.” Ameni! Ine ndiyamba kulalikirira ndiyeno sindifika ku zinthu izi.

282. M’bale Branham... (Kodi ine ndinatsiriza izo? Kodi ine ndinafika ku za ubatizo wa Woyera... Inde, zimenezu zinali za izo, sichoncho izo? Chabwino. Mundikhululukire ine, ngati ine sindizitenga izo, mungondikhululukira ine. I... Awa ndi mafunso odabwitsa kwambiri. Iwe ukhoza kungokhala usiku umodzi wonse pa funso limodzi lokha, m’bale, ndiyeno nkusalikhudza nkomwe ilo.) **Ine ndikukuyamikirani inu monga wantchito wa Mulungu, kukhulupirira—ndipo ine ndikukhulupirira Uthenga wa Choonadi. Mkazi wanga sakundimvera ine—akunena chirichonse—akunena chirichonse pa Uthenga uwu, ndipo sakufuna kumamvetsera kwa tepi iliyonse. Ine ndiri mu vuto la manjenje pa ntchito yanga naponso. Ine ndikufuna mkazi wanga kuti akhulupirire nayenso ndipo muwapempherere ana anga. M’bale Branham, ine ndikufuna kuti ndikhale bwenzi la Mulungu—ine ndikufuna ndipezeke ndiri mu chifuniro cha Mulungu kwa moyo wanga. Ine ndikufuna kuti ndikhale wantchito Wake. (Ndipo munthuyo walembapo “tembenuzani.” Dikirani miniti.) Pamene ine ndinali wamng’ono, ine ndinkamuuzala aliynse kuti ine ndikufuna kuti ndidzakhale mlaliki. Ine sindikudziwa zimene Mulungu akufuna kuti ine ndichite. Ndine wololera kuti ndizichitira chirichonse kwa Ambuye. Wanu mwa Ambuye.**

⁵⁸ Tsopano, funso labwino. Ndipo bamboyu ndi woonamtima. Mkazi wake, bwanawe wake yemwe ali gawo la iyeyo... Mundirole ine ndiwonjezere chinachake apa kwa izo? Abale anga, ine ndikunena izi mu Dzina la Ambuye. Limodzi la masiku awa, Ambuye akalola, ine ndikuganiza ine ndidzangopitirira ndi nudzapanga tepi ija ya *Chikwati ndi Chilekano* (mukuona?), kuibweretsa iyo komwe kuno ku kachisi.

Ngati iyo idzalekanitse iyo idzangoyenera kuti ilekanitse. Koma ife tikuti tidzatsimikizire kuti ndi Mawu a Ambuye.

⁵⁹ Yang'anani, abale anga. Mvetserani kwa izi. Kodi inu mukudziwa kuti nthawi zambiri inu mumatenga wokwatirana naye wolakwika kuno pa dziko lapansi? Maso ena okongola a bulauni, kapena a buluu, kapena otuwa amakudololerani inu ku malo amene inu—amene inu simukanayenera kumvetserako. Amuna ambiri amazindikira zimenezo.

⁶⁰ Mwamuna amene akukwatira poyamba azifikira kwa izo mwapemphero. Inu musati muziwatenga akazi chifukwa chokhala okongola kunjaku, koma okongola mkati, wina amene angadzakhale mayi kwa ana anu.

⁶¹ Ine ndikudziwa kuti izi zimveka moyipa kwa mtumiki kuti anene izi pa guwa. Koma ine ndinkayenda n—ndi ogula ng'ombe pamene ndinali Kumadzulo. Ife tinkagula ng'ombe zodzazibalitsa, ndipo iwo ankafuna kuti akhale ndi gulu. Ndipo ine ndinakaphunzira zochuluka kwambiri kumeneko zimene—pamene ine ndinkawawona ogulitsa awo ndi zinthu zimene anali kuchita, ogula amenewo. Ine ndinkakonda kupita ndi mzanga wakale, amabwera kuno ku tchalitchi ndi ine, ndipo ine ndinamutsogolera kwa Khristu, anali wachikunja wangwiro pakuyamba pomwe, Bambo Jeffries. Ambiri a inu mukumukumbukira iye, waziweto uko ku Colorado. Ife tinkapita, ndipo iwo ankabwera pa—ng'ombe.

Ine ndinawona ng'ombe yaing'ono ya nsoti tsiku lina ikugulitsidwa \$11,000, ka ng'ombe kakang'ono basi; iko kanali kasanaswe nkomwe. Ndipo ine ndinati—ndipo Jeff anati, “Ngati ine ndikanakhala nazo ndalama, ine ndikanaziika izo pa nsoti umenewo.”

Ndipo ine ndinaganiza, “Tsopano, iyeyu ndi waziweto; iye amaimvetsa ntchito yake.” Ine ndinati, “Jeff, chifukwa chiani kuti iwe . . . Choyenera chake ndi chiani? Iyo ndi ya Hereford. Iyo imene yagulitsidwa kanthawi kapitako pa \$300, kwa ine, imawoneka kuti ndi ng'ombe yokulirapo ndi chirichonse.”

⁶² Iye anati, “Penya, Billy, pali chinthu chimodzi chimene iwe sulikuchimvetsa pogula ng'ombe.” Anati, “Ine ndikuganiza iwe ukuyenera kumangopitiriza kulalikira kwako kwa pa msewu.” Koma anati, “Iwe suli kuzimvetsa ng'ombe.” Iye anati, “Tsopano, tayang'ana pa nsoti uwo uli apowo.” Ife tinayenda kupita pamenepo. Anati, “Iwe ukuwona kuyang'ana kolusa uko mmaso ake?”

Ine ndinati, “Eya.”

Anati, “Ana ake, ndi zidzukululu zake, ndi zidzukululu, zaidzukululu, zidzukululu zake zidzakhala nawobe mayang'anidwe olusa amenewo.” Ndipo anati, “Iwo azidzadzithamangitsa okha mosauka. Izo sizidzatha konse kukhala mayi kwa ana awo.” Ndipo anati, “Iwe sungathe konse kuzinenepetsa izo;

izo sizingakhale konse zanyama.” Iye anati, “Tayang’ana pa ng’ombe yaing’ono iyi apa imene ikugulitsidwa. Tayang’ana momwe iyo ikuwonekera yodekha. Tayang’anani pa mawonekedwe amtendere awo pa nkhope yake, mawonekedwe a mtundu umenewo, opanda kulusa mmaso ake.” Anati, “Iye adzakhala mayi weniweni kwa ana ake; ndi ana a ana ake, ndi ana a ana ake adzapitiriza kumakhala mwanjira imeneyo.” Ndipo anati, “Iwo onse adzakhala amayi, ngati iwo angadzathe kupeza thonde wa mtundu woyenera kwa nsoti umenewo (mwaona?), izo zidzawapanga ana awo. Koma kuyang’ana kolusa uko pa nkhope nthawizonse kudzapanga gulu losauka la ng’ombe, ngati munthu akuyesera kuti agule ng’ombe.”

Ine ndinati, “Inde, bwana! Zikomo inu.”

⁶³ Ndipo chinthu chomwecho chingagwiritsidwe ntchito pa akazi. Inu mukamutenga mmodzi wa odzilocha-pankhope awa ndi a maso-olusa, owoneka ngati mtundu wina wa chinyama, kuyesera kuti adzichotsere okha maonekedwe a umunthu, iye sadzapanga konse chirichonse. Iye azidzathamanga nthawi zonse. Ndipo Chikhristu si kukongola kunjaku, ndi kwa mkatimo: kwa mtendere, bata, kudzikometsera okha mwamtendere, mzimu wa bata, chimene chiri mtengo waukulu pamaso pa Ambuye. Ndi chimene ife tikuti tizichifunafuna pa akazi, ndi pa amuna, ndi aliyense amene ali. Tsopano . . .

283. M’bale Branham: Mafunso: Kodi mkazi Wachikhristu azivala miyala yonyezimira yophweka, monga ugufu kapena ngale?

⁶⁴ Chabwino, Mlongo, ine ndikudziwa izi zikutanthauza mochuluka kwa inu, ndipo izo zikutanthauza mochuluka kwa ine kuti inu muiketo chidaliro chanu kuti ine ndingakuuzeni inu choonadi. Tsopano kumbukirani, Baibulo linati, “Pamene inu mudzikongoletsa, musati muzidzikongoletsa n—ndi ngale zodula, ndi ngale, ndi mtundu wonse wa kuvala kwa miyala yonyezimira, koma mulole kuti kukhale kudzikongoletsa kwa mtendere, ndi bata, ndi mzimu wofatsa (zimene ine ndangobwereza kumene), chimene chiri cha mtengo waukulu pamaso pa Ambuye.”

⁶⁵ Tsopano, ine sindikutanthauza pa kutero, Mlongo, kuti ngati inu mukadakhala ndi pini. . . Tsopano, izi ndi ine osati Ambuye. Ngati inu mukadakhala ndi pini imene inu mukufuna kuti muzivala, kapena ugufu waung’ono umene amuna anu akupatsani inu, kapena mwinamwake yanu—chinachake chonga zimenezo zimene inu mumavala, tsopano, kwa ine, ine sindikuganiza kuti izo ndi zoipa. Tsopano, ameneyo ndi ine ndekha. Tsopano kumbukirani, ine ndikudzipangitsa ndekha kumveka; awo ndi malingaliro anga. Koma ine ndikuganiza ndi mafikiridwe a kwa izo; ndi momwe inu mumachitira izo. Mukuona? Ndi cholinga paseri pa izo. Ndipo pamene inu

mukuona kuti izo zikugwira pa inu, ndiye chisiyeni chinthucho chokha. Koma ine ndikuganiza ngati inu mukanavala mphete yanu ya chikwati. . .

⁶⁶ Tsopano, ine ndikudziwa inu anthu Achinazerene, izo zinkakhala kuti inu simukanati mumubatize ngakhale mkazi atavala mphete ya chikwati. Mukuona? I—ine sindimakhulupirira kuti izo ndi zoyenera. Mu Baibulo iwo ankavala mphete zachikwati, kokha iyo inkakhala chibadiri ankachitcha icho, mozungulira mutu wawo, zidutswa zisanu ndi zinai za zigwinjiri pa icho. Koma i. . . izo zinkasonyeza kuti iwo anali okwatiwa. Tsopano, ine ndikuganiza zimenezo ndi zabwino bwino.

⁶⁷ Ngati akazi akufuna kuti azivala n—ndi kudzipangitsa okha kumawoneka bwino, aukhondo, monga dona, bwanji, ine ndikuganiza palibe kanthu kwa izo, kwa ine. Koma pamene inu mufika pomapita kumakachiika chinthu icho mochipangitsa icho kukhala mwakunyada pang’ono, ndiye inu mukulakwitsa. Ndi cholinga chanu.

⁶⁸ Kodi inu akazi mukukumbukira kuno si kale litali iwo anali ndi chimene iwo ankachitcha “masiketi oyalutsa”? Ine ndikuganiza iwo akubwera nazonso, kapena iwo anafika moipa. Kukhala. . . Eya, iwo ndi, “otonzetsa” tsopano mmalo mwa, “kuyalutsa.” Koma iwo anakonda kukhala ndi seweru si kale litali. . . Iwo ankakhala ndi asungwana, akazi achichepere. . . Ndipo ndithudi, achikulirewo nawonso ankachita nawo izo, chifukwa iwo ali—onsewo amafuna kuti azikhala aang’ono. Ine sindikutanthauza inu alongo, ine ndikutanthauza akazi a mdziko. Ndipo iwo amadula awo—masiketi awo mpaka apa, pafupi utali wa phazi nthawi iliyonse, ndiye amavala mtundu wina wa chovala chamkati chowoneka mokongola. Ndipo pamene iwo akuponda patsogolo, iyo imawonetsa chovala chamkaticho chokhala ndi chilesi, ndi matakisi, kapena chirichonse chimene chinali pa izo. Chimene, inu mukudziwa. . .

⁶⁹ Uko kunali—msungwana anabwera kwa ine, amene anali msungwana wachi Dunkard, anali atangolandira kumene Mzimu Woyera. Iye anali wa mu Assemblies of God, ndipo uko kunali ku Fort Wayne, Indiana, kumene ine ndinakakwatitsidwirako. Ndipo iye anabwera kwa ine, dona wabwino wamng’ono, ndipo iye anati, “M’bale Branham, ine ndikufuna kuti ndikufunensi inu funso.”

Ine ndinati, “Chabwino, Mlongo, kodi ndi chiani ilo?”

Iye anati, “Kodi inu mukuganiza kuti ndi zolakwika kuti msungwana kwa—msungwana wa Chikhristu kuti azivala ‘siketi yoyalutsa’?”

Ine ndinati, “Mlongo, ichi ndi chinthu chimodzi i—ine sindingathe basi kuchimvetsa. Kodi ‘siketi yoyalutsa’ndi chiani?” Ndipo iye anandiuza ine chimene iyo inali. I . . .

Iye anati, “Iyo imawonetsa zamkati mwa siketi.”

⁷⁰ Ine ndinati, “Nch—nchiani chiri mwa akazi chimene chingamamupangitse iye kufuna kuwonetsa zovala zake zamkati kwa mwamuna wina? Nchiani chingati . . . Nchiani—ncha ntchito yanji kwa msungwana wa Chikhristu kuti azichita chinthu chonga chimenecho? Kodi inu mungati mulingalire Mkhristu?”

⁷¹ Tsopano, taonani, mwamuna, iye alibe zochuluka chotero pamene izo zifika ku thupi. Ndipo iye, ngati iye akanamapita wamaliseche mwatheka, izo sizikanati—apo sipakanakhala choyalutsa kwa izo. Osati kumutchingira mwamunayo, koma iwo . . . Inu mukudziwa kuti—ndi mkazi wa mtundu wanji amene angayesedwe ndi mwamuna atavula malaya ake ndipo atavala kabudula kapena chirichonse chimene iye akanakhala nacho? Chinthu chachikulu chowoneka mokandapalacho, icho chimawoneka chonyansa ndi chodwalitsa, ine—moipa. Kamuoneni mwamuna uyu kunja uko . . . Chabwino, ine ndikuganiza izo zingamupangitse mkazi kusanza kuti ayang’ane pa chinthu choterocho. Ngati iye anali . . . Koma tsopano, inu mumutenge mkazi ndi kumuika iye monga choncho, uyo ndi kachisi wosiyana. Inu mukumvetsa? Chabwino.

⁷² Koma ine ndikuganiza tikanena za ugufu, kapena . . . Tsopano, ngati inu mungamapite kumakadziunjikira nokha ngati kuti inu mumadutsa mu sitolo ya teni senti kuno mutavala maginito pa inu, i—ine ndikuganiza kuti . . . Ndikhululukireni zimenezo, ine sindimatanthauza kuti ndinene izo monga choncho, koma izo—uko nkulakwitsa.

⁷³ Ngati chirichonse chinanditembenuza ine nthawi yoyamba motsutsana nazo—chinandipangitsa ine kuchita manyazi ndi Amereka, chinali . . . Ine ndinali mu Switzerland tsiku lina, ndipo M’bale Arganbright ndi ine tinapeza malo abwino uko pafupi ndi Lausanne kumene ife tikanakhoza kupeza nyama yaikulu, yabwino, pafupi kukula *chonchi*, yolemera pafupi firii kotala ya paundi, ine ndikuganiza, kwa pafupi masenti sate mu ndalama za Chimereka. O, ife tinali kukhala ngati mafumu! Tsiku lililonse ife tinkapita kumeneko. Ndipo onse awo kumeneko amamwa vinyo, inu mukudziwa; madzi awo si abwino. Ndipo ine sindikanamamwa vinyo ameneyo, kotero ine ndinadzipezera ine chigubu chaching’ono kuchokera ku—sitolo ya zakudya chimene chinali ndi madzi otchededwa. Ndipo ine ndinkanyamula chigubu chimenecho kulikonse kumene ine ndinkapita. Ine ndikulingalira kuti aliyense ankaganiza, “Mnyamata uyo akunyamula mowa wake wake.” Kotero ine ndinkakhala nacho icho mdzanja langa. Ife tinapita uko ku malo awa kumene onse—ankagulitsa nyama zoterezi, ndipo tsiku

lina *Abiti Amereka* anayendetsa nabwerako. Pafupi galimoto ya Chevy modelo '28, anali ndi kagalu kakafupi atakaika pa chilolo ndipo anakabweretsa ako mkati umo, ndipo iye anali ndi zokwanira. . . Akazi awiri amenewo anali nayo miyala yonyezimira ya ku sitolo ya teni senti, zinthu zazikulu, zazitali, ndi ndolo, ndipo zikulendewera patali pansi, ndi utoto; ndipo onse a iwo usinkhu wa zaka fifite, okalamba ngati ine. Ndipo inu mukanaganiza kuti iwo amafuna kuti akhale ali fifitini. Koma kodi iwo amayesera kuti achite chiani? Iwo akuyesera kuyendetsa pa msewu wa moyo akuyang'ana pa kalilole wa mmbuyo, kuyang'ana mmbuyo ku zimene iwo anali kale.

⁷⁴ Tsopano, Mkristu samachita zimenezo. Mkristu samayesera kumachita zomwe iye sanali kale; iye sali kuyang'ana kumene iye anakhala ali, iye akuyang'ana kumene iye anali. Mwaona, mukuona? Musati muzisamala pa zimene munali kalelo; inu munazikhala kale zimenezo. Inu simudzabwerera konse kwa izo; izo ziri mmbuyo. Ndipo munthu aliyense amene angamayendetse pa msewu wamoyo akuyang'ana pa kalilole wammbuyo angachite ngozi; ndipo chomwechonso inu pa msewu wa Chikhristu uwu. Musati muziyang'ana mmbuyo ku zimene inu munali, ziyang'anani kuzimene inu muti mukhale muli. Paulo anati, “Kuiwala zinthu izo zimene ziri za mmbuyo, ine ndikulimbikira kupita ku malo a kuitana kwapamwamba.”

⁷⁵ Tsopano, koma izo zinakuchititsa iwe kumva manyazi. Iwo anabweretsa galu wamng'ono uyu, wokalamba wonunkhayo mmenemo ndipo anamukhazika iye pa tebulo apo! Tsopano, izo zikanamupangitsa aliyense kusanza! Ndi kumasewera naye galu ameneyo apo pomwe, atamukhazika iye apo ndi manja awo, ndiyeno nkuyamba kumadya ndi manja omwewo! Ndipo woperekera zakudya anabwera apo pomwe, ndipo anadzayankhula chinachake. Dr. Guggenbuhl anali ndi ine; iye anayamba kuseka, ndipo anapotoloza mutu wake.

Ine ndinati, “Nchiani—kodi akuti chiani?”

Anati, “Woperekera zakudyayo anati, ‘Nchotseni ameneyo apo!’”

Iwo anati, “Ayi, iye ndi Wachimereka; msiyeni iye yekha.” Mwa kuyankhula kwina, “Iye samadziwa mwa ubwino uliwonse.” Mukuona?

⁷⁶ Pamene ine ndinafika ku Saint Angelo ku Roma (tsopano, ganizani za izi), ku Vatican mu Roma, Italy, iwo anali ndi chikwangwani uko ku Angelo Woyera: “Kwa akazi Achimereka: Musanalowe mmanda awa, chonde valani zovala polemekeza okufa”—mpingo wa Katolika. Mukuona?

284. Funso: M'bale Branham, kodi Mkwatibwi adzakhala ali kuti pamene dziko likuphulika ndi kuwotchedwa lonse? Kodi Iye adzakhala ali ku malo monga ana a Israeli analiri

mu Gosheni pamene miliri inkagwa? Kodi Mkwatibwi adzakhala ali pa dziko lapansi pamene izi zikuchitika? Ngati ziri choncho, nkuti? Ndipo kodi Mkwatibwi yense adzakhala ali pa malo amodzi pa nthawi ya mkwatulowo?

⁷⁷ Mkwatibwi, pamene dziko lapansi likuphulika...Nthawi ya mkwatulo kudzakhala kuli kudzutsidwa kwa akufa ndi kusonkhanitsa palimodzi kwa amoyo, kuti—ndi amoyo, kuti mkwatulo uchitike. Tsopano, koma Mkwatibwi...Tsopano, onani, mmodzi wa iwo ndi mkwatulo kumbuyo komwe kuno zisanafike Zakachikwi. Ndipo pamene dziko liwotchedwa lonse nabwerera kuno zitatha Zakachikwi ndi pambuyo pa chiweruzo chaku Mpando Woyera. Mukuona? Oyera adzamanga misasa mofalikira pa nkhope ya dziko lapansi pamene Satana akubwera apo kudzazungulira Mzinda wokonedwawo ndipo Mulungu navumbitsa mvula ya moto ndi sulfure kuchokera Kumwamba ndi kuwawononga iwo. Chabwino. Tsopano, ilo ndilo Lemba.

285. Ndiponso, M'bale Branham, ine ndikukhulupirira mkazi ayenera kumakhala akumvera kwa mwamuna wake. Koma ngati mkazi wa Chikhristu ali ndi mwamuna wochimwa amene samakhala ngakhale kwa umodzi wa utumiki wanu—kubwera kwa umodzi wa utumiki wanu ndipo safuna—ndipo amafuna mkazi wake kuti azichita zinthu, kumadula tsitsi lake, kumavala zazifupi, ndi kumapita ku malo opanda umulungu, kodi mkazi ameneyu akuyenera kumakhala womumvera mwamuna uyu mwa njira iyi? Chonde talongosolani izi momveka bwino, pakuti ili ndi funso limene limafunsidwa mowirikiza.

⁷⁸ Ayi, Mlongo, inu simukuyenera kumamumvera munthu woteroyo. Ayi ndithudi. Pa chifukwa ichi inu mudzasiya chirichonse ndi kumamatira kwa Mulungu. Tsopano, chinthu... Ngati inu mukufuna—mwamuna ameneyo akamafuna kuti azikhala ndi inu, ndipo inu kuti mukhale—mukhale muli Mkhristu...Koma ngati iye azikupangitsani inu kuti muzivala zazifupi, kumadula tsitsi lanu, ndi kumachita zinthu zonse izi, ndi malo opanda umulungu, inu mufune poyamba Ufumu wa Mulungu ndi chirungamo Chake. Inu simuli omangidwa kwa munthu wonga ameneyo. “Koma bola ngati,” Baibulo limati, “pamene mkaziyo akukondweretsedwa ndipo mwamunayo akukondweretsedwa kuti azikhalira palimodzi (inu mukukumbukira zimenezo?), siyeni iwo...”

Ndipo tsopano, awa, ine sindinawalembe Malembawo, chifukwa ine ndinangozitenga izo apo (inu mukuona?) maminiti angapo apitawo. Ine ndikumatenga limodzi pano ndi kenako pakuti ine ndiribe nthawi...

⁷⁹ Koma Paulo ananena kuti bola ngati iwo—mwamuna wosakhulupirira ali ndi wosakhulupirira—kapena mkazi wokhulupirira kapena zina zotero, muloleni mkazi

wokhulupirirayo atsalebe ndi mwamuna wokhulupirirayo, bola ngati izo siziri motsutsana tsopano kwa Mulungu. Ngati iye akukondweretsedwa kumakhala naye iye... “Pitirirani nazo, Wokonedwa, ngati iwe ukufuna kuti uzipita ku mpingo, zimenezo ziri bwino bwino; koma ine sindimapita. Ine sindikhulupirira mu zimenezo; ine ndiribe kanthu kochita nazo zimenezo. Koma iwe zipitirira nazo; zimenezo ziri bwino bwino.” Koma pamene iye angamati, “Iwe sungati uzichita zimenezo,” tsopano pamenepo pali chinthu chosiyana. Iwe Sindinu omangika kwa zimenezo ndiye; inu mudzipatule kwa chirichonse chifukwa cha Mulungu.

286. M’bale Branham, kodi ziri (Tiyeni tiwone)...kwa munthu yemwe ali naye—yemwe ali naye mzake wamoyo, wosudzulidwa yemwe anakwatiranso asanabwere mu Uthenga kuti angamatumikire?

⁸⁰ Chabwino, mu 1 Timoteo 3:2, ngati inu mukufuna kuti muzilemba zimenezo apo, ndi Tito 1 mpaka 6 (Ine ndinazilemba izo apa), ine ndikufuna inu kuti muwerenge zimenezo kwa funso ili. Mukuona? Ngati mwamuna—ngati mwamuna akukhumba udindo wa bishopu kapena mlaliki (chinachake cha mu mpingo), iye akuyenera kukhala ali ndi mkazi mmodzi yekha. Ndiko kulondola! Mtumiki. Tsopano, apo ndi 1 Timoteo 3:2, ndi Tito 1 mpaka 6. Tsopano, Tito 1 mpaka 6, eya! Chabwino. Tsopano, zindikirani kuti Baibulo linanena kuti mwamuna uyo yemwe ali mtumiki mu nyumba ya Mulungu azikhala ndi mkazi mmodzi. Tsopano.

287. Wokonedwa M’bale Branham, pafupifupi zaka khumi zapitazo Mulungu anakomana nane tsopano ndipo anachiza chimene mphatso ya chikondi—kapena anaulula chimene mphatso ya chikondi inali, ndipo mofanana ndiye pemphero langa ndi la—kuti ine ndikufuna ndibwerere. Kodi ine ndidzailandira iyo ine ndisanafe? Kodi mwamuna wanga adzawamva Mawu, ndipo kodi ine ndichite chiani?

⁸¹ Ilo ndi lochuluka mwa funso. Tsopano, iye anati... Tsopano, zimene izo ziri apa, kapena—iye anati, “Mwamuna wanga,” kotero ine ndikulingalira kuti uyo akuyenera kukhala ali mkazi yemwe amanena iziyu. Tsopano, iye anataya chikondi chake choyamba. Mukuona? I—iye anafika pozizira mu Mzimu. Tsopano, Mlongo, mwinamwake chifukwa inu mumabwerabe ku mpingo ndi kumachita zimene ziri zolondola, inu simunataye chipulumutso chanu, koma inu mwataya chimwemwe cha chipulumutso chanu. Davide analirira kwa Ambuye nthawi ina, “Ambuye, bwezeretsani kwa ine chimwemwe cha chipulumutso changa.” Inu mukadali apabe Mkristu, Koma c—chimene inu mukufuna kuti muchite, Mlongo, ndi kumasula ndi kusiya chirichonse chimene inu mukuchidziwa momwe ziri, ndi kumamufunafuna Mulungu, ndi kumapemphera.

⁸² “Kodi mwamuna wanga adzawamva Mawu, ndipo kodi ine ndiwoti ndichite chiani?” Monga ine ndinanena mmawa uja, ingokhalani muli wamchere: “Inu ndinu mchere wa dziko lapansi.” Amuna anu aziyang’ana moyo wanu wosadziipitsa, ndipo mwamuna yemwe ali wosakhulupirira adzayeretsedwera kwa Ambuye ndi mkazi wokhulupirira. Muzingomawafunafuna Ambuye, khalani wodzichepetsa, ndi kumapemphera nthawi zonse, kumamupatsa Mulungu matamando, ndi kukhala achifundo kwa mwamuna wanu bola ngati iye akulolera kuti azikhala ndi inu mwanjira imeneyo.

288. La mautumiki a Lamlungu: Ngati mkazi achita cholakwika ndi...(Tsopano, dikirani miniti; ine kuli bwino ndiwerenge izi poyamba kwa ndekha. Inu mukuona? [M’bale Branham awerenga funsolo kwa yekha—Mkonzi.] Chabwino. Izi ndi zabwino bwino.) **Ngati mkazi achita cholakwika ndi—mwamuna wokwatira, nalapa ndi kuchikonza icho ndi mwamuna wake molingana ndi Malemba, kodi iye amasowanso kuti apite kwa mkazake wa mwamuna amene anachita naye, ngakhale ngati mkazi uyu sakudziwa kalikonse ka izo; kapena kodi iyo ndi ntchito ya mwamunayo kuti amuuze iye poyamba; kapena kodi iye akusowa kuti apwetekedwe nazo konse? Kodi tingamapite patali bwanji ndi kukonza uku pamene izo zatha ndipo zachitidwa, ndi pamene ubwenzi ukukhudzidwa?**

⁸³ Chabwino, Mlango wanga wokoneddwa, pali chinthu chimodzi chokha chimene inu mwachita chomwe chiri cholondola. Inu munachita nao, ine ndikulingalira, kapena winawake yemwe inu mukumudziwa amene anachita nao, mu kachitidwe kolakwika, kuti inu munatenga mwamuna wa wina ndipo munachita naye dama. Ndipo pamene inu munatero, pamenepo inu munagwa nkuchoka ku chisomo chanu. Ndiye inu munalapa, ndipo inu simukanakhala kuti mwalapa mpaka inu mutabwerera kwa mwamuna uyu ndi kukazikonza izo. Inu mumayenera kuti mumutenge mwamuna wanu ndi kupita kwa mwamuna uyo, chimene inu munachichita. Ndipo chimenecho chinali chinthu chimene inu munayenera kuchichita; ilo ndilo Lemba—inunayenera kuzichita.

⁸⁴ Dona anabwera kwa ine si kale litali wochokera komwe kuno mu Louisville, yemwe iye, ngati mkazi wamng’ono, iye anathamanga ndi mwamuna n—ndiyeno i...Iye ankadziwa kuti iye anali akuchita zolakwika. Ndipo iye anachoka mu mzindawo, ndipo anapita ku mzinda wina kutali, ndipo anakasintha dzina lake, anakakhala ndi anthu ena. Ndipo mwamuna uyu anamutsatira iye ndipo anakamuza iye pamene iye anakafika kumeneko, iye anali ndi zabwino pa mkaziyo. Iye ankayenera kuti akhalabe ali mkazake mwalamulo wamba kwa mwamunayo kapena iye akanaziwulula. (Ndipo pamene iye anali kumeneko, iye anakwatiwa ndi bambo wabwino wa

Chikhristu.) Ndipo anati ngati iye sakanatero, iye akanati achiphulitse chinthu chonsecho—anamuwopsyeza iye; kotero, iye ankachita kumakhala ndi amuna onsewo, chimene iye anachita molakwika, mmalo mosonyeza manga ake poyambirira. Ndipo iye anali ndi mwana, ndipo tsopano, msungwanayo ali pafupi wausinkhu wa zaka eyitini ndipo sakudziwa uti kwenikweni amene ali bambo wake enieni. Tsopano, iye akufika mu kusintha kwa uzimayi, ndipo izo zinamupezano iye. Tsopano, kodi iye angachite chiani? Ine ndinati, “Pali chimodzi chokha. . .”

Iye anati, “Ngati ine ndimuuza mwamuna wanga, iye andisiya ine; ndipo ngati ine—mwana wanga wamkazi akadziwa izo, iye adzipha.”

⁸⁵ Ndipo ine ndinati, “Ngati iwe uchisunga icho mu mtima wako, iwe upita ku gehena. Tsopano, dzisankhire wekha.” Pali chinthu chimodzi chokha choti uchite, ndi kuti utsuke mbale yakoyo. Ndiko kulondola ndendende. Khala woonamtima.

⁸⁶ Inu mukudziwa, nthawi zambiri mu masomphenya, momwe anthu amabwerera, akazi ndi amuna; Mzimu Woyera umazifukulamo zinthu zimenezo zomwe iwo anazichita mmusimo mu moyo ndipo (inu mwamvapo za izo ndipo inu mwaziwona izo, inu mukudziwa. Mukuona?)—ndi kuwauza iwo zinthu zimene iwo akuyenera kuti achite izo.

Iwo amati, “Chabwino, i—ine ndinazikonza kale izo ndi Ambuye.” Koma inu muli nazo ngongole kwa mwamuna wanu kapena kwa mkazi wanu kuti mupite mukawauze iwo. Ndiko kulondola. Inu mumayenera kuti muzivomereze izo.

⁸⁷ Tsopano, munthu uyu, ngati ali iye yemwe ali wolakwa, iye anazichita izo; iye anapita kwa mwamuna wake. Tsopano, inu mwadziyeretsa nokha, Mlongo, chifukwa pakati. . . I—inu munachita chigololo molakwira mwamuna wanu. Inu munapita kwa mwamuna wanu ndipo munadzikonza nokha kwa mwamuna wanu, ndiyeno inu munapita kwa bamboyo ndi mwamunanayo ndipo munakadziyeretsa nokha kumeneko. Inu mwakonzeka. Ngati mwamuna wanu apitirira k—kufuna kuti azikhala ndi inu, izo ziri kwa iye. Iye sakusowa kuti achite izo tsopano, koma i—koma ngati iye akufuna kuti azikhala ndi inu ndi kukukhulukirani inu, ndiye inu mukhale dona mokwanira kuti musadzakhale olakwa konse kwa chinthu choterocho kachiwiri. Koma ngati iye sakukhulukirani inu, ndiye imeneyo ndi—imeneyo ndi ntchito yake. Iye akhoza kukusiyani inu. Kulondola ndendende.

⁸⁸ Koma tsopano, mwamuna amene inu munachita naye mchitidwewo, tsopano, iye ndi amene akuyenera kuti apite kwa mkazi wake ndi kukamutenga mkazi wake ndi kubwera nayenso kwa inu. Inu mwachita gawo lanu, tsopano ndi nthawi yake kuti iye achite gawo lake. Mukuona? Gulu lachiwirilo. . .

⁸⁹ Mkazi uyu anachita mchitidwewo ndi mwamunayo, ndipo iye anamutenga mwamuna wake, anavomereza izo, ndipo anapita kwa mwamunayo ndipo anakavomereza izo, ndipo anazikonza izo bwino. Tsopano, mwamuna winayo anali mwamuna wokwatira nayenso; tsopano, iye akuyenera kuti apite kwa mkazi wake ndi kukamutenga mkazake ndi kubwereranso kwa mkazi uyu. Ndiye izo zonse ziri bwino. Mukuona zimene ine ndikutanthauza? Izo zakonzedwa ndiye. Koma kunja kwa izo, inu mukanali wolakwa, ndipo pansu pa mtima wanu inu mukhala mukutsutsika.

⁹⁰ Ine ndinali ndi mkazi si kale litali uko yemwe anali nacho icho kuyambira pa Nkhondo Yoyamba ya Dziko lonse. Ndipo iye anati, “O, M’bale Branham.” Iye anali atataya mazana a madola pa azamisala ndi chirichonse. Ine ndinali nditakhala pamenepo ndikumuyang’anitsitsa iye mu chipinda chimenecho. Meda anamubweretsa iye kumeneko. Iye anali atakhala pamenepo akupotokola kampango mmanja mwake monga choncho, anati, “Ine ndikumverera kuti dziko likuti liphulike, ndipo ine...” zonse monga chonchi.

Ine ndinangopitiriza kukhala pamenepo. Ine ndinati, “Tsopano, pali chinachake cha...Inu muli ndi chinachake mmoyo mwanu penapake?”

“Ayi, ine ndine mphunzitsi wa Sande sukulu.”

Ine ndinati, “Chabwino.” Ndinakhala pamenepo pang’ono pokha ndipo ndinayang’anitsitsa. Ine ndinati, “Ine ndikuwona galimoto yaing’ono yobiriwira, ndipo inu muli ndi bambo wa mutu wa bulondi, ndipo sitima inali pafupi kuti iyigunde galimotoyo.”

...?. . .Iye anati, “Inu musati mumuuze wina aliyense zimenezo!”

Ine ndinati, “Amuna anu anali ali mu ankhondo pa nthawi imeneyo.”

Iye anayamba kulira, analumphira mmwamba, “Inu musati mudzanene zimenezo kwa wina aliyense.” Mwaona? Zimenezo zinali patali pansu mu chikumbumtima chake. Iye anati, “Ine ndinalapa zimenezo kwa Mulungu kale kale.”

⁹¹ Ine ndinati, “Koma dikirani miniti. Inu simunachite chomulakwira Mulungu. Inu munachita cholakwira lumbiriro lanu la chikwati. Inu muyenera kuti mubwereranso kwa mwamuna anu ndi kukakonza kaye zimenezo poyamba.”

Iye anati, “Iye andisiya ine.”

Ine ndinati, “Mulungu wakusiyani inu mulimonse. Kotero tsopano, ndi uti amene inu mukufuna kuti akusiyeni inu?” Ine ndinati, “Pitani kwa iyeyo.”

Ndipo iye anati, “O, i—i . . .Iye akachita *izi*, ndipo ine ndiri naye ana awiri.”

Ine ndinati, “Chabwino, izo ndi zonse zimene ine ndingakuuzeni inu. Azamisala sanathe kuzikoka nkuzitulutsa nkomwe zimenezo mwa inu, koma Mzimu Woyera waziwulula; ndipo ine sindinayambe ndakuwonanipo inu mmoyo wanga.”

Iye anati, “Uko ndiko kulondola ndendende!” Anati, “Chabwino, i—ine sindingathe basi kumuuzza iye.”

Ine ndinati, “Chabwino, i...Ndakondwera kuti ine ndinakomana nanu.” Anapita mu chipinda china, ndipo iye anabwereranso mkati umo.

Meda anati, “Iye akukufunani inu mkati umo kachiwiri.”

Ine ndinapita mmenemo; ndipo ine ndinati, “Inu mukufuna chiani?”

Ndipo iye anati, “M’bale Branham, ine sindingathe kukamuuzza izo mwamuna wanga!”

Ine ndinati, “Mwamuna wanu ndi bambo wa mutu wakuda.”

“Eya!”

Ine ndinati, “Iye ali nacho chinthu chofanana choti achilapire kwa inu.”

Iye anati, “O, ayi osati mwamuna wanga!”

Ine ndinati, “Inu zikhala bwino kuti mupite mukamutenge iye ndi kukabwera kuno.” Ine ndinati, “Kodi inu mukumudziwa mkazi *winawake*, yemwe amavala diresi la pinki, amene amagwira ntchito mu ofesi ya kampani ya mtundu *winawake* wa magalimoto?”

Iye anati, “Zedi!”

Ine ndinati, “Kodi iwo samamutcha iye dzina *lakuti*?”

“Eya!”

Ine ndinati, “Masabata awiri apitawo iwo anakhala pansu pa mtengo wa mthundu ali n—atakhala mu galimoto ya bulauni ya Chevrolet ili ndi nambala ya lainsensi yake *yakuti-ndi-yakuti*, ndipo anali mu kachitidwe komweko.”

Iye anati, “Ayī osati mwamuna wanga!”

Ine ndinati, “Chabwino, inu pitani mukamutenge iye ndi kukabwera kuno.”

Iye ananyamuka. Maminiti pang’ono, apa iwo anabwereranso. Iye anati, “Izo ndi zoonala!”

Ine n—ine ndinati, “Inu mukuona? Tsopano pitani mukamuuzze Mulungu!”

⁹² Koma poyamba, pamene inu mubwera pa guwa ndipo mukakumbukira kuti pali mangawa, pitani poyamba ndi kukachikonza icho. Ndipo utali wonse pamene mbali ina iyi apa ili yolakwa pa kusakamuuzza mkazi wake...Mkazi uyu wadziyeretsa yekha. Tsopano, ziri kwa iyeyo ndi mwamuna

wake. Koma mwamuna winayu ndi mkazi wake ayenera kuti abwere poyera mu zimenezo. Ndipo inu simungathe... Ziribe kanthu zimene inu mungachite, izo zizikuzunani inu utali wonse pamene inu muli moyo mpaka inu mutazitsuka izo nkuyera. Pali njira imodzi yokha yoti mungachitire izo: Vomerezani izo. Ngati izo zisenda khungu pa inu, kazichiteni izo mulimonse. Kaneneni zoon, ndiye inu mwazikonza izo bwino. Amen!

⁹³ Ine ndikutha kumva ochuluka pa tepi akuti, “Uko nkulakwitsa.” Koma inu mudzangoziyesa izo nthawi imodzi ndi kudzawona ngati izo siziri. Chabwino.

289. Funso la Lamlungu mmawa” (Pepani kuti ndi nthawi ino, koma . . .) **Pa nthawi ya kulandira Mzimu Woyera, kapena ubatizo wa Mzimu Woyera, kodi apo pamakhala kusi yana? Kodi munthu amayankhula ndi malirime? Ngati si nthawizonse, ndi ziwonetsero zotani zimene zimadziwika?**

⁹⁴ Chabwino, kodi inu mungati mulingalire mayi kubala mwana ndipo nkusazidziwa izo? Iye ayenera kuti anali atakomoka kuti asazidziwe izo. Ngakhale inu simungalandire Mzimu Woyera popanda kudziwa izo. Pali chinachake chimene chimachitika mwa inu. Mukuona? Pali chinachake chimene chimakusinthani inu. Kachitidwe kanu konse, kachitidwe kanu konse kuzimu kamapangidwa mwatsopano kachiwiri, ndipo inu mumakhala cholengedwa chatsopano mwa Khristu, momwe Baibulo limaziikira izo, *cholengedwa chatsopano* mwa Khristu. Inu mumazidziwa izo.

⁹⁵ Tsopano, inu mukuti, “M’bale Branham, ndiye inu simukukhulupirira kuti munthu amayenera kuyankhula ndi malirime kuti alandire Mzimu Woyera.” Osati kuti atsimikizire kuti iye ali nawo Mzimu Woyera.

⁹⁶ Ine ndikanafuna membala aliyense wa mu mpingo wanga akanamayankhula ndi malirime. Ine ndikanakonda iwo kuti azichita zimenezo, ndipo ngati—ine ndikukhulupirira ngati inu mutamupempha Mulungu, Mulungu adzapereka izo kwa inu. Koma ndiroleni ine ndikuuzeni inu; ine ndikuwadziwa anthu ambiri amene amayankhula mu malirime ndipo ali opanda Mzimu Woyera. Ndipo palibe mtumiki amene ali owona kwa iyemwini ndi kwa osonkhana ake amene sangawauze osonkhana ake chimodzimidzi. Mdierekezi akhoza kusanzira zimenezo.

⁹⁷ Paulo anati, “Ngakhale ine ndingayankhule ndi lirime la anthu ndi angelo, ngakhale ine ndingapereke thupi langa kuti liwotchedwe ngati nsembe, ngakhale ine nditamamvetsa zinsinsi zonse za Mawu, ngakhale ine nditapereka katundu wanga yense kwa osauka, ndi zinthu zonse izi, ndi kukhala wopanda chikondi, ine apobe sindine kanthu. Ine ndikakhala nacho chikhulupiriro chakuti ine ndikhoza kusuntha mapiri ndi zina zotero; ine

apobe sindine kanthu.” Ndiye iye anati, “Icho chimene chinali chamderamdera chidzathetsedwa pamene icho chimene chiri changwiwo chibwera,” kapena “pamene icho chimene chiri changwiwo chapangitsidwa kudziwika.”

Tsopano, ine ndiri ndi funso pa zimenezo. Ine ndikuyembekeza ine ndifika kwa ilo usikuuno, la zimene zinachitika pamene Zisindikizo zinatsegulidwa. Ndipo ine ndikuganiza mwinamwake izo zifika kumene kwa inu pa funso ili.

290. Funso: M’bale Branham, kodi ife tichite chiani? Chinachake chakhazikika pa ine mwakuti ine sindikutha kubooleza. Pa Kugwa masamba kwapitaku, ine ndinalota ine ndinali nditataika mu mchenga woyera. Kunali kukuyamba mdima; ine sindinkatha kupeza njira yanga. Loto ili lakhala ndi ine chiyambireni pa kugwa masamba kwathaku. Tsopano, ine ndiri ngati wina wopambaza mu mdima. Mwana wanga (E-r-v-...), Ervin, ndi mkazake anali nawo mu loto langalo. Tsopano, iwo nawonso ali mu mdima. Ife tiri mu kusimidwa—ife tiri mosimidwa. Ine ndikukhulupirira Mulungu akusonyezani inu zomwe ziri—zimene ziri mu mitima yathu tsopano. (Akazi a...O, chabwino.) Ngati ife tiri kulakwitsa kapena malo ochimwirapo, tiuzeni ife. Ife tikufuna kuti tikhale olondola.

⁹⁸ Ine sindikumudziwa donayo, koma ine ndikungomverera ngati inu muli pano, dona, kuti vuto lanu ndi ili. Inu mwalola chinachake kuchitika kwa inu chimene chakupangitsani inu kukhala amanjenje, chifukwa kukhala mu “mchenga woyera” zimaimira ungwiro ndi chirungamo. Ndipo inu mukungomulola Satana kuti ayike china pamwamba pa inu. Loto lanu likutsimikizira kuti palibe chinthu cholakwika. Inu mwangokhala wamanjenje, ndipo pochita izi ndi kuganiza izi, inu mukulipangitsa banja lanu lonse kukhala lamanjenje. Siyani kuchita zimenezo; dzitengereni maufulu anu opatsidwa ndi Mulungu. Loto lanu likutsimikizira mwa kutanthauzira kuti inu muli mu mchenga woyera. Chirichonse chiri bwino bwino. Ndi inu, eniake, muli amanjenje.

⁹⁹ Ndipo inu mukamusiya mmodzi wa mu banja lanu kukhala wamanjenje, izo zimapita kwa wina wakeyo, ndi wina wakeyo, ndipo chinthu choyamba inu nonse mukungokangana ndi kupitiriza nazo. Ndipo membala mmodzi wina wa banjalo akakhala ngati wasokonezeka ndi chinachake, icho chimamusokoneza wina, ndi wina, ndi wina, chinthu choyamba inu kuchidziwa banja lonse lasokonezeka. Ndi Satana. Ndiye ngati mmodzi wina wa banjalo akusangalala, aloleni ena onsewo azisangalala palimodzi nawo. Koteru wina aliyense wa banjalo aziyesera kuchita izo.

¹⁰⁰ Ziyeserani, aliyense wa ana inu, kuti muziwathandiza abambo anu, amayi. Amayi, inu... Bambo, inu muziyesera kuwathandiza ana. Musati muzilola kulunda uko, mzimu wosakhulupirira kufika pomwe inu muli. Inu ndinu Akhristu. Inu ndinu obadwa mwa Mzimu wa Mulungu. Inu ndinu mchere wa dziko lapansi. Inu muli nawo maufulu opatsidwa ndi Mulungu. Ndipo Baibulo linati, “Ngati pali matamando aliwonse, ngati pali ukoma uliwonse, ziganizirani pa zinthu izi.” Musati muziganiza za chinthu cholakwika.

Ndipo Mlongo, ine ndikuganiza limenelo ndilo vuto lanu, wokonedwa Mlongo.

Ine ndikhoza kukhala pa zimenezo nthawi yaitali, koma molingana ndi zomwe ine ndinalonjeza, ndi maminiti makumi awiri okha... Ndipo ine ndikufuna kuti nditenge basi ochuluka a izi... ngati iwo sali, ayikeninso iwo pa desiki ndipo ine ndiwatenganso iwo kachiwiri.

291. Ena amati M’bale Branham ndi Mwana wa munthu. Ine ndimaganiza Lawi la Moto linali Mwana wa munthu. Kodi ine ndikulakwitsa?

¹⁰¹ Chabwino, limenelo ndi funso labwino, labwino kwambiri. Koma ine sindine Mwana wa munthu, koma mwana wa munthu. Apo pali kusiyana ndithu. Yesu Khristu anali Mwana wa munthu, Mwana wa Mulungu, Mwana wa munthu, Mwana wa Davide.

¹⁰² Tsopano, chifukwa chimene funso limenelo linafunsidwa mwinamwake munthu uyu kapena zakhala zikunenedwa, nchifukwa anthu amanditenga ine ngati mpenyi, chimene ine sindinayambepo... ine ndiri ndi funso mkati umu akungondikalipira ine pa zimenezo. Mukuona? Koma i—i—i—inu—inu... Pamene ine ndiziwerenga mafunso awa inu muziwona chifukwa chimene ine ndiziyankhira zinthu momwe ine ndizichitiramu. Mpaka ine nditsogozedwe motsimikizika kuti ndichite chinachake (mukuona?), ndiye i—ine ndidzanena zimene ine ndikuyenera kuzinena. Koma ora limenelo silinafike.

¹⁰³ Koteri ine sindiri—m—Mwana wa munthu wodzozedwayo. Ine sindimadzinenera kuti ndine mneneri Wake. Nthawi zambiri ine ndazinenapo izo pamene ine sindimaganiza kuti ine ndanena izo, ndimadzigwira ndekha pa tepi. Koma ine ndimanena zimenezo nthawizina, chifukwa ngati iwe ukufuna kuti uzimpatse izo mwa matchulidwe oti, *mneneri* ali mwa mawu a Chingerezi ali kokha “mlaliki.” Aliyense akudziwa zimenezo; katengeni dikishonare. Mukuona? *Mneneri* ndi “mlaliki” mu dikishonare ya Chingerezi. Koma mu Chihebri kapena Chigriki, *mneneri* ndi “mpenyi, wina amene amawoneratu zinthu ndi kuneneratu zinthu.” Koma mu kutanthauzira kwa Chingerezi, *mneneri* ndi “mpenyi.”

¹⁰⁴ Kotero ine sindikufuna kuti ndizidzitcha ndekha chirichonse koma m'bale wanu. Ine ndine m'bale wanu, ndipo inu muzingonditenga ine ngati M'bale Bill, kapena M'bale Branham, kapena chirichonse chimene inu mukufuna kuti muzichita pa zimenezo. I—i—izo ziri bwino, i—izo nzabwino. Zimene inu mukuzikhulupirira, sungani zimenezo kwa inueni. Inu mukuona?

¹⁰⁵ Ndipo tsopano, kodi funso lina lija linali chiani? Ine ndinafika podzikulunga mu izi, ine ndaiwala kuti zinthuzo zinali chiani. Chimodzi cha izo chinali, “Kodi ine ndinali Mwana wa munthu?” n . . . Ndi izi apa ine ndikukhulupirira. “. . . Mwana wa munthu kapena kodi Lawi la Moto ndilo Mwana wa munthu?” Ayi! Lawi la Moto ndi Kudzoza.

¹⁰⁶ Lawi la Moto . . . Tsopano, izi zikhoza kupita mozama pang'ono kupatula mutakhala ena a inu azumulungu, Dr. Vayle, mwinamwake M'bale kuno, ndi atumiki ena awa kuno ochokera ku Arkansas, ndi amzanga abwino kozungulira, iwo mwinamwake angadziwe.

¹⁰⁷ Tsopano, Lawi la Moto lija ndi *Logos* imene inatuluka kuchokera kwa Mulungu. *Logos*, chimene chiri mochitika chobwerapo cha Chidzalo cha Mulungu. Pamene Mulungu anakhala mu mawonekedwe kumene Ichu chikanakhoza kuwonedwa, Ichu chinali kudzoza kwa Mzimu waukulu umene unachokera apo, Ichu chikudzichepetsa, kubwera pansi, Mulungu, Atate, *Logos* imene inali uko pamwamba pa Israeli, kuti . . . Iye anali woyera, sakanakhoza kupirira tchimo. Apo pankayenera kukhala nsembe ya magazi mu Edeni momwe. Ndiye *Logos* imeneyo inadzakhala thupi ndipo inakhala pakati pathu; ndi kumene *Logos* iyi inkakhala mu thupi la umunthu, lomwe linali nsembe . . .

¹⁰⁸ Pamene munthu anapangidwa mu chifanizo cha Mulungu . . . Ndiyeno Mulungu anabwera pansi mu chifanizo cha munthu kuti adzamuwombole munthu; izo zinamubweretsa munthu ndi Mulungu palimodzi. Miyamba ndi dziko lapansi zinakumbatirana ndi kupsyopsonana china ndi chimzake; Mulungu ndi munthu anakumbatirana wina ndi mzake monga Utate ndi umwana pamene *Logos* inakhala thupi ndi kumakhala pakati pathu.

¹⁰⁹ Yesu anati, “Ine ndinabwera kuchokera kwa Mulungu, ndipo ine ndikupita kwa Mulungu.” Ndi kulondola uko? Itachitika imfa Yake, kuikidwa mmanda, chiukitsiro, ndi kukwera mmwamba, pamene thupi linatengedwera mmwamba kuti likakhale pa dzanja lamanja la Mulungu . . . Tsopano, ine sindikutanthauza kuti Mulungu ali ndi dzanja lamanja, Mulungu ndi mzimu. Koma pa *dzanja lamanja* zikutanthauza “mu mphamvu ndi ulamuliro wa Mulungu.” Kutu mu Dzina limenelo chirichonse Kumwamba chikutchedwa Ilo ndipo

chikumvera kwa Ilo. Chirichonse pa dziko lapansi chikutchedwa Ilo ndipo chikumvera kwa Ilo, Dzina la pamwamba pa maina onse, Yesu Khristu.

¹¹⁰ Tsopano, *Logos* iyi imene inali mkati mwa Iye, umene unali Mzimu wa Mulungu, Kudzoza, kudzera mu chisomo choyeretsa cha Magazi, kunabalira ana aamuna ambiri kwa Mulungu, amene ali odzozedwa ndi *Logos* iyi yomwe.

¹¹¹ Tsopano, pa tsiku la Pentekoste Ilo linabwera pansi, Lawi la Moto lija, ndipo linadzinyotsola mzidutswa monga choncho, ndipo malirime a moto anakhala pa aliyense wa iwo, osati malirime awo, koma malirime a moto anatera pa aliyense wa iwo, osankhidwa, gulu losankhidwa, lozindikiritsidwa ndi Lawi la Moto ili, kusonyeza kuti Mulungu anali atadzipatulira Iyeyekha mwa munthu. Kodi inu mukuzimvetsa izi? Mulungu, *Logos*, kudzipatulira Iyeyekha mwa munthu! Mulungu, osati mwa munthu mmodzi, Iye ali mu Mpingo Wake konsekonse. Ndicho chifukwa Yesu anati, “Ntchito zimene ine ndikuzichita muzidzazichita inunso, zochuluka.” Tsopano, ine ndikudziwa King James amati, “zokulirapo,” koma kumasulira kolondola pamenepo ndi “*zochuluka* zoposa izi inu muzidzazichita.” Mulungu anaikidwa mu chotengera ndi kupanikizidwira mwa Munthu mmodzi, Yesu Khristu. Koma tsopano Iye waikidwa mu zotengera ndi kupanikizidwira mu Mpingo wa konsekonse wonse wa Mulungu wamoyo.

¹¹² Pakali pano, pamene Mulungu ali pano akuyankhula kwa ife mu mitima yathu, Iye ali ku Afrika, Iye ali ku Asia, Iye ali ku Ulaya, Iye ali ku England. Kulikonse kumene okhulupirira asonkhana palimodzi, kumeneko Iye ali pakati pawo.

¹¹³ Tsopano, itachitika imfa Yake, kuikidwa mmanda, ndi kukwera mmwamba, ndi kubwera kwa Mzimu Woyera, Paulo pa ulendo wake wopita—yemwe anali Saulo—akupita ku Damasiko, iye anakanthidwira pansi ndi Lawi la Moto, *Logos*. Ndipo Myuda uyo sakanalitcha Lawi la Moto ilo, “Ambuye,” kupatula ngati iye akanadziwa kuti Ilo linali *Logos* yomwe ija imene anthu ake ankaitatira kudutsa mu chipululu. Mukuona? Tsopano, ameneyo sanali Mwana wa munthu, imeneyo inali *Logos*.

¹¹⁴ Tsopano, ife tikunena izi ndi kulemekeza, ndi chikondi, ndi ulemu. Mukuona? Monga Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, ndiponso kuti mu masiku otsiriza, monga izo zinali isanafike nthawi ya Loti, kapena mu nthawi ya Loti mu Sodomu, chomwechonso izo zidzakhala ziri mu tsiku limene Mwana wa munthu akudziulula Iyeyekha kachiwiri, kudziulula Iyeyekha. Tsopano, mu masiku otsiriza ano *Logos* imene inali pa Yesu—chimene Iye wakhala kuchokera kwa icho kubwerera ku Lawi la Moto kachiwiri ndipo watsikira pansi pa dziko lapansi kuti (ine ndimati ndinene chinachake, koma ine ndikuyang’ana tepiyu. Iwo sangathe kuzikhulupirira izo iwe utawauza iwo.

Izo sizikanapanga kusiyana kulikonse. Iwo. . . Anthu sakanati azikhulupirire izo, koma ine ndizidumpha izo)—koma wabwera pansu kuti, monga chiweruzo chofufuzidwa chikupitirira.

¹¹⁵ Ndipo tsopano, Lawi la Moto lalikulu ili limene mwamtheradi lazindikiritsidwa ngakhale ndi makamera amwasayansi, amene ali kuno padziko lapansi lero. . . Ndi icho chithunzi cha Ilo chapachikidwa ukocho. Ine ndikukhulupirira icho chikadali pamenepo, kodi si kulondola uku? Chiri kumeneko? Zatsimikiziridwa mwasayansi ndi opambana amene ife tiri nawo. George J. Lacy, mkulu wa FBI wa kudinda kwa zala ndi zolembedwa, anati, “Ine ndinkazitcha izo kuwerenga maganizo ine mwini, M’busa Branham, koma,” anati, “kuwalako kunakhudza diso la kamera. Ine ndinaziika izo pansu pa kuwala kwa vaoleti ndipo ndinali ndikuchiyesa kuno kwa masiku anai kapena asanu. Ndipo kuwala kunakhudza maso a kamera. Ndipo maso amenewo sangatenge kuwerenga kwa maganizo!” Tsopano, zimenezo zazindikiritsidwa.

¹¹⁶ Ndiye penyani ntchito za Ilo. Ilo, pakati pathu, likutsimikizira Yesu yemweyo amene anayamba wakhalapo mu Palestina, Mzimu womwewo umene unali pa Iye wabwera pamwambapa kudzera mu Thupi mpaka Iwo wabwereranso ku Umutu kachiwiri, chimene Iye akubwera posachedwa kuti adzalitenge Thupilo. Amen! Mutu kubwera kwa Thupi. Kodi inu mukuzimvetisa izi? Ameneyo adzakhala ali Mwana wa Mulungu, Mwana wa munthu, Mwana wa Davide, INE NDINEYO, Rozi la ku Sharon, Kakombo wa Mchigwa, Nyenyezi ya Mmawa.

¹¹⁷ Ine si Iyeyo; ine ndine wantchito Wake. Ndipo Lawi la Moto si Iyeyo; Izo ziri mu mawonekedwe a Mzimu (mukuona?) umene unali pa Mwana wa munthu ndipo wabwera tsopano kuti udzawadzoze ana a munthu, kuti abweretsenso utumiki ndendende basi monga Iye anati izo zikanadzakhala ziri, polinga kuti Mutu ndi Thupi lonselo zilumikizane palimodzi.

¹¹⁸ Monga nga—ngati piramidi momwe Inoki anaimangira. Ndipo ife tikupeza mu piramidi imeneyo, iwo sanapeze konse mwalawapamutu pa iyo. Bwanji? Mwalawapamutu ndi woti ubwerabe. Masitepe asanu ndi awiri m—mu piramidi. . . Ife tidzadutsa mu zimenezo tsiku lina, ndipo ine ndikungofuna kuti ndikusonyezeni inu momwe izo ziliri kwenikweni mwangwiro ndi Lemba.

¹¹⁹ Ndipo tsopano, ngati inu mutazindikira pa ndalama yanu ya dola ya Chimereka, mwalawapamutu wawukulu uwo, diso, akuti, “Chisindikizo Chachikulu.” Iwo udzabwera.

Ndipo zindikirani miyala imeneyo. . . Kodi alipo pano aliyense anafikako konse ku mapiramidi a mu Igupto? Chabwino, ngati inu mungazindikire. . . Eya, apo pali, kuli dzanja uko limene liri mmwamba kumbuyo uko. Chabwino.

Miyala imeneyo ili kumeneko mwanawiro kwambiri, ndi pamwamba pamenepo, pamene kangati kachisoti pamwamba pa izo, pamene mwala umenewo ubwera, izo zidzakhala ngati daimondi wamkulu akukwanira bwino pansi pamenepo mwanawiro basi ndi iyo.

¹²⁰ Tsopano, mwala umenewo sukanakwanira pansi apo pa maziko a mmusiwo, komanso iwo sukanakwanira pa maziko achiwiri kapena pa maziko achitatu. Iwo udzangokwanira kokha pa maziko a pamwamba, pamene nyumba yonse yakhala yokwanira kwa mwalawo. Ndipo Yesu sangathe kubwera mpaka Mpingo, Thupi la okhulupirira ndi utumiki umene Iye anawusiyapo nthawiina udzayenera kukhala uli wofanana momwe izo zinali apo. . . . Ndiyeno, izo zibweretsa. . . . “Iwo popanda ife sangapangidwe angwiro,” Paulo anatero, Ahebri 11. “Popanda ife iwo sangapangidwe kukhala angwiro.” Iwo ayenera kukhala ndi utumiki uwu kuti awadzutse Achilutera, Achiwesile, ndi onse awo kudutsa mu mibadwo yawo. Pamene uwo ubwera, pamene gawo ilo la—kumene mphungu zisonkhana. . . . “Basi kumene kwafa nyama mphungu zisonkhanirako,” funsolo linali. O, izo ndi zangwiro basi. Ine ndikuyembekeza izo zaliyankha funsolo.

292. M'bale Branham, kodi Satana angathe kugwiritsa ntchito mphatso ya malirime kapena uneneri mwa munthu yemwe ali nao Mzimu Woyera?

¹²¹ Limenelo ndi labwino sichoncho ilo? Inde, bwana! Ngati. . . . Izo ziyenera kumayang'anidwa mwatcheru, kwambiri mbiri. Ngati inu mungazindikire mu I Akorinto 14:29, inu amene mukufuna kuti muzilembe izo. . . . Mukuona? M—munthu amene analemba izi sanalebepo dzina lake; iwo anangoti, “Mulungu akudalitseni inu.” Mukuona? Mu I Akorinto 14:29 ife tikupeza kuti mphatso iliyonse mu mpingo imayenera kumaweruzidwa poyamba. Mukuona? Inu muyenera kusamala, chifukwa mizimu yoyipa imakwawira umo. Chifukwa kumbukirani, mvula imagwera pa olungama ndi osalungama. Mvula yomweyo imene inatumizidwa kuti idzachetse tirigu nayonso imachetsa maudzu, madzi omwewo. Ndi angati akudziwa zimenezo? Tsopano, izo zikuyenera kumveketsa bwino mbewu ya serpenti kwa inu ndiye, momwe kuti mwana uyu anabwererapo. Ine ndikuyesera kuti ndizisankhe izo apa kuti ndizitenge izo nthawi yanga isanathe, koma ine sindikutha kuzipeza izo: kotero, momwe mwana uyo analiri wa mbewu ya serpenti. Mukuona?

¹²² Mulungu ali ndi lamulo. Tsopano, pa izi, mu lamulo ili la Mzimu wa Moyo inu muyenera kumayang'anitsitsa, chifukwa Satana amazembera umo.

¹²³ Ndipo Paulo, pamene chinachake chinkaululidwa kwa winawake, icho chinkayenera kukhala ndi pafupi oweruza awiri kapena atatu izo zisananenedwe pamaso pa mpingo.

¹²⁴ Tsopano, ndiponso apa ine ndikhoza kuzibweretsapo izi apo. Ine ndikuwona wanga. . . Ine sindikuganiza kuti M'bale wanga ali pano usikuuno, koma winawake ankamuseka winawake chifukwa chochoka pa kachisi ndipo anapita uko kwa M'bale Junior Jackson pofuna mpingo. Anati, "Iwo apita uko pakati pa 'mbalame zakufa.'" Kodi inu simukuchita manyazi kuti mungapange ndemanga yonga imeneyo? Yense yemwe inu muli, ngati inu muli mwana wanga pano mwa Khristu, ine ndikuchita manyazi nanu. Musati muzichita chinthu monga chimenecho. Junior Jackson ndi m'bale wanga. Don Ruddell ndi m'bale wanga.

¹²⁵ Chabwino, chifukwa chake, nchifukwa pamene ine ndinakhazikitsa mpingo kuno mu dongosolo linalake, pamene ine ndinabwerera, kuti ndidzawone ngati ine ndingadzapeze mawonetseredwe a mphatso, theka la iwo anachoka kwa izo. Chifukwa pamene iwe ukanati uziyamba kuti uyankhule, kapena kulalikira, kapena chinachake, izo zimafika. . . Izo zimafika pamalo akuti iwe unkalephera kuti ulalikire nkomwe kupatula winawake atayankhula mu malirime, winawake kutanthauzira, winawake nkupereka kutanthauzira; ndipo theka la izo sizinali kufika pokwaniritsidwa nkomwe.

¹²⁶ Tsopano, ine ndimakhulupirira mu kuyankhula mmalirime. Ine ndimakhulupirira mu kutanthauzira, koma icho chiyenera kumakhala chinachake cholunjika kwa mpingo, osati, "Ambuye akubwera posachedwa," kapena chinachake—zimene ziri zabwino. Koma, "Musati muzigwiritsa ntchito kubwereza kwachabe," Yesu anatero, "momwe achikunja amachitira."

¹²⁷ Ichu chiyenera kumakhala chinachake. "Pitani mukamuuze M'bale *Wakuti-ndi-wakuti* chinthu chinachake chimene iye anachita n—ndi kuti atenge. . ." "Kuti, pitani mukamuuze M'bale, Mlongo *Wakuti-ndi-wakuti*, pamene iye anachita chinthu chinachake kumusi uko tsiku lina, iye analakwira malamulo a mwamuna wake—lumbiriro la kwa mwamuna wake. Kupatula ngati iye akonza ichi—moyenera, Mzimu Woyera umudulapo iye." Pamenepo inu muli naye PAKUTI ATERO AMBUYE!

¹²⁸ Ndiye zibweretsani tchimo limenelo umo. Apo ndi pamene ife tiri ndi mpingo monga iwo unali pamene Anania ndi Safira anabwera umo. Ndiye ife tiri ndi mpingo umene ukuima molimba.

"O," inu mukuti, "M'bale Branham. . ." Munthu wina, ine ndinamuza iye kuti; iye anati, "Chabwino, inu mumatipanikiza ife kwambiri pa malopo."

¹²⁹ Ine ndinati, "Kodi ine sindiri pamalopo ndiye kwa alendo amene ine sindinayambe ndawawonapo mu moyo wanga? Koma ine ndiri nacho chikhulupiriro ndi chidaliro mwa Mulungu wanga yemwe anandituma ine kuti ndizichita izi, ndipo

palibe nthawi imodzi imene zinakhala ziri zolakwika kapena sizidzakhala ziri konse utali wonse pamene ziri za Mulungu.” Ndiko kulondola.

¹³⁰ Osati kuyankhula mu malirime ndi zinthu monga izo... Ine ndikukhulupirira kuti malirime amenewo ndi anthu amene ali ndi mphatso zimenezo, ngati iwo ali Akhristu enieni ndipo akukondweretsedwa nazo izo, iwo azikomana pa okha palimodzi, chifukwa—ndi kupereka malirime awo ndi kutanthauzira ndi kuwona zomwe iwo angachite kuti azipititsa patsogolo Ufumu wa Mulungu. Iwo ali nawo utumiki wawo wawo, koma uwo si uli wa pano pakati pa omvetsera kumene—ochimwa akuchitiridwa nao ndi zina zotero. Baibulo linati, “Iwo adzati inu ndinu osaphunzitsidwa.”

¹³¹ Nthawizina iwo amafika kwambiri popanda ulemu nazo—ndi zina zotero... Sikuti gulu lathu linalibe izo, koma ine ndimawalola iwo kuti apitirire nazo kanthawi. Ine ndinati, “Zipenyeni izo.”

¹³² Tsopano, ine ndinawauza abale (pali mboni pano zikudziwa izi), ine ndinati, “Zisiyeni izo zokha. Pakapita kanthawi ine—ife tidzapeza ngati izo ziri za Mulungu kapena ayi. Ngati izo sizingapirire chikwapulo, ndiye uyo ndi mwana wapathengo.” Ndipo ndendende zimene Baibulo linanena. Ndipo pamene kukwapulidwa kunabwera, chinachitika ndi chiani? Kodi ine ndinakuuzani inu izo kale kalelo? Mukuona? Afunseni abusa pano.

Iye anati, “Nanga bwanji *izi* ndi *izo*?”

¹³³ Ine ndinati, “Ingozisiyani izo zokha! Iwo ali makanda. Ife sitingati tiziweruze izo, koma penyani pamene izo zibwere kwenikweni pokanikizira pansu ku Mawu.”

¹³⁴ Tsopano, M’bale Junior Jackson anali ndi ufulu woti atsutsane nazo izo. Iye akufuna ampingo wake... Anthu onse akufuna kuti aziyankhula ndi malirime ndi zinthu mwa omvetsera. Amenewo ndi mavuto a M’bale Junior; i—izo ziri kwa iyeyo. Koma Junior Jackson amaukhulupirira Uthenga uwu chimodzimodzi momwe—wina aliyense wa ife tonse timachitira. Iye ndi mmodzi wa ife. Ndipo sikuti ndi “mbalame yakufa” kupita kumeneko. Junior Jackson ndi mwamuna wa Mulungu amene ine ndimamukonda ndi mtima wanga wonse. Ndipo sali pano usikuuno, kotero ine ndikhoza kutsanulira kwenikweni izo momwe ine ndikufunira kutero.

¹³⁵ N—ndipo Don Ruddell... Ine sindikuganiza kuti Don ali pano usikuuno, chifukwa iwo ali ndi mpingo wao wao. Koma ngati ine nditamuwona munthu aliyense amene amabwera ku kachisi uyu, atatuluka ndi kupita kwa Don Ruddell, k—kapena M’bale J.T. Parnell, kapena M’bale—aliyense wa abale awa kuno amene ali abale athu kuno ndi mzika zimzathu za Ufumu, ine ndingakhale wokondwa kwambiri ine sindikanadziwa choti

ndichite. Ine ndikanati, “Ambuye, mudzazitseni uyu mobwereza kachiwiri. Tiloleni ife tiukhuthulire kwina iwo ndi kudzazitsapo ndi winawake.” Ine ndikanazikonda izo. Ine ndikanakonda kumawawona anyamata amenewo. . . Iwo ndi anga—iwo ndi ana anga.

¹³⁶ Tsopano, J.T. k—kapena wina aliyense wa iwo sasowa kuti azikhulupirira monga momwe ine ndimachitira; iwo sasowa kuti azichita zimenezo. Monga ine ndinakuuzani inu mmawa uno, ine sindimagwirizana ngakhale ndi mkazi wanga, kapena iye samagwirizana ndi ine. Nanga bwanji ngati ine ndikanapita pa gome ndipo Junior akanakhala ndi chitumbuwa chokhala ndi apulo ndipo ine nkukhala ndi chitumbuwa chokhala ndi nthuza. M’bale, ife tonse tikudya chitumbuwa, ife tizigwirizana pa zimenezo, koma. . . Ndipo ife tonse tikulalikira Uthenga wofanana. Khalidwe la mpingo wake. . .

¹³⁷ Inu mukudziwa, Petro ndi Paulo anali nazo zosiyana, osati mu ziphunzitso zawo, koma momwe Petro ankachitira khalidwe lake. Iwo anali ndi—kusiyana pang’ono mu zimenezo, koma izo sizinawalekanitse konse iwo. Iwo anali abale. Bwanji, zedi ife tizikhala nako kusiyana, osati zosiyana. . . Ine sindimagwirizana ndi a Assemblies of God. Ine sindimagwirizana ndi kachitidwe kawo, koma pali anthu a Assembly of God ambiri amene ali abale ofunikira. Ine sindimagwirizana ndi chiphunzitso cha aumodzi, koma alipo ochuluka a anthu amenewo omwe ali anthu ofunikira.

¹³⁸ Ine ndimagwirizana—sindimagwirizana ndi Abaptisti, ndi Achipresbateria ndi kachitidwe kawo, koma mkati mmenemo, muli Akhristu owona.

¹³⁹ Mwanjira ina kapena imzake madzulo ano ine ndinatenga telegalamu. Ine ndinaiphonya iyo. M’bale, mlaliki wa Chibaptisti, anati iye w—wakhala akufunafuna kwa nthawi yaitali kuti afike pamalo—kapena afike pa malo pamene anthu azilemekeza Mulungu mmenemo mmalo molemekezana wina ndi mzake.

¹⁴⁰ Ndipo m’bale wofunikira amabwera ku mpingo uno anati, “Ine ndikutengerani inu ku malo oterowo.” Iye amakhumba kuti abwere kuno, wa Chibaptisti. Inu mukuona, iwo amwazikana konsekonse. Ine sindikanati ndigwirizane ndi kachitidwe kawo, koma ine ndithudi ndimalikonda gululo. Koteri musamanene zimenezo pokhudza abale.

¹⁴¹ Tsopano mkati muno, mphatso izi ziri—ziyenera kumayang’aniridwa. Palibe mphatso. . . Muiyenera kumaiyang’ana iyo. Satana akhoza kusanzira mphatso iliyonse. Tayang’anani pa Mabitoloji awa tsopano akuti azisanzira machiritso Auzimu—onyansa, auve, ovunda, obadwa kuchokera ku gehena. Mukuona? Chabwino.

293. Kodi Daniele anali munthu wachinai mu ng'anjo ya moto chifukwa iye anali mneneri mu m'badwo umenewo?

¹⁴² Ayi, uyo anali Yesu. Munthu wachinai anali—wonga Mwana wa Mulungu. Ine sindikuganiza kuti iye anali mneneri, chifukwa iye anali mu khola la mikango; koma i—ine sindikanakhulupirira kuti Daniele anali mu ng'anjo ya moto. I—ine sindingathe nkomwe... Tsopano, apo inu mukhoza kukhala mukulondola, komano ili ndi lingaliro langa chabe.

294. M'bale Branham, mu Genesis 6 ndi ndime ya 12, Mulungu ananena kuti mnofu wonse unali utayipitsa njira yake. Kodi izi ziri ndi polozera ku chilekano ndi chikwati? Ngati ziri choncho, kodi Yesu sanali ndi kulozera kwa chinthu chomwecho pamene Iye ananena kuti, "Momwe izo zinaliri mu masiku a Nowa, chomwechonso izo zidzakhala ziri pamene Mwana wa munthu adzakhala ali kuululidwa" mu Mateyu 24, ndime ya 38 ndi 39?

295. M'bale Branham, kodi padzakhala pali ana aliwonse obadwa nthawi ya Zakachikwi—zaka chikwi—Zakachikwi, ulamuliro wa zaka chikwi wa Khristu kuno pa dziko lapansi? Kapena kodi padzakhala pali chizindikiro chirichonse pa dziko lapansi—tchimo lililonse (ndikhululukireni ine) pa dziko lapansi mu nthawi imeneyo; ndipo kodi padzakhala pali anthu pa dziko lapansi mu matupi ogwirika mu nthawi imeneyo?

¹⁴³ Ine ndiyesera kuti ndingothamanga kudutsa mwa iwo mofulumira ndithu. Tsopano, mu Genesis mutu wa 6, ndime ya 12, Mulungu anati mnofu wonse unali utayipitsidwa... Eya, chimenecho chinali chikwati, chilekano, ndi chinthu china chirichonse. Baibulo linati, "Momwe izo zinaliri mu masiku a Nowa, momwe iwo anali kukwatirira, ndi kuperekedwa mu chikwati," ndi zina zotero monga choncho. Chimenecho ndi chimodzi cha zizindikiro cha nthawi yotsiriza, chimodzi chabe cha zizindikirozo.

¹⁴⁴ Tsopano, ngati izo ziri zonse zomwe dziko linali kuchita, ine sindingathe kuzitcha izo umboni wa nthawi yotsiriza, monganso momwe ine sindingatchere kuyankhula mu malirime umboni wa Mzimu Woyera. Izo ndi zoonza kuti pakuyenera kubwera nthawi pamene chikwati ndi chilekano zidzangokhala monga momwe zinaliri mu masiku a Nowa, koma pali zinthu zina zambiri zimene zikupita limodzi ndi zimenezo; ichi ndi chimodzi chokha cha zizindikirozo.

¹⁴⁵ Ndipo kuyankhula mu malirime ndi chimodzi cha zizindikiro za Mzimu Woyera, koma osati chizindikiro chosalephera cha Mzimu Woyera, mosachulukanso kuposa basi momwe akazi ndi amuna akukwatirira ndi kulekana ndi kukwatirananso. Icho sichingakhale chiri chizindikiro chokha. Ngati icho chikanakhala chimodzi chokha chimene chinalipo,

ine sindikanati ndichitche icho zimenezo. Mukuona? Zinthu zina ziyenera kupitapo ndi kuyankhula mu malirime kapena mphatso ina iliyonse kuti zipange izo kukhala Mulungu.

¹⁴⁶ Tsopano, “Kodi ana azidzabadwa mu ulamuliro wa Zakachikwi wa zaka chikwi?” Ilo ndi funso lomwe liri mu malingaliro anga, limene ine ndinakuuzani inu tsiku lina. Ine sindikudziwa. Izo zikuwoneka mochulukwa kwambiri ngati izo zikanakhoza kukhala ziri; izo zikuwoneka mochulukwa kwambiri ngati kuti izo sizikanakhala ziri. Ine ndikhala woonamtima ndi inu momwe ine ndikudziwira kukhala kwake. Ine sindikudziwa mpaka nthawi ino. Ngati Mulungu ati adzaziulule konse izo, ine ndidzakuuzani inu. Koma dikirani; izo zidzayenera kubwera kuchokera kwa Mulungu. Inu ndinu ana anga. Ine sindikanakuuzani inu. Ine sindikudziwa kaya uko kudzakhala kuli kapena uko sikudzakhala kuli. Ine sindingathe kunena.

¹⁴⁷ “Kapena kodi padzakhala pali tchimo pa dziko lapansi mu nthawi imeneyo?” Ayi! Sipadzakhala pali tchimo pa dziko lapansi. Satana wamangidwa.

¹⁴⁸ “Ndipo kodi padzakhala pali anthu pa dziko lapansi mu matupi ogwirika mu nthawi imeneyo?” Inde, bwana! Ife tidzakhala nawo matupi athu aulemerero komwe kuno pa dziko lapansi, kumadya, kumamwa, kumanga manyumba, n—n—ndi kumakhala moyo monga momwe ife tikuchitira mu tsopano kwa zaka chikwi. Ndi—nthawiyaokha ya Mkwatibwi ndi Mkwati.

296. M'bale Branham, kodi Yesu ankatanthauza chiani mu Mateyu 12, ndime 32, pamene Yesu anati, “Aliyense amene ayankhula mawu motsutsa Mzimu Woyera, izo sikudzakhululukidwa kwa iye, ngakhale mu dziko lino, ngakhale mu dziko liri nkudzalo”? Chonde talongosolani ndime izi za Lemba kwa ine. Zikomo inu. Ndipo liri ndi dzina la bamboyo; iye ndi mtumiki. Chabwino.

¹⁴⁹ M'bale, ndine—inu ndi wafioloje, ine sindiri. Koma ine ndikufuna ndinene ichi, kuti Yesu anati, “Aliyense amene ayankhula motsutsa Mzimu Woyera izo sizidzakhululukidwa kwa iye.” Mwa kuyankhula kwina, kuti ndiziike izo ndi Lemba lina lonse, “Mtundu uliwonse wa tchimo udzakhululukidwa kwa munthu, koma kuchitira mwano Mzimu Woyera sizidzakhululukidwa kwa anthu.” Kuchitira mwano Mzimu Woyera ndi kuwuseleula iwo, kuwunena iwo, kuwunyogodola, kuchita chinachake chonga izo ndi pamene iwe umawoloka mzere wa pakati pa cholondola ndi cholakwika.

¹⁵⁰ Tsopano, ngati inu muwuwona Mzimu Woyera...Mwa chitsanzo, bwani ngati Mzimu Woyera ukanabwera panso pano ndi kumazindikira za mumtima monga Iwo umachitira, ndipo nanga bwani ngati umenewo ukanakhala uli Mzimu Woyera, ndipo inu mukanati musakhulupirire kuti Iwo unali, ndipo inu mukanatuluka ndipo inu nkumakauseka Iwo ndi

kumakaunena Iwo; ine sindikusamala chimene inu mukanachita konse, inu mwathedwa. Ndipo inu simungathe kuchita zimenezo. Izo zimatsimikizira apo pomwe kuti inu sindinu wa Mulungu, chifukwa Mbewu ya Mulungu imakhalabe ili mwa munthu ndipo iye sangathe kuchimwa. Ndipo kodi tchimo ndi chiani? Kusakhulupirira. Pamene iye awaona Mawu akuwonetseredwa, iye aziwakhulupirira Iwo. Ndipo iye angakhoze kokha . . .

¹⁵¹ Onani, pali tchimo limodzi lokha, tchimo limodzi lokha. Ndi angati akudziwa zimenezo? Kumeneko ndiko kusakhulupirira. Ndiko kulondola. Kuchita chigololo si tchimo. Kusuta ndudu, kunena mabodza, kulumbira, zimenezo si tchimo. Zimenezo ndi zotsatira za kusakhulupirira. Inu mumachita zimenezo, chifukwa inu sindinu wokhulupirira. Uko nkulondola. Kotero, mukuona, pali tchimo limodzi lokha, ndipo limenelo ndilo kusakhulupirira. “Iye amene sakhulupirira waweruzidwa kale.” Ziribe kanthu zimene angamachite kapena kalikonse, iye waweruzidwa pa kuyamba pomwe. Chabwino.

297. M'bale Branham, kodi ndi zolakwika kuti aang'ono osakwatiwa—osakwatiwa (sananene kuti chiani) kuti azidula tsi—tsitsi lawo? Ine ndikulingalira kuti ndi mkazi.

¹⁵² Inde! Inde, n—ndi zolakwika kuti mkazi aliyense adule tsitsi lake.

Limenelo ndi funso lalifupi chabe. Kodi i—kodi inu mukuyamba kugona? Chabwino, i—ife tithamanga mofulumira basi monga momwe ife tingathere. Ine ndimayesera kuti nditenge mbewu ya serpenti ija moyipa kwambiri.

Mumupempherere mwana wathu wamwamuna mu . . .

Limenelo ndi pempho la pemphero. Ine ndinangozitola izi apo ndi kuthamanga nazo, basi . . .

298. M'bale Branham, kodi akazi amalolezedwa kuti azigwira ntchito mu malo amchigulu pamene iwo ali ndi mwamuna wathanzi ndi ana? Ine ndikufunsira funso ili kwa winawakenso.

¹⁵³ Chabwino, i—i—i—ine sindikudziwa za zimenezo. Ine sindinganene. Koma i—ine ndangokhala ndi kumverera uku. Ndiroleni ine ndinene izi: Ine ndikukhulupirira, ngati ine ndikadakhala ndiri—mkazi ndipo ine nkumadziwa kuti mwamuna wanga ndi wathanzi ndipo anali ndi ntchito yabwino, akugwira ntchito, ine ndikukhulupirira izo zikanakhala—chosangalatsa chachikulu kwa ine kuti ndizikhala pakhomo, kumasamalira ana anga ndi kumapanga . . . n—n—ndi kumasamalira ana anga ndi kumawalera iwo, ndi kumawakonda Ambuye. Ndipo ngati ine ndikanakhala nayo nthawi iliyonse nditatha zochapa zanga ndi zinthu zimene ine ndimati ndichite, ine ndikuganiza ndikanati ndiziwaphunzitsa ana anga momwe angamawatumikire Ambuye.

154 Tsopano, ngati inu muli ndi—ngongole kapena chinachake chimene inu mukuyesera kuti muwathandizire amuna anu kulipirira, kapena chinachake chimene inu mukuyenera kuti muzichita chimene. . . Chabwino, ine ndikuganiza zimenezo ndi zabwino ngati inu mukuyesera kuti muzimuthandizira iye. N—ndipo inu muzikhala dona. Ndipo i—ine ndikuganiza ndi zovuta. Palibe mwamuna amene ali ndi kumvetsa kwabwino amene amafuna mkazi wake kuti akakhale mu gulu, kumene kuli gulu lazolawula, amuna auye ndi zinthu monga zimenezo. Koma ngati mkazi akuyenera kuti alowe mu zimenezo, ine ndikuganiza kuti iye ayenera kuti—mwamuna wakeyo ayenera kudziwa kuti mkaziyo ndi Mkristu weniweni amene akhoza kudaliridwa, mkazi wodalirika.

155 Koma tsopano, monga kungonena kuti iye asamagwire ntchito, i—ine sindikudziwa. Mukuona, palibe Lemba loti liyikire kumbuyo izo. Ine basi—ine ndikungoperekapo lingaliro limenelo. Koma ine ndikuganiza ngati mkazi akufuna kuti azigwira ntchito ndipo iye akufuna kuti azigwira ntchito. . .

156 Tsopano, ine ndithudi ndimatsutsana nazo kuti akazi azigwira ntchito mu maofesi awa kumene amuna onse amalonda awa. . . Iwo amakhala akupitiriza nazo, kumanena nthabwala zauve izo. Ndipo mkazi wabwino, waukhondo atakhala pamenepo, ndi zinthu zonse zonyansa zakuda izo zikuyankhulidwa monga choncho, i—ine ndimatsutsana nazo zimenezo. Ine ndikuganiza inu mumayenera kuti muchoke pakati pa zinthu zonga zimenezo.

157 Koma tsopano, ngati mkazi angathe kudzigwira yekha ng—ngati dona weniweni ndipo akuyesera kuti azimuthandizira mwamuna wake kuti achite chinachake apeze—zovala zina za ana kuti azipita ku sukulu, k—kapena kulipira ngongole ithe, kapena chinachake chonga izo, ndipo iye akafuna kuti agwire ntchito mpaka zimenezo zitatha. . . Tsopano, izi si Ambuye, chifukwa ine ndiribe Lemba la izi. Ine ndikungonena kuti awo akhoza kukhala malingaliro anga; koma ngati mwinamwake, ine sindikanaganiza kuti basi chifukwa chakuti iye akufuna kuti azigwira ntchito kuti azingoyendayenda ndi kumakhala—kapena—ndi ndalama zochulukirapo zoti azizimwaza, azithamangathamanga, ndi kuthamangira kogulitsa mowa, kapena kumamwa, kumasuta, ndi kumapitiriza nazo; ine sindikuganiza kuti iye akuyenera kuti azichita zimenezo. Ine ndikuganiza kuti iye akuyenera azikhala pakhomo, ndi kuyesera kuti akhale dona, ndi kumasamalira pa nyumba pake.

299. Ngati Yesu mu chachiwiri. . . (Ayi!) Ngati Yesu—ngati iwe uli mu chikwati chachiwiri chomwe mbali zonsezo analekanapo. . . a—i (k-u-l-a-p- . . .) kulapa. . . kodi kulapa ndi kokwanira, kapena kodi iwe umasowa

kuthetsa—kapena kodi iwe umasowa kuti uthetse chiyanjano cha chikwati chakocho kuti zikhale moyenera?

“Ng—ngati iwe uli mu chikwati chachiwiri chimene mbali zonse analekana...” Ine ndikuganiza ine ndayankha kale zimenezo. Mukuona? Inde, ndayankha kale zimenezo. Pamene mbali zonse z—ziri...ine basi...

¹⁵⁸ I—ine ndikukhumba ife tikanati tisasowe kumadutsa mu zinthu izi, anthunu. Ine ndiri ndi abwenzi akhala pomwe pano, uko mwa omvetsera awa pano amene ine ndikuwadziwa...Izo zikukhala pafupi ngati zindiphe ine kuti ndizinena izo, koma i—ine ndiyenera kuti ndizinena zimenezo. Mukuona? Ndipo dziko liri mu chikhalidwe chachivundi choterochi.

¹⁵⁹ Mkazi wina wosauka, wamng’ono, wachikulire amalakwitsa ndi kukwaturana ndi chidakhwa chinachake n—ndipo iwo amatembenekira mu njira imeneyo, kapena mwamuna wina wosauka atakwatira wina woyenda mu msewu ndipo asakudziwa izo, ndiyeno nkukhala womangika kwa mkazi ameneyo kapena mwamunayo utali wonse pamene iwo ali moyo. Chimenecho ndi chinthu choipa. Chikwati ndi chinthu chopatulika.

Nthawi zambiri ana ochimwa amathamangira umo ndi kumachita zinthu zimenezo, ndiyeno iwo amadabwa kuti zonsezi ndi za chiani. I—ziri...ine ndikukhulupirira, ngati Ambuye adzandiloleza ine kuti ndidzafotokoze chikwati ndi chilekano ichi momwe izo ziyenera kumakhalira, ine ndikukhulupirira zidzapangitsa kumveka mwamphumphu konse kwa izo. Zonse ziri...[Kutha kwa mbali yoyamba ya tepi; mbali yachiwiri ikuyambika ndi funso losakwanira—Mkonzi.]

300. Ife tikuona...Chifukwa chiyani ife sitikutha kugulitsa nyumba yathu? Zikomo inu. Ife...P.S. Ife tapemphera ndi kusala—ndi—kuti tiigulitse iyo, komabe popanda zotsatira.

¹⁶⁰ Chabwino tsopano, M’bale kapena Mlongo (iwo sanalembepo dzina lawo), koma aliyense yemwe ali, tsopano, ngati inu mukuyesera kuti mugulitse malo anu ndipo inu mwachita zomwe inu...Inu mukufuna kuti muigulitse iyo ndipo mwinamwake kuti mukagule inanso kapena chirichonse chimene inu mukufuna kuti muchite, ine sindikudziwa. Ngati cholinga chanu chiri chabwino, inu mukuyesera kuti mugule nyumba...Ngati inu muli ndi ana kapena chinachake monga choncho, inu mukufuna kuti muwapezere iwo nyumba yabwinoko kapena chinachake...Ine sindikudziwa kuti zonsezo ndi za chiani, koma ine ndinganene ichi: Ngati inu mukuyesera kuti muigulitse iyo, ndi kumasala ndi kuyesera kuti muigulitse iyo, ndiye zilekereni izo kwa Ambuye ndi kuiwala za izo. Mukuona? Chifukwa izo zikhoza kukhala kuti Mulungu...

Inu mukhoza kusamukira kwinakwakenso, ndipo izo zikhoza kusakhala zolondola. Mukuona?

¹⁶¹ Ngati inu muli Mkhristu ndipo mukudalira mwa Ambuye, chifukwa inu zedi inu muli kapena inu simukanati muzisala ndi kumapemphera. Mukuona? Koteru ine ndikanangozipereka izo kwa Ambuye. Kuti, “Tsopano, Ambuye, pamene ili nthawi Yanu yoti ife tiigulitse iyo, Inu mumutumiza wogula.” Ndiye apo izo zaperekedwa kwa Ambuye, chotsanipo manja anu pa izo ndi kumapita patsogolo. Ine ndikukhulupirira kuti izo zigwira ntchito. Ine ndikukhala ngati ndikuchita mwaliwiro apa, chifukwa ine nthawi ikunditheru.

301. M’bale Branham, kodi ndi zolakwika kuti mkazi azipiringa tsitsi lake?

¹⁶² Ine ndadutsa kale mu zimenezo. Zedi, ine sindikusamala, zingolisungani ilo liri lilatali. Mukuona? Ine sindi...ine ndikudziwa inu...Ine sindikutanthauza izo kuti ndikhale “wanthabwala” ndi inu asungwana. Mukuona? Zimenezo ndi moonamtima. I—i—inu mukufuna kuti mudziwe, ndipo inu mukundifunsa ine. Inu muli nacho chidaliro mwa ine kapena ine simukanati mundifunse ine zimenezo. Tsopano, ine ndiri ndi chidaliro mwa inu, Mlongo, kuti zimene ine nditi ndikuuzeni inu, ine ndikukhulupirira kuti inu mukazichita.

¹⁶³ Ine sindingathe kuziikira izo kumbuyo ndi Lemba. Ngati inu mukufuna...Ngati inu mulibe tsitsi lokongola, lopiringizika ndipo inu ndinu mkazi, inu mukufuna kuti muziwoneka wokongola kwa mwamuna wanu, kwa bwenzi wanu wamwamuna, kapena chinachake monga choncho, i—ine sindingathe kukuuzani inu za kupiringa tsitsi lanu k—kapena kodi iwo anazitcha chiyani izo, kulilocha ilo kapena chinachake? I—ine ndiribe kanthu konena pa zimenezo; zimenezo ziri kwa inu. Inu mukuona? I—ine...Inu basi, pakati pa...Inu mungowapempha Ambuye choti muzichita, I—Iye akuuzani inu zimenezo, chifukwa i—ine ndikuyesera kuti ndizifotokoza zinthu mwa Lemba. Mukuona?

302. Chonde tafotokozani l Akorinto 13:8-12. Tsopano pakuti Mawu angwiro abwezeretsedwa kwa Mpingo k—kodi ndime izi zakwaniritsidwa?

¹⁶⁴ Tsopano, ine ndikuganiza ine ndangodutsa kumene mu zimenezo, sichoncho ine? “Ndipo pamene icho chimene chiri changwiro chabwera, icho chimene chiri cha mderamdera chithetsedwe apo.” Paulo anati, “Ngakhale ine ndingamayankhule ndi malirime a anthu ndi angelo, ndipo ine nkumachita zinthu zonse izi apa...Koma pamene icho chimene chiri changwiro chibwera...” Tsopano, kodi pali chirichonse changwiro kupatula Mulungu? Ayi, bwana! Kodi Mulungu ndi wangwiro? *Pachiyambi panali* [Osonkhana akuyankha, “Mawu.”—Mkonzi.] *ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo*

Mawu anali Mulungu. Mawu akadali Mulungu. Mukuona? Chabwino. Pamene icho chimene chiri changwiro chibwera, icho chimene chiri chamderamdera chithetsedwa apo.

303. M'bale Branham, kodi ndi zolakwika kumeta tsitsi mwa mphwamphwa pamwamba?

¹⁶⁵ Ine ndikuli—ine ndikulingalira uyu ndi mwamuna; i—ine ndikuyembekeza iye ali. Chabwino, tsopano, akazi ena amachita zimenezo. Zedi. Ine ndinali kupita pa basi nthawi ina pamene ine ndinali wolondolera zinyama wa boma kuno. Ndikupita uko. . . Ine ndinali nditakhala pamenepo, ndipo munthuyo anali akuyankhula monga choncho, anali atavala chisoti cha wowotcherera, ndipo ine ndinali ndikungoyankhula kwa iyeyo. Ndipo iye anali akupitirira nazo kusuta ndudu, anali ndi magalasi a wowotcherera atawakankhira mmwamba monga choncho. Kunali kumtunda uko chaku Sellersburg. Ndipo ine ndinali nditakhala pamenepo ndikuyankhula kwa munthu ameneyo. Iye ananena chinachake pamenepo, ndipo ife tonse tinayamba kuseka; ine ndinamumenya iye pa mwendo; ine ndinati, “Mnyamata, i—izo ndi zotenga kwenikweni mkatewo, sichoncho izo?”

Ndipo ine ndinali nditakhala pamenepo monga choncho, ndipo—molunjika wina—mkazi anakhala moyang'anizana ndi pamenepo anati, “Ndikuti, Ruth, kodi iwe ukupita ku. . .?”

¹⁶⁶ Anali atavala maovololo, wamkulu wonenepa, wojintcha basi ngati mwamuna, atakhala pamenepo akusuta ndudu ndi kumaipemerera iyo mmphuno mwake, ine ndinkaganiza iye anali mwamuna. Chinachake cha kugwetsa tochi ya gasi ndi kuchita chinachake, kumenya pa mutu wa winawake ndi kumukhoma chomwe *inu-mmachitcha-icho*, ndipo anayamba kuseka. Inenso ndinaseka ndipo ndinamumenya iye pa mwendo pomwe, ndikuganiza kuti iye anali mwamuna. Ine sindinkadziwa kusi yana kwake. Iwe sungati uwasiyanitse iwo. Ndipo Baibulo linati, “Mkazi aliyense amene avala chovala choyenera mwamuna, ndi themberero.” Ndi zimenezotu.

¹⁶⁷ Ayi, M'bale, ngati inu mukufuna muzimeta mwa mphwamphwa pamwamba pa tsitsi lanu, ine ndikuzani inu; Inu mungodikirira mpaka inu mutadzafika usinkhu wanga, inu mudzakhala nalo ilo. Kotero. . . Izo nzabwino bwino. Ine sindimatanthauza izo monga choncho, bwanawe. Adalitse mtima wako ngati iwe ukukhulupirira kuti M'bale Branham akukuuza iwe choonadi. Ine sindikuganiza kuti Mulungu amanena chirichonse za amuna, chake—chophimba chake ndi bola ngati iye amalidula tsitsi lakelo. Ngati iye alisiya tsitsi lake lizikula motalika ngati mkazi, Baibulo limati ndi chamanyazi kuti mwamuna azichita zimenezo.

¹⁶⁸ Koma tsopano, ngati inu—bola ngati inu muli nalo tsitsi lanu ndipo ndinu mnyamata wamng'ono. . . Ndipo ine ndikudziwa

ine ndanena zochulukana zonse za izo: “Ndi inu, Marike, okhala ndi kumeta tsitsi kwa mphwamphwa pamwamba apo,” ndi zonse monga choncho, ndi zinthu monga izo, koma i—ine ndimangonena zimenezo. Mukuona?

¹⁶⁹ Ine si—ine sindikuganiza kuti Mulungu amasamala momwe mwamuna amalidulira tsitsi lake, bola ngati iye amadula ilo, chifukwa mutu wake ndi Mulungu. Koma mutu wa mkazi ndi mwamuna; chotero, iye ayenera... Ndipo ngati alidula tsitsi lake, iye amanyozetsa mutu wake. Ndiye mkazi wopanda ulemu ayenera azisudzulidwa ndi kuchotsedwa apo. Nkulondola uko? Koteru ngati mkazi adula tsitsi lake, iye ali—mwamuna wake ali nawo mwamtheradi ufulu wa Baibulo kuti amusiye iye chifukwa chokhala molakwika—munthu wopanda ulemu. Ndi angati akudziwa kuti izo ndi Choonadi? Ndi zimene Baibulo linanena, pakuti iye akunyozetsa mutu wake. Palibe mkazi wopanda ulemu amene akuyenera kumakhala naye.

304. M'bale Branham, pamene Yesaya ankayankhula kwa ana aakazi a Zioni (kapena ankayankhula kwa, ine ndimatanthauza, ine ndikulingalira iwo amatanthauza “ankayankhula za”)—ana aakazi a Zioni za mapini opotera, kupiringiza tsitsi, ndipo mmalo mwa tsitsi loikidwa bwino bwino, dazi; mmalo mwa... Kodi zimenezo zingakhale za lero kapena kodi Baibulo lakalelo liribe chochita monga ena amanenera?

¹⁷⁰ Baibulo lakale nthawizonse liri ndi chochita, ndipo mawu aliwonse amene Mulungu amawanena amakhala ndi chochita. Inde, bwana! Chinthu chokha chimene iwo amachita kuchokera ku Baibulo latsopano kupita ku Baibulo lakale, ilo limangozikulitsa. Yesu anati, “Inu munamva iwo akuti, ‘Iwe usati uzichita chigololo’ (iwe unkayenera kukhala uli mu kuchitako); koma Ine ndikuti kwa inu, aliyense amene ayang’ana pa mkazi nasilira pa iye wachita chigololo ndi iye kale mu mtima mwake.” Zinthu zake zofunikira zomwe izi ziri!

Tsopano, ine ndiyenera kuti nditseke, abwenzi. Izi zikufika mochedwerapo pang’ono kwambiri. Tsopano, ilo ndi lalitali kwambiri. Tiye ni tiwone ngati ine ndingapeze chinachakenso apa. Tiye ni tiwone.

305. M'bale Branham, kodi akazi (o, mai!) azivala chotani tsitsi lawo?

¹⁷¹ Kachiwiri, basi mulimonse momwe inu mukufuna kumachitira. I Timoteo 2:9. Mukuona? “Aloleni akazi azidzikometsera okha ndi zovala zaulemu.” **Ine ndikufuna kuti—ine ndikufuna kuti ndizivala langa mokondweretsa kwa Mulungu.** (Mulungu akudalitseni inu, Mlongo wokondedwa.) **Zikomo inu. Mulungu atakudalitsani inu. Zitipempherani ife.** Ndipo munthuyo walembapo dzina lake.

¹⁷² Sharon, zedi, Mlongo! Mulungu akudalitse iwe. Zilivala ilo bola ngati liri lalitali, Mlongo. Ndi msungwana wamng’ono. Mulungu akudalitse iwe, Wokonedwa. Ziri bwino. Iwe zipitirira nazo kumene.

306. Mkwatibwi akadzakwatulidwa kodi aliyense wa anamwali opusa adzapulumutsidwa kapena kodi iwo onse adzataika?

¹⁷³ Ayi! Mukuona, chirichonse chidzatsirizidwa kwa mpingo wa Amitundu pamene Mkwatibwi adzatengedwa kuchokera pa dziko lapansi. Mzimu wa Mulungu ukulisiya pa dziko lapansi: “Iye amene ali woipa akhale ali chiipirebe; iye amene wolungama akhale ali chirungamirebe; iye amene ali woyera akhale ali chiyererebe.” Mwa kuyankhula kwina malo opatulikawo akusandulika autsi, kumene—Woimira mlandu amaima akuchondelera mlandu. Khristu akuchoka pa malo opatulikawo; tsiku Lake la kukhalira pakati latha. Mkwatulo ukubwerapo; Iye akuchoka pa malo opatulikawo, akupita apo ndipo akutenga Bukhu la Chiwombolo, ndipo akudzitengera onse amene Iye anawaombola. Palibe aponso ntchito yokhalira pakati. Ndi angati akumvetsa zimenezo? Ine ndiri nazo izo pa chimodzi cha Zisindikizo—kapena pa chimodzi cha... Eya, Zisindikizo, ine ndikukhulupirira zinali, kuti Khristu akubwerapo kuti adzatenge za ntchito Yake yokhalira pakati.

¹⁷⁴ Tsopano, miniti yokha. “Kodi anamwali opusa adzakhala akupulumutsidwa?” Ayi! Chirichonse chimene chingamchitikire iye—chikuchitika tsopano. Ikadzatha nthawi imenoyo iye ali mu chikhalidwe... Tsopano, iye adzayenera kuti adzadutse mu nthawi ya chisautso. Ndipo chifukwa chake chiri, chifukwa kuti iye wakana Chitetezero mwa chidzalo Chake. Iye ndi wokhulupirira, wokhulupirira modzinenera, koma iye adzayenera kuti adzadutse nthawi ya chisautso. Baibulo linati, “Ndipo ena onse a iwo, chinjoka chinalavula madzi kuchokera mkamwa mwake kuti chipite ndi kukapanga nkondo...” Ndipo ora lake limene ilo liri. A . . .

¹⁷⁵ Sipanayambe pakhala nthawi mu mbiriyakale pamene mipingo ya mwadzina inakhalapo yanjala kwambiri kuti ipeze ubatizo wa Mzimu Woyera. I—ine ndimawayankhulira Amuna Achikhristu Amalonda. Mowirikiza, ndi Achipresabateria, ndi Achilutera, Akatolika, ndi onse, Achibaptisti mwa mazana, Mpingo wa Khristu, Anazarene, a Pilgrim Holiness, Seventh Day Adventist, aliyense wa iwo akukhamukira umo kuyesera kuti apeze... Mukuona?

¹⁷⁶ Tsopano, ichi ndi chinthu chokhudza. Chonde musachitenge icho ngati chiphunzitso, koma kodi inu mukumvetsa zomwe Malemba anati zikanati zidzachitike pamene icho chikanachitika? Nthawi ikanakhala itatha. Pakuti taonani, apo panali anamwali asanu ndi awiri—kapena anamwali khumi anapita kunja kuti akakomane naye Mkwati, ndipo theka la iwo

anali ndi mafuta mu nyali zawo, theka la iwo analibe. Ndilo gawo la Thupi limene liri lakufa ndi gawo limene liri lamoyo. Asanu ochenjera, pamene iwo—kufuula kukubwera, “Taonani Mkwati. . .” iwo onse akukonza—akudzuka ndi kukonza nyali zawo kuti azipita ku mgonero wa chikwati. Koma pamene namwali wopusa anati, “Tipatseniko ife ena a mafuta anu, nyali zathu zazima. (Mukuona?) Tipatseniko ife a mafuta anu.” Iwo anati, “Sichoncho, ife tangokhala nao otikwanira ifeeni. Pitani mukagule iwo.” Ndipo pamene iwo anapita kuti akawagule iwo, Mkwati anabwera.

177 Pamene kulengeza kunapita uko, kutsimikizira, “Mkwati akudza,” aliyense ankafuna kuti akhale bwino, mwamsanga ndithu. Kodi ora lake si limenelo pamene cholembedwa chiri pakhoma?

178 “O, ife tikufuna ubatizo wa Mzimu Woyera.” “Ife tikufuna *ichi, icho* kapena *chinacho!*” Koma pamene iwo anapita kuti akawagule Iwo, Mkwati anabwera. Ochenjera anapita mkati, ndipo iwo anasiyidwa kunjira kumene kudzakhala kuli kulira, kubuma, ndi kukukuta kwa mano.

179 Ine ndiri ndi mafunso okongola basi apa oti apite ndi zimenezo: “Anali ndani mwamuna uja amene anavala mwinjiro amene analowa umo, amene sanavale chovala chaukwati?” Ndi mafunso onse awo amene akumangiriza kumene mu zimenezo.

307. Kodi munthu azipereka chakhumi kwa munthu wina, kapena kodi Mkhristu azigwira ntchito?

180 Zedi iye azitero. Iye ndi munthu mmodzi amene amalolera kugwira ntchito, ndiye Mkhristu.

181 “Kupereka zakhumi kwa munthu wina?” Izo zikutengera yemwe munthu wina wakeyo ali. Mukuona? Ndi kulondola uko. Mu Ahebrei 7, nthawi yoyamba imene kupereka chakhumi kumanenedwa m—mu kuima kumene ife. . . Dikirani miniti, ine ndikukhulupirira, funso lachiwiri. Ayi! A, nha. Ayi! La M’bale. . . Anati, “**Mafunso awiri a M’bale Branham.**”

182 Pamene. . . Mu Ahebrei mutu wa 7, pamene Abrahamu, ankachokera kokapha mafumu, anakomana ndi Melkizedeki, iye anamupatsa Iye chakhumi. Ameneyo anali Melkizedeki, Mfumu ya Salemu, amene ali Mfumu ya Mtendere, ndi Mfumu ya Chirungamo, amene sanali winawake koma Mulungu Mwiniwake. Mukuona?

183 Koma pamene inu mumapereka zakhumi. . . Kwenikweni, kumene inu muli ndi ngongole ya zakhumi ndi kumene inu mumapeza chakudya chanu. “Bweretsani inu zakhumi zanu zonse ku nyumba Yanga yosungira, atero Ambuye. (Nkulondola uko?) Ndipo ndiyeseni Ine nazo atero Mulungu, ngati Ine sindingati nditsegule mazenera Akumwamba ndi kutsanulira apo dalitso limene inu simudzakhala nalo malo okwanira kuti

zotsatira, zotsatira, zotsatira, zotsatira, zotsatira za mwanayo sizikanati zidzalowe ngakhale mwa osonkhana a Mulungu. Ndiko kulondola.

¹⁸⁸ Koma inu mukuona, kunalibe kanthu kamphamvu mokwanira kumeneko koti kalikhululukire tchimo limenelo. Magazi a Chipangano Chakale sanali kukhululukira machimo; iwo ankawaphimba. Koma Magazi a Yesu Khristu amawasudzula iwo. Izo ndi zosiyana tsopano. Pamene Magazi a Yesu Khristu abwera umo, izo ndi zosiyana.

309. M'bale Branham, ife tikufuna kuti tikhale pafupi ndi Uthenga wanu momwe ife tingathere. Kodi ife tisamukire ku Arizona kapena Jeffersonville?

¹⁸⁹ Zikukomereni nokha, kwina kulikonse. Ine zedi ndimakukondani inu, ine sindikusamala kumene inu muti mupite, chomwe muti muchite. Koma tsopano, ngati langizo, ine ndikukhulupirira ine ndikanabwera ku Jeffersonville. Ngati inu muti musamuke mulimonse, ine ndikanati ndizibwera ku Jeff. Ine ndikukhulupirira ndiri kuno mochuluka kuposa ku Arizona. Zimenezo ziri bwino.

310. M'bale Branham, k—kodi tachedwa kwambiri kuti tizilalikira kwa ochimwa panonso?

¹⁹⁰ Ayi! Ayi! Musati mutengere zimenezo mu malingaliro anu, m'bale. Pitirizani kumanga nyumba. Pitirirani kuchita chirichonse chimene inu mungathe. Zingopitirirani nazo mpaka inu mudzaitanidwe kuti muchokeko. Mukuona?

311. Funso nambala 2. Kodi opulumutsidwa azidzipatula okha kwa ochimwa mu kupembedza? Kodi opulumutsidwa azidzilekanitsa kwa ochimwa kuti azipembedza?

¹⁹¹ Ine sindikudziwa ndendende zimene inu mukutanthauza ndi zimenezo. Ngati inu mukutanthauza ochimwa monga uko mu...Iwe umapembedza Mulungu paliponse. Koma ine ndikuganiza ngati ife titero, ndiye ife tikhala nawo bwanji mpingo, chifukwa ochimwa amabwera kumene mu mpingo ndi kukhala pambali pa Mkhristu. Musati nkonse muzidzipatula nokha kwa chirichonse kupatula tchimo, osati wochimwa. Zimutengani wochimwayo ngati inu mungathe, koma musakhale otenga nawo za tchimo lake.

312. Kodi mkazi wopulumutsidwa azidzikaniza yekha kwa mwamuna wake ngati iye ali wochimwa?

¹⁹² Ayi, bwana! Ayi, bwana! Ameneyo ndi mwamuna wanu. Inu mumukankhira iye kutali kwambiri ndi Mulungu kuposa kale lomwe pa kuchita zimenezo. Mukuona? Uko nkulondola, M'bale, Mlongo. Inu munamukwatiwa iye; iyeyo ndi wanu, ndipo inu ndi wake.

313. M'bale Branham, kodi tanthauzo la kulepheretsa ndi chiani? Kodi anthu amakhala afulu kuti akwatire kapena

awa angokhala mawu ena a chilekano? Ine ndikanafuna kudziwitsidwa kwina pa izi.

193 Zedi iwo ali okwatirana. Bola ngati iwo atenga lumbiriro limenelo, iwo akwatirana. Chimodzimodzi ngati mnyamata, ngati mnyamata amulonjeza msungwana kuti amukwatira iye pansu pa chikhulupiriro chabwino, iye ali wokakamizikira kwa msungwana ameneyo. Iye ali basi ngati kuti wamukwatira iye. Chinthu chokha chimene lamulo limachita, ndi kuwapatsa iwo—chikalata cha ufulu choti azikhala palimodzi kuletsa kuti azikhala mwamuna ndi mkazi mwa mwambo chabe. Koma pamene mwamuna amuza mkazi, “Ine ndidzakukwatira iwe, Wokonedwa; ine ndidzakutenga iwe kuti ukhale mkazi wanga. Kodi iwe unditenga?” iye wakwatira.

194 Lumbiriro lanu ndi lopatulika; ndi chimene chimakukwatitsani inu mulimonse. Palibe mlaliki amene angakukwatitseni inu, palibe majesitireti, kapena kanthu kena kalikonse; ndi lumbiriro lanu lomwe kwa Mulungu ndi kwa mwamuna uyu. Pamene inu mulonjeza, inu wakwatirana.

195 Tayang’anani. Inu mukuti, “M’bale Branham, kodi izo. . .? Inu mukuti. . . Inu munati inu muzingoyankha izi mwa Baibulo.” Kodi inu mukufuna Baibulo pa izo? Kwezani manja anu ngati inu mukufuna izi. Tsopano, ife tatsala ndi maminitisi sikisi kapena eyiti. Chabwino.

196 “Yosefe, mwamuna wake, pokhala mwamuna wolungama (mwamuna wake wachitomero, akumutcha kale iye mwamuna wake). . . Yosefe, mwamuna wake, pokhala mwamuna wolungama, anali ‘kulingalira’ kuti amusiye iye mwamseri pa chifukwa ichi; koma iwo asanakhale palimodzi, iye anapezedwa akuyembekezera mwana mwa Mzimu Woyera. (Mukuona?) Ndipo Mngelo wa Ambuye anawonekera kwa iye mu loto ndipo anati, ‘Yosefe, iwe mwana wa Davide, usawope ayi kudzitengera kwa iwemwini, Maria, mkazi wako.’” Wokwatira kale, iye anali atamulonjeza kale iye.

197 Ndipo cha. . . Ndipo dona wamng’ono iwe, ngati iwe ulonjeza kuti udzakwatiwa ndi mnyamata ameneyo, iwe umakhala wokakamizikira kuti uchite zimenezo. Ngati iwe ukwatirana ndi wina uli ndi chikakamizo icho, iwe u—kuyambira apa mpakana—iwe udzakhala ukukhala mu chigololo. Ndipo zindikirani, chinthu chomwecho kwa mnyamata akalonjeza kuti amukwatira mkazi. . .

198 Musati inu muzipanga lumbiriro lanu kwa wina aliyense kupatula ngati inu mukutanthauza kuti mulisunga ilo. Kumbukirani, ndi limenelo Baibulo pa izo. Yosefe analonjeza kuti amukwatira Maria. Ndipo Mulungu ananena kuti izo zinali. . .

199 Werengani malamulo a Chipangano Chakale pa zimenezo. Mukuona? Lamulo la Chipangano Chakale,

ngati iwe umulonjeza kuti umukwatira mkazi, ndipo iwe nkukamukwatira wina, iwe unali kuchita chigololo; ndipo izo zinkakuponjera iwe kunja kwa msasa. Inde, bwana! Iwe umayenera kuti uzisunga malumbiro ako pamene iwe umulonjeza mkazi zimenezo. Iye ndi chida chaching'ono chopatulika, ndipo icho nchoti chizibweretsa moyo wa mwana mu dziko kachiwiri. Kotero pamene iwe umulonjeza iye, iwe uyenera kuti uzimukwatira iye.

314. Kodi ziri mochedwa kwambiri kumachita mautumiki aku ndende ndi ntchito zotero monga za umboni poyesera kuti tipulumutse miyoyo? Ndiponso kodi wina azigulitsa zonse zomwe iwo ali nazo tspano, Ambuye akubwera posachedwa kwambiri?

²⁰⁰ Chabwino, bwanji—inu mwatani... Ine ndikuyembekeza kuti ine sindinanene kanthu kalikonse kamene kangamakupangitseni inu kuti muzikhulupirira zonga zoterozo. Ndatero ine? Ngati ine ndatero, ndikhulukireni ine! Ine sindikutanthauza... Mukuona? Musati muzingopeka zinthu zimenezo. Pitirirani nazobe, kumalalikirira, kumakhala ndi utumiki wa kundende, kutengera aliyense, ndipo musati... .

²⁰¹ Penyani kuno. A Seventh Day Adventists kuno si kale litali, pafupi zaka fifite kapena sisikite zapitazo, ine ndinaziwona izo mu pepala ya *Courier-Journal* (ine ndiri nayo iyo penapake kumbuyo kwa galimoto), chidutswa chachikulu cha pepala ya *Courier-Journal*, kumene iwo anasomeka mapiko akalewo, kumene pamene iwo ankatchedwa achi Millerite iwo asanakhale a Seventh Day Adventists. Ndipo iwo anali ndi mkwamba wonse wawukulu mu pepala ya *Courier* kuno ku Franklin, Kentucky, pamene iwo onse anagulitsa malo awo ndipo anatenga... Iwo anaika tsiku linalake, ankazitsimikizira izo mwa Lemba—Yesu anali akubwera pa tsiku limenelo—ndipo iwo anapita pamwamba apo ndipo anatenga azeze awo ndi zinthu, ndipo anakakhala pamwamba pa phiri. Mmawa wotsatira anatsikapo, mame anali atagwetsera nthenga zonse pansu, ndipo iwo anabwera pansu ataphwetsedwa. Mukuona? Ndi zipembedzo zotsatira munthu ndi zinthu.

²⁰² Inu musati muzikhulupirira zimenezo. Yesu akhoza kusabwera kwa zaka zana panobe. Ine sindikudziwa kuti Iye abwera liti. Palibe munthu amene akudziwa kuti Iye abwera liti! Koma ine ndiyesera kumalalikirabe ndi kumachita chirichonse chimene ine ndingathe mpaka Iye achite kubwera. Ngati Iye sakhala ali kuno lero, ine ndikhala ndikumuyembekezera Iye mawa. Ngati Iye sakhala kuno—sabata ino, ine ndidzakhala ndikumuyembekezera Iye sabata yamawa. Ngati Iye sakhala kuno mu zaka khumi zotsatira, ndipo ine nkudzakhala ndiri moyo, ine ndidzakhala ndikumuyembekezera Iye zaka makumi atatu zinazo. Mukuona? Ine ndidzakhale ndikumuyembekezera. Ine sindikudziwa kuti Iye abwera liti,

koma ine ndikufuna kuti ndizikhala woona kwa Mawu Ake ndi woona kwa anthu Ake, ndi kumakhala moyo ngati Mkhristu, ndi kumayembekezera kubwera Kwake. Mukuona?

²⁰³ Pitirirani nako kulalikira mautumiki aku ndende, fikitsani aliyense populumutsidwa amene inu mungathe. Ine sindikudziwa kuti Iye abwera liti; palibe amene akudziwa. Koma ine ndinganene chinthu chimodzi ichi. Ichi ndi chimene ine ndikuyesera kuti ndizikuuzani inu, ndipo ine ndikuyembekeza inu simukuyesera kuikapo kutanthauzira kwanu kwanu... Osati kumulambwaza munthu uyu. Mulungu akudalitseni inu M'bale, Mlongo, aliyense yemwe inu muli. Izo zimawoneka ngati anali winawake wochokera kunja kwa mzindawu, chifukwa izo zinali p—pa positi khadi, ine ndikuganiza, kuchokera ku Denver, Colorado, ndi...Eya, Pike's Peak, Colorado. Kotero akhoza kukhala kuti winawake anaitumiza iyo pa makalata, koma i—izo ziri bwino mwangwiro. Iwo akhoza kudzaipeza tepiyi.

²⁰⁴ Koma tiyeni tizikumbukira, inu musati musinthe chirichonse, kupatula njira zanu kuchoka ku tchimo kupita ku chirungamo. Zingopitirirani nazobe pa ntchito yanu, kumapita nazo kumene chimodzimidzi basi. Onse amene mukumvetsa zimenezo momveka nenani, “Ameni.” [Osonkhana ayankha “Ameni!”—Mkonzi.] Mukuona? Zichitani zimenezo tsopano!

315. M'bale Branham, mu Mateyu 12:40, iwo amati, “Monga Yona anali mu—masiku atatu ndi usiku utatu mu mimba ya chinsomba; chomwechonso adzakhala Mwana wa munthu masiku atatu ndi usiku utatu mu mtima wa dziko lapansi.” Izo zingakhale motani tsiku limenelo kuti iwo amati—lero iwo akunena kuti Iye anaikidwa mmanda Lachisanu usiku ndipo anauka Lamlungu mmawa, kupanga izo usiku uwiri wokha ndi tsiku limodzi?

²⁰⁵ Tsopano, ngati inu mutazindikira, iwo anati, “Monga izo zinaliri” (inu mukuona?) mu masiku pamene Yona anali mmimba masiku atatu ndi usiku utatu. Ndi mkati mwa masiku atatu ndi usiku utatu, mkati mwa masiku atatu amenewo ndi usiku utatu, chifukwa inu simungalipangitse Lemba kunama. Mneneri anati, “Ine sindidzalola woyera Wanga kuti awone chivundi, ngakhalenso ine sindidzasiya moyo Wake mu hade.” Ndipo chivundi chimayamba mu thupi laumunthu mu maora seventethuu, amene ali masiku atatu ndi usiku utatu. Nthawiyina mkati mwa masiku atatu ndi usiku utatu umenewo—Iye ayenera kuti atuluke kuchokera mmanda.

²⁰⁶ Kotero pokhala masiku atatu ndi usiku utatu, sizikutanthauza kuti izo zikuyenera kukhala ndendende zimenezo; ndi nthawiina mkati mwa masiku atatu amenewo ndi usiku utatu. Iye ankayenera kuti atuluke mmenemo, chifukwa uneneri sungatheke kusweka, apo...Iye sakanati

awone chivundi ndipo ilo likanavunda ngati Iye akanakhala ndendende nthawi imeneyo.

316. M'bale Branham, ngati mwamuna anakwatirapo ndipo analekana (Kodi izi si zoipa (mukuona?), ochuluka kwambiri? Tsopano, ine sindikunena kalikonse kowatsutsa anthuwo; izo ndi basi zimene ziri pa malingaliro a anthu. Zedi, iwo akuvutitsidwa. Mkwatulo, anthu sankakonda kulingalira mochuluka za zimenezo; panalibe zochuluka kwambiri za zimenezo. Koma tsopano, izo zangokuta mdziko. Ndipo anthu akumawerenga zinthu zimenezi mu Lemba. Ndipo anthu, osankhidwa, kunja uko akumabwera muno kuti adzayang'ane pa izo. Ndipo iwo akumaziwona izo, ndipo iwo ali owona mtima. Iwo akufuna kuti adziwe. Ndicho chifukwa ine ndikufuna kuti ndiziyankhe izo basi ndi kumveka kokwanira kwa izo momwe ine ndingaziperekere izo kwa inu.)—**anali atakwatirapo ndipo analekana ndiyeno anakwatiranso mkazi yemwe nayenso anayamba wakwatiwapo ndipo analekedwa ndiyeno anadzakwatiwa kwa iye, ndipo awiri awa ang—angati—akwatitsidwe pamaso pa Mulungu—kodi iwo ali okwatirana pamaso pa Mulungu? Zingatheke bwanji kuti onsewo kapena mmodzi wa iwo adzakhale mu mkwatulo?**

²⁰⁷ Motani? Ine sindikudziwa. Ine sindingathe kukuuzani inu. Funsolo akuti, “Kodi iwo angathe kudzakhala mu mkwatulo?” Atalekana, aliyense wa iwo atalekana, aliyense wa iwo ali ndi mzake yemwe ali wamoyo, ndiye iwo anakwatiranso, onse a iwo akwatira kachiwiri. Ndipo tsopano, wina ali. . . Mkazi uyu ali ndi mwamuna yemwe ali moyo; mwamuna uyu ali ndi mkazi wamoyo. Ndipo tsopano, iwo ali ndi ana ndi zina zotero ndipo akufuna kuti abwere kwa Mulungu. Kodi iwo angathe kupita mu mkwatulo? Zimenezo zidzakhala kwa Atate akumwamba. Ine sindingathe kuyankha zimenezo. Mukuona?

²⁰⁸ I—ine ndinawona chinthu chimodzi. Baibulo linanena kuti iwo azitchedwa achigololo. Ndipo Baibulo linanena umonso, “Wachigololo sadzati adzalowe Ufumu wa Kumwamba.” Ndizo zonse zimene ine ndingathe kunena. I—ine ndikudziwa, izo zikungondipha ine kuti ndizinene zimenezo, koma ine sindingathe kunena kupatula zimene Mawu akunena. Ine ndiyenera kumakhala nawo amenewo. Ine ndikuyembekeza kuti zonsezo ndi zolakwika. Muli malo mu Baibulo. . .

²⁰⁹ Ine sikuti ndikukulangizani inu. Chonde, ndiroleni ine ndingokupatsani inu Lemba laling'ono. Chonde, chonde mus—mus—musati. . . Ngati inu mukukhala mokondwa ndi mwamuna wanu, mukukhala mokondwa, ndi mkazi wanu, chonde khalani mwanjira imeneyo. Kodi inu mutero? B—basi chifukwa ine ndinakuuzani inu zimenezo, m—musati muwasiye ana aang'ono amenewo opanda kwao ndi zinthu zonga izo. Mulungu wapangapo kubwezeretsedwa mu malo kwa anthu a—a—

amene anachita zinthu molakwika. Inu mukukumbukira, Yesu ananena za Davide pamene iye anali wanjala, iye analowa mu kachisi wa Mulungu ndipo anakadya mkate wopatulika, umene unali wololezedwa kwa wansembe yekha, ndipo akupezeka ali wopanda cholakwa. Wansembe nayenso ankachitira mwano Sabata pa tsiku la Sabata ndipo ankapezeka wopanda cholakwa, ndipo wamkulu kuposa Sabata anali kuno. Mukuona? Apo . . . i . . . T—tiyeni tingozisiyira izo kwa Mulungu, ndipo pitirirani, ndi kumangokhala momwe inu . . . Basi—zingokhalirani moyo kwa Khristu tsopano.

²¹⁰ Tiyeni tiwone, apo pakhoza kudzakhala mwayi woti inu mudzalowe umo. Musati mupange . . . Zolakwitsa ziwiri sizidzatheka kupangitsa chinacho kukhala chabwino. Basi zingopitirirani ndi kumakhala moyo momwe inu muliri—ngati inu muli okondwa palimodzi. Inu mukhoza kukhala muli ndi mzanu wolakwika. Ine ndinene chinthu chimodzi ichi: ngati inu muli ndi mzanu wolakwika mwa mkazi uyu—mu moyo uno, inu simudzakhala nazo konse izo mu winawo. Zolakwika zonse zidzakhala zitakonzedwa.

317. Kodi okhulupirira onse obadwa kachiwiri adzapita mu mkwatulo?

²¹¹ Ayi, otsalira okha, otsalira okha, osati okhulupirira onse obadwanso kachiwiri. Baibulo linati, “Ndipo akufa ena onse sanakhale moyo kwa zaka chikwi,” kenako iwo anawukitsidwa ndipo analekanitsidwa, nkhusa kwa mbuzi. Si onse obadwa kachiwiri ati adzapite mu . . . malingana ndi Lemba.

318. Kodi umboni wake ndi chiani kuti munthu ali kwenikweni wodzazidwa ndi Mzimu Woyera?

²¹² Yohane 14:26: Iye adza . . . “Pamene Mzimu Woyera adza (mwaona?), Iye akusonyezani inu zinthu ziri nkudza.” Mukuona? Iye akhala . . . Iye azipangitsa izo kukhala zangwirowo; “zopangidwa ndi anthu” sizingati zizichita; ndipo Iye ali Mawu. Pamene Iye Mzimu Woyera adza, Iye adzizindikiritsa Iyeyekha mwa inu ndi Lemba. Ndipo chimenecho ndicho chizindikiro choona chakuti Mzimu Woyera uli mwa inu, chifukwa Iwo uli Mawu.

²¹³ Tsopano penyani! Bwanji ngati iwe ukanayankhula ndi malirime? Ine ndikungofuna kuti ndikufunseni inu zimenezo. Yesu anati pamene Mzimu Woyera adza zimene Iye ati achite. Ndipo bwanji ngati iwe ukanayankhula ndi malirime, ukanalumphwa mmwamba-ndi-pansi, ukanafuula, ndi china chirichonse, ndiyeno nkubwera ku Mawu; ndipo ine nkukuuuzani inu ubatizo wa—kutsimikizira kwa inu mwa Lemba momwe ine ndachitiramu, kuti ubatizo mogwiritsa ntchito udindo wa Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera uli mwamtheradi kusamvetsetsa mu Lemba—palibe aliyense amene anayamba wabatizidwapo monga choncho—ndipo inu nkumapitirira nazo ndi kukangamila

izo mulimonse? Kodi inu mungandiuze ine kuti Mzimu Woyera mkati mwa inu ungachite chinthu monga chimenecho? Iwo ungate bwanji kuwakana Mawu Ake omwe?

²¹⁴ Pamene ine ndikukuwonetsani inu zimene zikuyenera kuti zizichitika mu tsiku lino, momwe kuti Mwana wa munthu ali woti adziulule Iyeyekha, ndi zomwe Iye ali woti azichite, ndi Malemba onse awa amene akhala alipo tsopano, ndiyeno nkumamuwona Iye akubwera pansu pomwe ndi kudzazindikiritsa izo, ndipo inu nkukangamira apobe ku chipembedzo ndi kumanena kuti ndinu wobadwa kachiwiri? Kodi inu mungati mupangitse kukhala zomveka zimenezo?

²¹⁵ Kodi ine ndingamamuze mkazi wanga kuti ine ndimamukonda iye, n—ndipo nkumakayenda ndi mkazi wina, ndi kumathamangathamange naye, ndiyeno nkumamuza iye kuchokera mu mtima mwanga kuti ine ndimamukonda iye? Kodi inu mukuganiza kuti chimenecho chikanakhala chikondi choona? Kodi iye angandiuze ine kuti akundikonda ine, ndipo pamene ine ndichokapo, iye nkumakathamanga thamanga ndi mwamuna wina?

²¹⁶ Ndizo ndendende zimene Israeli anachita kwa...Inu mukudziwa Baibulo pamenepo, momwe Iye ananenera, anayankhulira...Israeli, anati, “Inu mwatanyula miyendo yanu ndipo mwamutengera mmenemo mwamuna aliyense angabwerepo, ndipo inu mwasewera gawo lauhule kwa Ine; ndipo ine ndikulekani inu mwa chisudzulo.” Ndendende! Kodi icho nechiani? Inu mukuchita chigololo molakwira thupi lanu lomwe. Ndipo pamene mkazi apita kunja ndi kukakhala ndi mwamuna wina, kapena mwamuna ndi mkazi wina, pamene iwo ali okwatira kwa iwo, iwo akui pitsa mnofu wawo womwe. Ndipo pamene munthuyo anena kuti Iye ndi Mkristu ndipo nkumakana mwamtheradi Lemba kuti ndi loona, iye akuchita chigololo molakwira Thupi limene iye akudzinenera kuti ali mmenemo. Mukuona? Kotero izo ndi chilemba cha wotsutsakristu, mochuluka kuti zikanati zinyenge Osankhidwa ngati kukanakhala kotheka.

319. M'bale Branham, kodi ziri bwino kuti—mwana wamng'ono azivala timathalauza ndi akabudula?

²¹⁷ Wamng'ono bwanji? Inu mungokhala woweruza wa zimenezo; ngati muli Mkristu. Msungwana wamng'ono kapena mwana wamng'ono kwambiri, ine ndikulingalira, ine sindikudziwa, i...Chinthu chokha chimene ine ndikuchidziwa, Baibulo limanena kuti ndi themberero kuti mkazi azivala chovala ch—chimene chiri choyenera mwamuna. Mukuona? “Mkazi,” sanati, “mwana.” Koma tsopano, ine basi...Inu zikukomereni nokha pamenepo, i...Kwa mbali yanga, ine sindikuwona kanthu kolakwika kuti mwana wamng'ono kwambiri, msungwana wamng'ono kwambiri wausinkhu wa

zaka zinai kapena zisanu ali ndi... Pamene iwo ali ana aang'ono, inu mukudziwa momwe ine ndikutanthauzira, iwo amathamangathamanga kunja uko pabwalo. Ngati iye wavala, zimene inu mukuzitcha timathalauza kapena chirichonse chimene chiri, ali mwana wamng'ono kwambiri, i—ine sindikuwona kalikonse kolakwika ndi zimenezo. Mwinamwake...

²¹⁸ Mukuona, ine ndikungokuuzani inu zimene Mawu akunena. Ndi themberero kuti mkazi azivala chovala choyenera kwa mwamuna.

320. Kodi ife tizidzisonkhanitsa tokha palimodzi kuti? Ndipo inu munanena kuti mudzisonkhanitsa nokha pa Malipenga.

²¹⁹ Ine ndikukhulupirira, nkhumukhireni, Mlongo, aliyense yemwe inu muli, i—inu mukulakwitsa pamenepo. Ine sindinanene konse kuti muzidzisonkhanitsa nokha pa Malipenga. Ine ndinati Israeli anasonkhanitsidwa pa Malipenga, osati Mkwatibwi wa Amitundu. Ayi, ayi! Malipenga, kuwomba kwa Malipenga Asanu ndi awiri kunali koti kumusunokhanitse Israeli (ndi angati akudziwa zimenezo?) kuchokera konsekonse... Eya, osati... Ayi, ayi! A, nha! Ayi, osati—o—osati Israeli. Kotero, si zimenezo ayi... Ife sitikusonkhana pa Malipenga ndi—pa—Mkwatibwi sakutero. Malipenga akubwera pambuyo pa Phwando la Pentekoste. Mukuona? Ndipo mkwatulo ubwera... Ndipo izo... osati funso ili tsopano.

321. M'bale Branham, ngati inu muli nayo nthawi chonde longosolani Mateyu 10:41. Ine ndikanafuna kuti ndidziwe yomwe ili mphotho ya mneneri?

²²⁰ Chabwino tsopano, Yesu anati, “Aliyense amene amulandira mneneri mu dzina la mneneri, amalandira mphotho ya mneneri.” Mphoto ya mneneri ndi kukhala bwenzi naye mneneri. Aliyense amene alandira munthu wolungama mu dzina la munthu wolungama, amalandira mphotho ya munthu wolungama. Ndi kulondola uko? Ndipo ngati iwo akufuna kuti adziwe yomwe ili mphotho ya mneneri, ndiko kukhala bwenzi kwa mneneriyo. Mukuona? Imeneyo ndiyo mphotho. Iye ndi mzanu.

²²¹ Monga mkazi wa Chishunemu, izo zikhoza kudzagwira ntchito nthawi ina. Mukuona? Izo zinatero kwa iye. Mukuona? Muziwasamala antchito a Mulungu.

O, mai! Tsopano, ndife... i—ine basi ndikanati ndingotseka ndipo, mzanga, i—ine ndikudana nazo kuti ndichite izo, koma basi tangoyang'anani apa, tangoyang'anani zomwe, mazana. [M'bale Branham akukakamizidwa ndi osonkhana kuti ayankhe mowonjezera—Mkonzi.] Ayi! Koma—ine ndikudziwa, koma mukuona, i—ine ndikukonda inu kumanena zimenezo, koma ine ndikuganiza za anthu osauka awa ayendetsa mazana a

mailosi apobe usikuuno. Mai, iwo basi—pali ochuluka kwambiri mmenemo, ine . . .

322. M'bale Branham, ine ndikanafuna kuti ndidziwe za Zakachikwi. Kodi izo zidzakhala utatha Mgonero wa Chikwati, k—kapena izo zidzakhala pa dziko lapansi, zonse za izozo. Ine ndikuti—sindiri kumvetsa za zimenezo.

²²² Chabwino, M'bale kapena Mlongo, ndi zovuta kuti ine ndizimvetse zimenezo, mwiniwanga. Koma chinthu chokha chimene ine ndinganene ndi ichi: kuti Mgonero wa Chikwati ukubwera zisanayambike Zakachikwi.

²²³ Tsopano, mukuona, winawake, ine ndikudziwa penapake muno ali ndi funso pa zimenezo, amene anati, “M'bale Branham, muli—inu mukulakwitsa pa masabata sevente a Daniele. Apo adzakhala alipobe masabata sevente.” Ayi, Mesiya anali woti abwere ndi kunenera, ndipo mkati mwa masabata sevente, masabata sevente, zimene ziri zaka seveni, Iye anali wo—Iye anali woti adzadulidwe kumchotsa pakati pa amoyo ndi kupangidwa nsembe. Ndi angati akukumbukira zimenezo? Chabwino. Ndi zaka zingati ndiye zimene Yesu analalikirira, Mesiya? Zitatu ndi theka. Ndiye ziripobe 3½ zotsimikizika.

²²⁴ Ndipo mu Chivumbulutso mutu wa 11, aneneri awiri awa, iwo akunenera masiku wani sauzande thuu handiredi ndi makumi awiri atatu. Zaka zitatu ndi theka limodzi zikanali zolonjezedwa kwa Israeli pamene Mkwatibwi wa Amitundu akhala atapita. Ndi angati akumvetsa zimenezo tsopano? Mukuona? Chabwino, chabwino.

323. Izi ndi . . . Ine ndiri ndi thandala la chakudya cha masana ndipo ndimawatumikira ana aku sukulu yapamwamba kwa gawo lalikulu. Chibwererani mu Kuwala, ine ndinatenga makina a pinibolo (jukubokosi; iwo ati) jukubokosi ndaichotsa. Ana aang'onowo amasuta ndipo iwo amafuna nyimbo za roko n rolo p—pa wailesi. Ine ndimatsegula maora anai okha pa tsiku. Ine sindima—ine sindimavomereza kusuta kapena kumwa, koma ine ndikudandaula chifukwa chokhala ndi malowa.

²²⁵ Inu mukudziwa, limenelo ndi vuto. Mukuona? Chinthu chake ndicho, kuti inu m—inu muli—winamwake mukuyenera kumapeza zapamoyo. Koma inu mukudziwa chimene izo zikanachita kwa ine? Izo zikanandipangitsa ine manjenje kwambiri ine sindikanatha . . . i—i—izo . . . Inu mukhoza kupirira nazo izo, koma gulu laling'ono ilo la “Marike” mkati umo kumapitiriza nazo monga choncho, ndi “Mariketa,” i—ine—izo zikanandipengetsa ine misala. Mukuona?

²²⁶ Ndipo ine ndikukuuzani inu; i—ine . . . Ngati awo akanakhala ali anga, ine ndikudziwa chimene ine ndikadachita. Ine ndikanati, “Inu musiye zimenezo kapena tulukani muno.” Mukuona? Ine ndikanati ndiziyendetsa malo a mtundu

wabwino kapena osakhala nawo nkomwe. Koma inu, ngati inu mukuyenera kumachita izo kuti muzipeza zapamoyo, ine sindikufuna kuti ndisakulabadireni inu, M'bale kapena Mlongo. I—ine ndikudziwa kuti ndi kovuta kunena zinthu izi; koma i—izo basi. . . Izo si zolondola (inu mukuona?), chifukwa izo zikuwoneka monga ziri ngati . . .

²²⁷ Monga winawake ananena mmawa uno zokhudza akazi athu kuvala madiresi awo aafupi kwambiri, azimayi athu achikulire, anali chitsanzo choipa kwa madona achichepere. Ine ndikuganiza kuti izo ndi zolondola aponso. Inu mukuona?

²²⁸ Ndipo ine ndikuganiza chinthu icho chomwe. Pamene iwo akukuwonani inu uko kumene kusuta konse uku ndi kutengeka kukuchitika, ndipo nkumadziwa umboni wanu, ndi kutukwana konse uku n—ndi kumakhala pamene pali ana aang'ono awo monga choncho, ndipo iwo akumapitiriza nazo monga choncho, ndipo inu nkusamanana kanthu pa izo, ndi chinthu choipa pa umboni wanu. Inu kachiteni chirichonse chimene Ambuye ati akutsogolereni inu nacho. Ine ndipemphera kuti Mulungu akutsogolereni inu ku njira yolondola.

324. Ngati (k-u-i-m-. . .) kuima mu mzere kuti ulowe mu mpingo chidzangokhala chiri chikumbutso chabe, chidzachitike nchiani ngati ife sitidzadutsa mu chisautso? Kodi ife ndi oti tidzakhale—tiziwona—zofanana—kuvutika kwina? Ngati ife sitiri oti tiwona. . .

Mukuona? I. . . Funso ili mwinamwake ndi ili. Ine ndikuyesera kuti ndifulumire; i—i—ine sindimayenera kuti ndichite izi. Ndimayenera kuziyika izi mmbuyo, chifukwa apo pali malo omwe iwe ungakhale pa izo kwa ora (mukuona?) ndi izo—basi nkuziphwasulira izo pansi. I—ine ndilekeza.

²²⁹ Yang'anani. Anthuwa akufuna kuti anene zimenezo, kuganiza kuti iwo—Mpingo ufika podzagunda chisautso. Mukuona? Iwo sudzatero; Iwo sungati (mukuona?), chifukwa Iwo wawomboledwa kale.

²³⁰ Tsopano, mpingo, o—okhulupirira mwadzina monga Loti, iye adzadutsa mu nthawi ya chisautso (mukuona?) ndi kudzapulumutsidwa monga momwe zinaliri ndi moto. Nowa anadutsa mu nthawi yachisautso, ananyamulidwira pamwamba pa icho, anatuluka umo ndi Hamu amene anadzaliyipitsa dziko lapansi kachiwiri. Mukuona? Loti anatuluka umo, ana ake omwe aakazi anagona ndi iye, ndipo anabala ana mwa ana ake aakazi omwe. Mukuona? Koma Abrahamu anabala apo Mbewu Yachifumu, anabala apo Mbewu ya lonjezo. Enoki anapita ku ulemerero mu mkwatulo, anangoyamba kuyenda ndipo anapita kwawo. Iye sanadutse konse mu nthawi ya chisautso. Inu mukuona?

²³¹ Ndi inu apo. Mukuona? Uwu suli, Baibulo silingatero mwa choimira. . . Ndipo zoimira sizingati zilephere. Mukuona?

Ilo siliri kuneneratu kuti Mkwatibwi...Tsopano, mpingo udzadutsa mu nthawi ya chisautso.

²³² Tsopano, anthu amati, “Nanga bwanji oyera oyambirira?” Uko kunali kusuntha kwa nyengo. Izo zinali pansi pa kuzunzidwa, chimene ngati inu mukanakhala muli kuno kudzaimva *Mibadwo ya Mpingo* iyi, ndi kuwona momwe iwo anapitira kunja mu mdima uja ndipo ankayenera kuti achite zimenezo, ndiye izo zikusonyeza kumene iwo ankayenera kuti atenge kuzunzika kumeneko, chifukwa uliwonse wa mibadwo ya mpingo ndi chirichonse chinkayamba kusonyeza kuti iwo ankayamba kuchitirapo mwamdima ndi mwamdima, mpaka potsiriza iwo anapita ku malo amphumphu oti iwo analikana Dzina Lake ndipo anatenga dzina lina kuti iwo anali amoyo ndipo iwo anali okufa, Sarde. Ndiyeno izo zinatulukira uko, Tiyatira ndi Sarde, ndiyeno zinatulukira uko—ndiyeno izo zinayamba kutulukira uko ku Filadefiya ndi zina zotero, ndiyeno zinafika ku nthawi ya kuitanira kunja kwa Mkwatibwi amene anali woti athawe chiweruzo chonse. Uyo anawerengedwa ngati woyenera kuti athawe chiweruzo chonse ichi ndi mkwiyo umene unali woti ubwere pa dziko lapansi, kuti inu mukhoze kuwerengedwera ngati oyenera kuti muzithawe izo, osati kudutsa mu zimenezo, kuzithawa izo. Mukuona? Kodi inu mukumvetsa tsopano, aliyense? Mukuona?

²³³ Mpingo, ofundawo, chirichonse cha kunja kwa Mkwatibwi wosankhidwa chidzadutsa mu nthawi ya chisautso. Iwo sadzauka mu chiukitsiro choyamba: “Okufa ena onse sanakhale moyo kwa zaka chikwi,” odzozedweratu okha, okonzedweratu, Mkwatibwi wosankhidwa, kusankha kwake kwa Mulungu. “Ndi ndani amenewo, M’bale Branham?” Ine sindikudziwa. Ine sindingathe kukuuzani inu omwe iwo ali, koma ine ndikudziwa kuti adzakhala alipo uko, chifukwa Ambuye anati iwo akanati adzatero. Mukuona? Iwo ndi amene ati adzakwere mmwamba kuchokera mu chisautso, koma ena onsewo adzadutsa mu chisautso, kupita pansi, ndipo chirichonse chidzakhala chitaphedwa zisanayambe Zakachikwizo. Ndiyeno—olungama adzatulukira uko mu Zakachikwi ndi kudzakhala moyo zaka chikwi.

²³⁴ Ndipo zikadzatha zaka chikwi, ndiye chiweruzo cha Mpandowachifumu Woyera wawukulu chikubwerapo, ndiyeno okufa, onse abwino ndi oyipa ali kuwukitsidwa. Ndipo mabuku ali kutsegulidwa, ndipo Bukhu la Moyo liri kutsegulidwa; ndipo oyera, Mkazi ndi Mwamunake, akukhala ndipo akuliweruza dziko. Ndipo apo zikufika pochitika mwambiwo: “Ndipo Iye adzawaweruza mafuko onse ndi ndodo ya chitsulo.” Mafuko onse adzaima pamaso pa Iye pamenepo, ndipo Iye adzawaweruza iwo ndi ndodo ya chitsulo. Iye adzalekanitsa nkhusa kwa mbuzi ndi kunena kwa mbuzi, “Chokani,” ndi nkhusa, “Bwerani, inu odalitsidwa ndi Atate Anga.”

²³⁵ Tsopano ndiye, uko kudzakhala kuli msonkhano wa msasa wa oyera mofalikira pa dziko lapansi. Ndipo Satana akumasulidwa kuchokera mu ndende yake ndipo akupita kuti akapange nkondo kachiwiri ndi oyera, ndendende basi zimene iye anachita mu Ulemerero pa kuyamba pomwe. Ndiyeno Mulungu navumbitsa moto ndi sufure kuchokera mmiyamba, ndipo dziko lonse nkuchotsedwapo. . . Ilo basi lidzawotchedwa lonse ndi kuwonongedwa. Ndipo uko kudzakhala kulibenso nyanja, sikudzakhala kulibenso madzi, sikudzakhala kuli kalikonse kati kadzatsalire pa dziko lapansi. Ziphala zamoto zidzafalikira ndi kuphulika ndi kupemerera, ndi chinthu chonsecho. . .

²³⁶ “Ndipo ine ndinawona Miyamba Yatsopano ndi Dziko Latsopano: pakuti miyamba yoyamba ndi dziko lapansi loyamba zinapita; ndipo uko kunali kopandanso nyanja. Ine, Yohane, ndinawona Mzinda Woyera ukutsika kuchokera kwa Mulungu kuchokera Kumwamba munga Mkwatibwi atakongoletsedwera kwa mwamuna wake.” Mukukumbukira zimenezo? Ndipo mwa Mkwatibwi uyu. . . “Taonani Kachisi wa Mulungu ali ndi anthu,” ndipo Mulungu azikhala limodzi ndi iwo pa Mzinda wowumbidwa mwa piramidi uwu mailosi fifitini handiredi mbali zonse. Ndipo pamwamba pa Mzindawo padzakhala Kuwala. Amen!

O, mzinda uja pa Phiri la Zioni,
Monga mlendo, komabe ine ndikuwukonda
iwo apobe.
Iwe ndidzakomana nanu mu mibadwo
imeneyo,
Pamene ine ndidzafika mu mzinda umenewo
pa phirilo.

²³⁷ Pamwamba pa Phiri la Zioni azidzakakhala Mwanawankhosa. Ndipo Mzindawo sudzamasowa kuwala, pakuti Mwanawankhosa ndiye Kuwala kwakeko. Ndipo pamwamba pa Mwanawankhosa kudzakhala kuli Atate, amene ali *Logos*, Mulungu, Kuwala kwakukulu, Kuwala Kwamuyaya kumene kuzidzawala pamwamba basi pa Mpandowachifumu. Ndipo Yesu sadzakhala ali pa Mpandowachifumu wa Atate Ake, Iye adzakakhala ali pa Mpandowachifumu Wake. Ndipo Atate azidzayandama pamwamba pa Mwanayo, chimene Atate ndi Mwanayo adzakhala ali Mmodzi. “Ndipo pamene iwo akadali nkuyankhula, Ine apobe ndizidzayankha. Iwo asanati aganize, ine ndikuwaganizira iwo.” Ndiko kulondola.

²³⁸ Ndipo Yesu adzapereka m’badwo wangwiro, ngwiro kwa—Mulungu wamoyo wangwiro, umene Iye wawuwombola ndi kuwupereka iwo kwa Atate. Ndi kulondola uko? Adzautembenezira iwo kwa Mulungu Atate amene ali Mzimu, osati munthu, Mzimu. Chirengedwe chonse chabwino

chitasonkhana palimodzi, ameneyo ndiye Mulungu. Ndipo mu ubwino... Tsopano, chirichonse chopotozedwa kuchokera ku chabwino ndi choipa; umenewo ndi ufumu wa Satana. Zabwino zonse ndi za Mulungu. Zoipa zonse ndi zake. . .

²³⁹ Ndiyeno Mulungu akukhala wogwirika mwa Munthu wotchedwa Yesu Khristu amene anali Mwana Wake. Mwana uyu anapereka Moyo Wake kuti Iye akhoze kubweretsapo ana ena, kuti Mulungu akhoze kukhala wogwirika, akugwira ntchito mwa onse ndi zonse. “Pa tsiku limenelo inu mudzadziwa kuti ine ndiri mwa Atate, Atate mwa Ine, Ine mwa inu ndi inu mwa Ine.”

²⁴⁰ O, m’bale, limenelo lidzakhala tsiku lenileni. Inu simudzasowa kumadzayendetsa kuchokera ku Birmingham kuti mudzamvere Uthenga; Uthenga udzakhala uli ndi ife kumene apo sichoncho izo? O, iyo idzakhala ili—iyo idzakhala ili yodabwitsa, nthawi yodabwitsa. Ife tikuyembekezera tsiku limenelo; Mulungu alifulumizitse ilo kuti libwere.

²⁴¹ Mzinda wawukulu uwo uli pamenepo (tsopano, mukuona?), iwo sudzakhala. . . Inu mukuganiza, “Mailosi mazana fifitini mmwamba?” Ndi zimene Baibulo linanena. Tsopano, iwo sudzakhala mailosi mazana fifitini molunjika mmwamba monga choncho. Mukuona? Ife tiri ndi kuyeza kwina kwa chirengedwe kumene mbali zonse zimakhala zofanana; ndiyo piramidi. Mukuona?

²⁴² Ndipo Mzindawo uzidzayambira mwinamwake pafupi pa madigirii sikisite. Ndipo ngati iwo ukuyamba, mailosi mazana fifitini a izo, tangoganizani kukwera kwake komwe pati padzakhale, koma momwe zizidzatengera nthawi kuti ukafike pamenepo. Iwe sudzamadziwa nkomwe kuti ukuyenda chokwera phiri. Pakuti mailosi fifitini handiredi chokwera pa madigirii sikisite, iwe uzidzangokhala ngati *chonchi*. Mukuona? Ndipo Mzinda wonsewo uli pa phiri ili. Ndipo iwo ndi wokwera basi momwe iwo uliri kotalika; iwo ndi wautali basi momwe iwo uliri mwakutambalala. Usinkhu, monga kuya, monga kutambalala, i—izo ndi zofanana; makoma onse ndi ofanana. Piramidi imakhala ndi makoma anai, ndipo makoma anai amenewa adzakhala ali. . .

²⁴³ Tsopano, makoma ozungulira Mzindawo adzakhala a—ali mapazi 216 kukwera kwake, mikono 144, ndipo uliwonse wa iwo ndi mwala. Tangoganizani za Mzinda umenewo, amzanga. O, mai! Nchiani—kodi ife tikukhaliranji kuno mu malo otentha awa? Kodi ife tikuchitiranji zinthu izi? Chifukwa chiani ife tikuyendetsa monga choncho? Chifukwa chi—chifukwa chiani ife tikuvutikira? Izo ndi zoyenera inchi iliyonse ya ulendowu.

O, kuvutikira kwa mnjirayi sikudzaoneka
ngati kanthu,
Pamene ine ndidzafika kumathero a njirayi.

Uko nkulondola. Ndipo, o, nthawi yake yomwe iyo idzakhala ili.

²⁴⁴ Ndipo kumeneko Yesu adzakhala pa Mpandowachifumu. Ndipo kuchokera pansi pa Mpandowachifumuwo kuzidzayenderera mtsinje wa Moyo, ukuyenderera pansi pa makoma anai awa kupita mu maphompho aang’ono, ndi kupita mu nthambi zazing’ono, ndi kubwera apo kudzapanga mtsinje, ndi kutsikira kudutsa mu Mzindawo. Iwo uzidzayenderera chotsika kumene kudutsa mu misewu monga choncho, ndipo ku mbali iliyonse kutaima mitengo ya moyo imene iti izidzabala—kapena izidzasintha zipatso zake—masiku sate aliwonse. O, Mzinda wakewo.

²⁴⁵ Ndipo kumbukirani, Mulungu, Mlengi, amene analenga miyamba ndi dziko lapansi, ali mu Ulemerero pakali pano akuukonza Mzinda umenewo. Abrahamu ankawufunafuna Iwo. Iye anachoka kwawo; iye anasiyana ndi chirichonse chimene chinali chofunika kwa iye ndipo anali kufunafuna. . . Chifukwa? Iye anali mneneri. Ndipo pokhala mneneri, iye anali wolumikizana ndi Mzimu ndipo anali gawo la Mzimuwo. Ndipo Chinachake chinkamuza iye mkati mwake, “Ulipo Mzindawo,” ndipo iye anayamba kuwufunafuna Iwo. Anati, “Ine ndine mwendamnjira, mlendo. Ine ndikufunafuna Mzinda umene Wowumanga wake ndi Wowupanga ndi Mulungu.” Iye ankadziwa kuti Mzinda umenewo unali kwinkwakwe. O, mai! Ndipo ine ndikukhulupirira kuti pa malo pomwepo pamene iye ankawufunafuna Iwo, uko komwe mu Palestina, uko ndi kumene Iwo uti udzaukitsidwe, pakuti Iwo uli pa Phiri la Zioni. Uko ndi kumene Iwo uti udzakhale uli.

²⁴⁶ Tayang’anani kumene Iwo uti udzatambasukilire mp—mpaka mu nyanja, kuchokera ku nyanja mpaka ku nyanja. Taganizani za Mzinda wa mailosi mazana fiftini uli kumeneko pa mapiri a Ambuye. O, izo zidzakhala zodabwitsa.

²⁴⁷ Ndipo mkango ndi mwanawankhosa zizidzagona pansi limodzi. Mkango uzidzadya maudzu ngati ng’ombe. Ndipo chimbalangondo chidzakhala chiri chofatsa, ndipo nkhandwe izidzawetedwa. Nthawi yake yomwe iyo iti idzakhale ili! Palibe kanthu kamene kati kazidzavulaza kapena kuwononga; chirichonse chidzakhala chiri mu mtendere ndi chikondi. Uko sikudzakhala kulonso usinkhu wokalamba; uko sikudzakhala kulonso kudwala, sikudzakhalanso kufa.

²⁴⁸ Abale, iyi si nkhani ina ya Santa Claus, nthano inayake, izi zinalembedwa mu Mawu. Ndipo Mawu sanayambe alepherapo. Ndipo kuganiza za lonjezo lomwe la. . . Osati mmbuyo mu tsiku la Baibulo, koma mu tsiku lino, tsiku limene Mulungu—lero. Palibe kadontho kamodzi kayamba kalepherapo ka Mawu Ake. O, ine ndikupita ku Mzinda umenewo. Ine ndikuwukonda Iwo, sichoncho inu?

249 Ayi! Tsopano, M'bale, Mlongo, iyo ikuti twente itapitirira naini. Ine ndikudziwa ine ndiri nao abwenzi ena pano ochokera kutali komwe ku Kentucky. Ine ndikudziwa ine ndiri nawo abwenzi pano ochokera ku zigawo zosiyana za dzikoli. Ngati inu mukufuna kuti mukhale usiku wonse, ine ndikakulipirirani chipinda chanu. Ine ndinakuuzani inu, inu muli ndi chakudya chimene chikukudikirani inu ndipo ndikulipirirani motelo yanu ngati inu mukufuna kuti mutsalire. Ndipo chinthu chokha chimene inu mukuyenera kuti muchite ndi kukamuwona iye kumbuyo uko, ndipo ine zedi ndichita zimenezo. Ine ndichita chirichonse chimene ine ndingathe kuti ndikuthandizeni inu. Ine ndimakukondani inu.

250 Ine sindikutanthauza kuti ine ndiyankhe mafunso awa mwinamwake nthawizina mosiyana. Ngati inu simukuzikhulupirira izo, izo ndi zabwino mwangwiro. Ine ndikufuna kuti inu muzindikonda ine chimodzimodzi basi, chifukwa Mulungu akudziwa ine ndimakuchitirani inu mwanjira imeneyo. Ine ndikungoyankha mafunso awa mwa kupambana kwa kudzi—ine ndikhoza kukhala kuti ndimalakwitsa mwa ena awo, amzanga, koma uko sikunali kulakwitsa kwadala. Ngati ine ndikadakhala ndi pafupi mafunso sikisi kapena eyiti, kotero ine ndikadangokhala basi ndi iwo nkungowalongosola iwo mpaka mmusi, koma ine, mmalo moti ine ndidutse mwa iwo tsopano. . . Ine ndiri nawo ochepa a iwo okhudza chikwati ndi chilekano. Ine basi ndinangokhala—ndimaganiza kuti ine ndikanayankha ochepa a iwo. Ine sindinathe kuwapezanso ena ali apa, kuwatenga iwo, koma ine ndiri ndi mafunso ena ofunikira kwambiri pano, mafunso ofunikira kwambiri. Ine ndikufuna kuti ndikuyankhireni inu amenewo ngati ine ndingathe.

251 Tsopano, ngati inu mukukhala kozungulira kuno, mudzamuimbire Billy, Lachitatu; ine ndidzakhala nditadziwa pofika apo ngati ine nditi ndidzabwerere. Ine ndipemphera sabata ino. Koma ine ndiri nako kuyankhulana kwapadera kochulukaka, o, mulu pafupi monga *choncho*. Ndipo ine ndiri nazo pafupi zochulukaka *choncho* mu Arizona zoti ndidzazipange limodzi la masiku amenewa pamene ine ndingathe. Ndipo awo ndi anthu amene ali kudwala kwenikweni. Ena a iwo ali ndi mavuto, ndipo basi iwo sakudziwa choti—amuna ndi akazi omwe ali ndi mavuto.

252 Ndipo ena a awa pano anachita kusinthidwa kuti akhale a kuyankhulana kwapadera, chifukwa ine sindikanatha kuwawerenga iwo apo bwino, zimene anthu amanena mmenemu zokhudza zochitika mu ukwati wawo ndi zinthu monga *choncho*. Ndipo ine ndinamumapangitsa Billy kuti apite ndi kukafufuza yemwe iwowo anali, n—ndi kuwaitana iwo, ndi kuwauza iwo kuti ife tingowaika iwo pa kuyankhulana kwapadera, chotero

ine ndikhoza kuyankhula pa izo. Zina zovuta kwambiri, ndipo ndi mafunso amene akuyenera kuti ayankhidwe.

253 Ine ndiri pano kuti ndiyesere kukuthandizani inu, chifukwa ine ndikukukondani inu. Inu ndinu ana anga amene ine ndakubalirani kwa Khristu. Ine ndikudzitengera aliyense wa inu. Ine ndikudzitengera inu usikuuno; ine ndimadzitengera inu nthawi zonse; ine nthawizonse ndimadzitengera inu ndipo izo—ngati m'bale wanga ndi mlongo. Inu ndinu ana anga; i—ndine bambo wanu mu Uthenga, osati bambo monga zikanakhalira ndi wansembe, ine nd—ndine bambo wanu mu Uthenga monga Paulo ananenera uko. Ine ndakubalirani inu kwa Khristu, ndipo tsopano, i—ine akutomeretsani inu kwa Khristu; kumeneko ndi kukupalitsani inu ubwenzi kwa Khristu monga namwali wosadetsedwa. Musati mundikhumudwitse ine! Musati mundikhumudwitse ine! Inu zikhalanibe namwali wosadetsedwa.

254 “Kodi ine ndizichita motani izo, M'bale Branham?” Zingokhala molondola ndi Mawu; zikhalani moyo woyera ndi wangwiro; musati muzikhala ndi kanthu kochita nazo zinthu za mdziko. Ngati chikondi cha ilo chiri mu mtima mwanu, itini, “O, Yesu, chonde chotserani icho kutali ndi ine. Ine sindikufuna kuti ndizikhala monga choncho.”

Tsopano ine sindikutanthauza kuti ndingokhala munthu winawake a—amene akunena izi. I—ine ndikutanthauza kuti ndikhale wokhulupirira weniweni. Kukhulupirira Yesu Khristu ndi kumamukhalira Iye moyo tsiku lililonse. Osamachita choipa ayi.

255 Tsopano, nthawi zambiri ine ndimayankhula za chikhulupiriro cha Chikalvini. Tsopano, musati muziganiza kuti izo zimakulolani inu kumasuka kuti muzichita chirichonse chimene inu mukuchifuna. Munthu wina tsiku lina... Ine ndinati, “Kodi inu munapita ku tcharitchi?”

Iye anati, “Ine ndinapita kukasaka.”

Mkazi wa mwamunayo anabwera kwa ine, ndipo iye anali akubwera kuchokera kochapa zovala Lamlungu. Ndipo ine ndinati, “Chifukwa chiani inu simunapite ku tcharitchi?”

Iye anati, “Ine ndimachapa zovala zanga.”

Ine ndinati, “Inu simukanati muchite zimenezo.”

“Chabwino,” iye anati, “ine sindine wazamalamulo wakale.”

Ine ndinati, “Koma ine ndimaganiza kuti inu ndinu Mkhristu.” Mukuona? Ine ndinati, “Kodi inu mukudziwa kuti mukuika chopunhwitsa mu njira ya winawake.” Mukuona? Ine ndinati, “Izo...”

“Chabwino, a a, i—ine ndikukhulupirira izi. Ine sindisowa kuti ndizichita zinthu zimenezo. Ine sindine wazamalamulo.”

256 Chabwino, tayang'ana M'bale wanga, Mlongo, tayang'ana kuno. Paulo anati, “Ngati kudya nyama kungaike chopunthwitsa mu njira ya m'bale wanga. Ine sindimadyanso nyama utali wonse pamene dziko likuima.” Ndipo ine ndikuganiza izo zingakhale gawo lonse zabwino. . .

257 Tsopano, kuti, “M'bale Branham, inu mumasaka. Kodi inu simunayambe mwasakapo Lamlungu?” Ndiroleni ine ndikuuzeni inu chinachake. Ayi—ine sikuti ndikudzisisita pa nsana ndekha pa izi, koma i. . . Ine si Wachisabata tsopano, ine ndimakhulupirira kuti Mzimu Woyera ndiwo Sabata lathu. Ine ndimakhulupirira zimenezo, koma ine ndimakhulupirira kuti ife tizilemekeza chiukitsiro icho ngati chikumbutso. Icho ndi chikumbutso chomwe ine. . . Ngati inu mumalemekeza tsiku lililonse, zilemekezani chiukitsiro chimenecho.

258 Tsopano, palibe lamulo la kusunga tsiku lina lililonse, chifukwa inu mumalowa mu Sabata, mtendere, pamene inu mulowa mwa Iye. Ine ndiri nalo funso limenelo apa kuti ndiliyankhe posakhalitsapa mulimonse, ngati Ambuye alola, la kuti kodi tsiku la Sabata ndi chiani? Ine ndilongosola izo, Mulungu akalola.

Ndipo tsopano zindikirani, zikumbukirani izi. Mukuona? Pamene ine ndinali mnyamata wamng'ono, komwe kuno kumene ma Eichs ankakhala kutsatira mseuwu, ine ndinali pafupi usinkhu wa zaka fortini; ine ndinkatchera misampha pofuna zapamoyo. Chinthu chokha chimene ine ndinali nacho choti chithandizire kuti tipeze mkate mnyumba mwathu chinali kugwira akanyimbi, abwampini, maoposamu.

Ine ndinkakonda kutchera misampha, ndipo ine ndinkayenera kumachita zimenezo. Ine ndinkapita ku sukulu ndikununkha ngati kanyimbi, ndipo i—ine ndinali ndi chovala chimodzi chokha, ndipo ndi zokha zimene ine ndikanatha kuvala. Ndi zonse zimene ine ndinali nazo. Amayi ankandivula izo ndi kuzichapa izo, ndipo ndinali kuzivalanso izo; ndipo tsopano, ndi momwe ine ndinkapitira ku sukulu, mnyamata wamng'ono. Koma ine ndinali nditaima kumtunda uko usiku wina; ine ndinati, “Ine ndatchera misampha iyo kwa a Wathen, kuntunda uko.” Ine ndinkanyamuka mmawa uliwonse pafupi 2:00 koloko ndi nyali kuti ndikawonjole misampha imeneyi, ndi kubwererako mu nthawi yabwino kuti ndipite ku sukulu. Ine ndikagwira kalulu; ine ndinkapeza ma senti fifitini pa iye. Ine ndinkakhoza kugula bokosi la zipolopolo kuchokera pa zimenezo, ndipo mwinamwake izo zinkapha akalulu atatu kapena anai. Zimene ife tinalibe kuti tipangire masakono ena ndi akalulu—bwanji, supu ya chakudya chamadzulo, ine ndinkakhoza kugulitsa enawo, ndipo mwinamwake nkupeza zokwanira kuti ndikagulepo buledi, kapena chakudya china, kapena ufa wina woti tikapangire nsuzi nazo. Ine sindikudziwa

ngati inu munasowa kumakhala moyo monga choncho kapena ayi.

259 Ine ndinkatchera zingwe za mbedza mu mtsinje; ndinkapita, ndi kukazitenga nsomba zimenezo, ndi kuzigulitsa izo masenti khumi pa libisi. Kutchera zingwe za mphuta. Ine ndinalibe ngalawa; ine ndinkasambira kupita uko ndi chipika. Kulowa mu mtsinje—ndipo kuli kuzizirabe—kuika chitini changa cha nyambo pa chipika apa ndi k—kumapalasa ndi nkhati ndikupita monga choncho, thupi langa lamaliseche liri mu mtsinje, ndi kuyendetsa ichi. . . Ine ndiri ndi chingwe kumbali iyi, nditadzimangirira nsomba zangazo. Nsomba zachikale zija za milamba zikumenyetsa zipsyepsye pa ine mmiyendo zikuchita monga choncho, ndipo ine nkumaika nyambo yanga apo. . .

260 Koma penya, usiku wochuluka ine ndinkakhala ndikupita ku mtsinje umenewo pa 11:00 koloko ndi kukagwedeza chidutswa chirichonse cha nyambo kuichotsa pa chingwe chimenecho. Ngati ine sindinathe kukola zokwanira mu masiku sikisi, ine sindimafuna kuti ina ibwerepo pa la seveni. Ine ndimayima kumeneko mu mvula.

261 Usiku wina ine ndikutha kudziwona ndekha nditaima, nditatsamira. . . Ine ndinali wochimwa; koma ine ndinali kuima, nditatsamira pa nsanamira monga choncho, pakhomo. O, inali ikukhuthukira pansu mvula, pafupi 11:00 koloko. Ine ndinati, “Ine ndichedwa usikuuno, koma ine ndikupita kuti ndikawonjole uliwonse wa misampha imeneyo. Ine sindizigwira izo pa Sabata.” Ine ndinkati, “Ine sindi—ine sindimakatchera misampha imeneyo.” Mulungu ankazilemekeza zimenezo.

262 Ine ndikukumbukira nthawi pamene ine nthawizonse ndinkafuna, ine nthawizonse, moyo wanga wonse ndinkafuna kuti ndidzakhale msaki. Agogo anga aamuna anali. Inu mukudziwa, agogo anga aakazi anabwera kuchokera kumalo otetezedwa; iwo ankalandira pensioni. Ine ndimangokonda mthengo.

263 Ndipo ine ndikukumbukira ine nthawizonse ndinkafuna. . . I—ine ndinkangofuna moyo wanga wonse. . . Ndinkaganiza ngati ine nditi ndidzapeze konse ndalama zokwanira mpaka kuti ine nkukhoza kukhala nayo mfuti ya .30-30. . . Ngati ine ndingati konse ndichite zimenezo, ndiye ine ndidzagula misampha yambiri. Ine ndingamadzapite ku mapiri; ine ndidzalisiya dziko lonse kuti lizipitirira. Ine ndinkaganiza, “Mwinamwake nthawi ina ngati ine nditadzatenga ya .22 yanga ndi kumaphunzira kuti ndikhale wowombera bwino, msaki wina nthawiina azidzafuna kuti ine ndipite naye. Ngati ine ndingadzafike pokhala wowombera bwino, iye azidzandilola ine kuti ndizipita naye kwa chitetezo chake; ine ndidzayamba kumapita kosaka.” Ine ndikuyang’ana, zitapachikika pa makoma anga, ndi mfuti zopambana zimene ndalama zingathe kuzigula zapachikika

pamenepo, mpaka kuti ine ndikhoza kumawabwereka anthu mifuti kuti apite kokasaka.

²⁶⁴ Iye amandilola ine kuti ndizipita ku mapiri ndi kumakalalikirira, ndipo ena a anamulondolera opambana amene alipo pa dziko amanditenga ine kokasaka, mwaulere. “Chisomo chodabwitsa, kukoma kwake kuchimva.”

²⁶⁵ Pamene ine. . . Ngakhale mmawa uno, msaki wa agwape wachikulire kuno kwinkwake ali ndi Remington ya .35—ine sindimaisowa kwenikweni mfutiyo—koma iye anaika nkono wake mondikumbatira ine, anati iye akufika pokalamba kwambiri kuti azisaka, “Ine ndikufuna kuti ndikupatse iwe mfuti yanga.” Ine ndinaganiza za zimenezo pamene ine ndinali mnyamata wamng’ono, momwe, ngati ine ndinayamba ndalingalirapo kuti ndikanadzakhala konse ndi mfuti yonga imeneyo, o, mai, chimene iyo ikanakhala ili. Ndipo tsopano, ine ndikungoganiza, zitapachikika apo pa khoma langa, mfuti zabwino, malo oti ndipite kukasaka.

²⁶⁶ Ine ndikukumbukira ndikupita kwina, ndipo anyamata ankakhoza kugula chitsononkho cha ayesikirimu. Ndipo nthawizina ena a iwo ankakhoza kukhala ndi ndalama yapadera ndipo iwo ankakhoza kundigulira ine chimodzi. Mai, ine sindikanatha kuti ndiwagulire iwo mowabwezera. Ine ndinkaganiza, “Ngati ine. . .”

²⁶⁷ Ndipo iwo nthawizina anakonda kugula zakale izi, zimene ife tinkazitcha “zitumbuwa za nyama za mudlark.” Sindikudziwa ngati inu nonse mukuzikumbukira kapena ayi, koma ena inu a nthawi-zakale. . . Inu munkagula izo ndi faifi senti, mulu wonse wa anyezi wokazingidwa ndi izo. O, ine ndinkazikonda zinthu zimenezo. Ndiri mwana wamng’ono ife tinalibe. . . Tinkangokhala ndi chikondamoyo chothira uchi—inu mukudziwa momwe izo zinkakhalira—kuti uzidye.

²⁶⁸ Tsopano, winawake akandigulira ine chimodzi cha zitumbuwa zanyama zimenezo, ndipo mnyamata, ine ndinkachita kunyambita zala zanga pamene ine ndinachigwira icho. Icho ch—icho chinali—chinkakoma bwino kwambiri. Ndipo ine ndinkaganiza, “Mnyamata, munthu uyo, ngati ine ndikanadzakhoza kokha kudzamugulira iye chitumbuwa chanyama.” Ndipo tsopano, ine ndikhoza kuwugulira mpingo chakudya chawo chamadzulo.

²⁶⁹ Ine ndikukumbukira zinthu zonsezo, ndipo kodi izo zinachokera kuti? Chisomo cha Mulungu, palibe kanthu kamene ine ndinakachita.

²⁷⁰ Ine ndikukumbukira ndikuyenda chotsika ndi msewu kuno ndipo ine ndinkayankhula kwa winawake. Bambo anga—inu nonse mukudziwa zimenezo—iwo ankamwa; iwo ankapanga kachasu. Ndipo i—panalibe munthu amene anali ndi chochita ndi ine. Ine ndinkakhoza kupita chotsika mu msewu ndi

kuyesera kuyankhula kwa mwamuna; ine ndimakomana nayebe mwamuna ameneyo lero. Kuyesera kuti ndiyankhule kwa winawake, ngati palibe aliyense woti ayankhule naye, iwo ankakhoza kuima, “Eya, u, nhu.” Mukuona? Ine ndinali Branham.

²⁷¹ Chotero, ine ndinkamverera moyipa kwenikweni, ndipo ndinkapotoloka, ndi kuyenda kuchokapo. Ine ndinkaganiza, “Ine sindine wolakwa pa zimenezo. Ine sindinkachita zimene abambo anga ankachita. Ine sindinayambe ndamwapo mmoyo wanga. Chifuwa chiani kuti ine ndizikomana nazo zimenezo?” Ndipo ine ndinkamuza mkazanga kuno si kale litali, “Ine pafupifupi ndinkafuna kuti ndizikhala kunja kwa mzinda.” Mulungu wakhala wabwino kwa ine.

²⁷² Ine ndinaganiza uko kumene iye anamuza Natani atakhala kumeneko nthawi ina. Natani... Davide anati, “Kodi ndi koyenera kuti ine ndizikhala mu nyumba ya mkunguza ndipo likasa la Mulungu liri pansu pa hema kunja uko litaphimbidwa.” Iye...

Natani, mneneri, anati, “Davide, chita zonse zimene ziri mu mtima wako, chifukwa Mulungu ali ndi iwe.” Mneneriyo analakwitsa, osati mwakufuna.

Usiku umenewo Ambuye anabwera kwa mneneri, anati, “Pita ukamuze wantchito wanga Davide, ‘ine ndinamutenga iye kuchokera koweta nkhusa, akukusa nkhusa zochepa zija kunja uko; ndipo ine ndinamupatsa iye dzina longa munthu wamkulu amene alipo pa dziko lapansi. (Sananene konse kuti Iye anamupatsa iye dzina lokulitsitsa, Iye anangomupatsa iye dzina longa amuna otchuka amene analipo pa dziko lapansi.) Ine ndakuchitira zinthu zonse izi iwe, Davide. Ine ndawadula nkuwachotsa adani ako kulikonse kumene iwe umapita. Ine ndakhala ndiri pambali pa iwe. Ine sindinayambe ndakulepherapo iwe, ndipo ine sinditi ndikulephere iwe. Koma ine sindingati ndikulole iwe kuti umange mzinda.’”

²⁷³ Ine ndinaganiza za zimenezo, za malo tsopano kumene Mulungu wandithandiza ine ndi kundilola ine kuti ndidziwe anthu aakulu, kundirola ine kuti ndipite kuzungulira dziko. Ndipo anthu ochokera kozungulira dziko kumaitana kuti ndibwere ndidzawapempherere iwo, ndi anthu odwala, n—kufuna maminiti pang’ono ndi iwe, kumene zaka pang’ono zokha zapitazo sakanati ngakhale atembenuze—iwo kuti atembenuze mutu wawo kuti andiwone ine pa msewu. Ndipo tsopano, amuna amalonda akulemera chifukwa cha anthu amene ine ndikuwabweretsa mu mzindawu ndi kukhala nawo kuno, kudzera mu zakudya zawo ndi zolipiridwa ku motelo, ndi zinthu monga izo, kukhala—kupita ku mamotelo ndi kozungulira mzindawu ndi zinthu monga izo.

²⁷⁴ Anthu amene. . . Anthu sankandikonda ine nkomwe; palibe yemwe anali nane chochita. Ndipo tsopano, mwa thandizo la Mulungu, ine ndikukhulupirira kuti ine ndikulondolera Mkwatibwi wa Yesu Khristu. O. “Chisomo chodabwitsa, kukoma kwake kuchimva.”

²⁷⁵ Kodi izo zachokera kuti? Maphunziro anga? Ine ndiribe aliwonse. Kodi izo zachokera kuti? Umunthu wanga? Ine ndiribe uliwonse. Kodi izo zabwera kuchokera ku kudziwa kwanga kwa zamulungu? Ine sindidziwa zirizonse. Kodi izo zafika ku chiani? Chisomo cha Mulungu chimene chinandipulumutsa ine.

Ndi chisomo chinaphunzitsa mtima wanga
kuti ndiziwopa,
Ndi chisomo chachotsa mantha angawo;
Kukondwa kwake momwe chisomo icho
chinawonekera,
Ora limene ine ndinakhulupirira koyamba.
Kudutsa mu ngozi zambiri, kuvutikira, ndi
misampha,
Ine ndabwera kale;
Ndi chisomo chimene chinandibweretsa ine
motetezeka patali chonchi,
Ndi chisomo chiti chinditengere ine kwathu.
Ndipo pamene ife tikakakhala tiri uko mu
Mzindawo zaka zikwi khumi,
Umene uli wowala kuposa dzuwa;
Ife sitidzakhala ndi nthawi yapang’ono kuti
tiyimbe matamando Ake,
Kuposa pamene ife tinkayamba kumene.

O, momwe ine ndikumukondera Yesu, Dzina lokongola ilo limene linandipulumutsa ine pamene ine ndinali—wochimwa, limene linandichiza ine pamene ine ndinali kudwala, limene likundipatsa ine lonjezo la kwathu mu Mzinda umenewo. Ine ndiri nako kwathu mu Thanthwe limenelo. Palibe kanthu kenanso kali kofunikira tsopano koma kuwabweretsa ana onse a Mulungu palimodzi ndi kuti, “Tiyeni tizipita.” Ora, pakati pa usiku pakugunda; ndi mochedwa kuposa momwe ife tikuganizira. Tiyeni tipemphere.

²⁷⁶ Ambuye Yesu, kutseka kwa tsiku langwiwo. . . Momwe ife tikanayimira pamwamba pa phiri ndi kumaliyang’ana dzuwa, pamene milozo yofiira ikubwera mmwamba kudutsa mu mapiri aakulu akumadzulo kutaliko, pamene diso lalikulu likudzitseka lokha, mbalame nkuyamba kupanga ulendo wao waku chisa, nkubwerapo usiku. Ife taliwona tsiku lina lalikulu Lauzimu pamene Mzimu Woyera wakhala ukutithandiza ife kuti tiyankhe mafunso awa. Tsopano, ife tikupita ku chisa chathu, Ambuye. Tisamalireni ife; musati mulole kanthu kena katicanthe ife, Ambuye. Tisungeni ife kwa maserpenti a usiku ndi choipa.

Mulole Mulungu akhale pafupi nafe nthawizonse, akutitezera ife ndi kutithandiza ife.

277 Ine ndikupemphera, Atate akumwamba, kuti Inu mumudalitse wina aliyense amene wakhala ali mu msonkhanowu, iwo amene sakanatha, onse amene azidzamvetsera matepiwa. Mulole mafunsowa asakakhale olimba kwambiri. Ndipo ngati ine ndalakwitsa, Ambuye, Inu mukuwudziwa mtima wanga; ine sindimatanthauza kutero. Ine ndikupemphera, Mulungu, ngati pali chirichonse cholakwika, kuti Inu musachilole konse, musachilole konse kuti chipitirire; mukalole tepi ikaima. Musati mulole kuti ine ndimunyenge wina aliyense, Ambuye. Ndiroleni ine ndikhale wantchito Wanu woona, pakuti icho ndi chokhumba cha mtima wanga wonse. Kaya ine ndikhala moyo kapena ndifa, kaya ine ndichedwa kapena ine ndipita nazo, kaya ine ndigona kapena kaya ine ndidzakhala ndiri maso pamene Iye azibwera, izo ziribe kanthu kwa ine, Atate, kufuna Kwanu kuchitidwe. “Pakuti ine ndikudziwa kuti muwomboli wanga ali Moyo, ndipo pa masiku otsiriza Iye adzaima pa dziko lapansi ili. Ndipo ngakhale mphutsi za mkhungu zitawononga kale thupi ili, komabe mu mnofu wanga ine ndidzamuwona Mulungu.” Ameneyo anali mneneri Yobu pamene iye anakuwona kudza kwa Ambuye.

278 Ndipo, Ambuye, lero monga antchito Anu, ife tikuyang’anira ndipo tikukuwona kudza Kwanu. Kotero izo ziribe kanthu kwa ife, Ambuye, liti, motani, kuti. Ife tikungofuna kuti tizikukondweretsani Inu. Ife tiri mmanja Mwanu. Tisungeni ife, Ambuye, mpaka dzuwa lituluke. Perekani izi, ndiyeno ife tonse tiziguba waku Zioni kumene Mzinda uwo uli kumene Mwanawankhosa ali Kuwala.

279 Ana anga okonedwa pano, Ambuye, amene ine ndawabalira kwa Inu kudzera mu nsinga za Baibulo, iwo ali chipatso cha Mawu awa. Iwo amandikonda ine, ndipo ine ndimawakonda iwo. Ndipo ine ndikudziwa kuti Inu mumatikonda ife tonse. Ife tikupemphera, Mulungu, kuti Inu mutipatse ife pakati kwambiri ndi Mawu Anu kuti ife tizikhoza kumamuwona Iye yekha. Perekani izi, Ambuye. Mutilole ife kuti tikhale ozadza kwambiri ndi Mawu Ake kuti Mzimu ukhoze kumatigwiritsa ife ntchito kulikonse pa malo aliwonse kuti tiziwonetsera Mawu aliwonse amene Iye wawalonjeza. Perekani izo kwa ife tonse. Kuno pa omvetsera awa apa . . .

280 M’bale wanga Jackson azibwerera tsopano, kutali komwe uko mu South Africa. Pitani naye iye ndi mkazi wake; khalani muli nawo iwo, Ambuye. Atsogolereni iwo pa ulendo wawo.

281 Apa pali M’bale Lee Vayle akulemba, akuika mawu aliwonse amene ine ndikuwanena apo, kuyesera kuti apange bukhu. O, Mulungu, muthandizeni M’bale Vayle ndi Mlongo Vayle.

²⁸² Apa pali abale awa ochokera uko m—mu Arkansas, n—ndi a Martin apaubale, n—ndi—abale ena onse awa. Ine ndikupemphera kuti Inu mukhale nawo wina aliyense wa iwo.

²⁸³ Khalani naye M'bale Neville, M'bale Capps, M'bale Ruddell, M'bale Jackson, onse. O, Mulungu, pali ochuluka kwambiri. Iwo amabwera kuchokera ku Georgia, kuchokera ku Alabama, ndi kudutsa dzikoli ndi kuzungulira dziko. Ife tikuganiza za nyimbo:

O, iwo achokera Kummawa ndi Kumadzulo;
 Iwo achokera ku maiko akutali;
 Kudzadya ndi Mfumu yathu,
 Kudzadya ngati alendo Ake, (Iye wawaitanira
 iwo kuti adzagawane nawo za Iyemwini.)
 Kudala kwake amwendamnjira awa momwe
 aliri.
 Kumayang'ana nkhope Yake yolemekezeka,
 Ikuwala ndi chikondi chaumulungu;
 Ogawana nawo modala a chisomo Chake,
 Monga ngale mu korona Wake kuti aziwala.

²⁸⁴ O, Mulungu, mulole ife tiwale chotero monga ngale mu korona Wake, kuti ena akhoze kuwona ndi kumakhumba kuti azimutumikira Iye. Perekani izi, Ambuye. Atetezeni iwo pa njirayi. Mudalitseni wina aliyense.

²⁸⁵ Ndipo Atate, pa nthawi yanu yoikika...Ine ndine wantchito wanu. Ngati inu mukufuna ine kuti ndipitirize izi sabata lotsatirali kapena kuti ndidzatenge zoyankhulana zija, uwululirani kwa ine, Ambuye, ndipo ndiroleni ine kuti ndidziwe pakati pa tsopano ndi Lachitatu chotero kuti ife tikhoze kumvetsa. Perekani izi, Atate, kuti anthu akhoze kudwabwera. Ndipo ine ndikupempherera mdalitso uwu kuti Inu mutithandize ife n—ndipo mukomane nafe ife kachiwiri kuno pa nthawi ya kusonkhana kwathu kwina.

²⁸⁶ Khalani naye M'bale Neville ndi amuna awa amene akubweretsa Mawu kutali uko mu Texas, ndi uko mu Arkansas, ndi malo osiyana; ingokhalani nawo iwo, Atate. M'bale Peary Green ndi gulu lonse ilo kumeneko, k—khalani nawo basi onse a iwo, Ambuye; iwo ndi ana Anu aang'ono. Kulikonse kuzungulira mdziko iwo akudikirira kudza Kwanu. Tithandizeni ife, Atate ife tikupemphera, pamene ife tikudzipereka tokha kwa Inu. Mu Dzina la Yesu tigwiritseni ife ntchito. Amen.

²⁸⁷ Ine ndimaikonda nyimbo ija, *Abwera Kuchokera Kummawa ndi Kumadzulo*. Ndi angati akuidziwa iyo? Ine sindikudziwa momwe ine ndimaidziwira iyomo, koma ine ndikuganiza ndikudziwa ndime. Inu mukhoza kuiyamba iyo, Mlongo. Ine sindikudziwa ngati iwo angaithe iyo.

Kummawa ndi Kumadzulo;
 Achokera kutali,
 Kudzadya ndi Mfumu,
 Monga alendo Ake,
 Amwendamnjira odala.
 Kuwona nkhope Yake,
 Yowala ndi chikondi;
 Ogawana achisomo Chake,
 Ngale mu korona Wake.

O, Yesu akubwera;
 Mayeso athu adzatha.
 Ambuye akadza nthawi iyi
 Kwa omasuka ku tchimo.
 Zibweretsa chisangalalo,
 Pena chisoni ndi mantha?
 Pakudza mu Ulemerero,
 Tidzakomana mlengalenga. (Kodi inu
 mukuikonda iyo? Tiyeni tiyese iyo kachiwiri.)

Kummawa ndi Kumadzulo;
 Achokera kutali,
 Kudzadya ndi Mfumu,
 Monga alendo Ake,
 Amwendamnjira odala.
 Kuwona nkhope Yake,
 Yowala ndi chikondi;
 Ogawana achisomo Chake,
 Ngale mu korona Wake.

O, Yesu akubwera;
 Mayeso athu adzatha.
 Ambuye akadza nthawi iyi
 Kwa omasuka ku tchimo,
 Zibweretsa chisangalalo, pena chisoni ndi
 mantha?
 Pakudza mu Ulemerero,
 Tidzakomana mlengalenga. (Ndi angati
 akufuna kuti adzakomane naye Iye
 mmwamba umo? O, mai!)

O, Yesu akubwera; (Ingotsekani maso anu ndi
 kumalingalira kuti inu mukulimva lipenga
 likuwomba.)
 Mavuto athu adzatha.
 Ambuye akudza nthawi iyi
 Kwa omasuka ku tchimo,
 Kaya zibweretsa chisangalalo, pena chisoni
 ndi mantha?
 Pakudza mu Ulemerero,
 Tidzakomana mlengalenga. (Inu mukuikonda
 iyo?)

288 Pat, khala wolimbamtima bwino! Lidzatulukira tsiku kwa inu limodzi la mmawa uwu. Ine sindinawone kumene izo zimapita, koma izo zimawoneka bwino. Ameni! Inu muli nayo nthawi yaitali, m'bale, izo zidzabwerera. Ndipo monga mkate pa madzi zidzabwerera kwa inu tsiku lina. Ndiko kulondola. Chabwino.

O, inu mukumukonda Iye?

Chikhulupiriro changa kwa Inu,
Mwanawankhosa wa Kalvare,
Mpulumutsi waumulungu!
Mundimve ndipempha,
Mndichotsere machimo,
Msalole ndichoke kumbali Yanu.

Poyenda mu mdima,
Nkhawa pondizinga,
Mkhale Namulondolera wanga,
Mdimu usanduke usana,
Zisoni zithawe,
Ndiloleni lero nkhale Wanu! (Kodi inu
simukuikonda imeneyo?)

Chikhulupiriro changa kwa Inu,
Mwanawankhosa wa Kalvare,
Mpulumutsi waumulungu!
Mundimve ndipempha,
Mndichotsere machimo;
Nsalole ndichoke kumbali Yanu.

Chodala ndi chimango (O, mai!)
Cha mitima yathu mchikondi;
Chiyanjano cha paubale
Chonga chija chakumwamba.

Ku mpando wa Atate
Titsanulira pemphero;
Mantha, ziyembekezo, zolinga nzimodzi,
Zitonthozo ndi zosamalira.

Koma pamene tisiyana,
Zimatipatsa kuwawa;
Koma tikhala amodzi mu mtima,
Kuyembekeza kukomanso.

289 Mlongo Wilson, inu mukukumbukira pafupi zaka sate-firii kapena sate-faifi zapitazo mu msonkhano waung'ono wa mnyumba ife tinkagwirana manja wina ndi mzake? Ine ndimadziwa kuti inu mukukumbukira zimenezo. O, tiyeni tingofikira apo tsopano ndipo kumugwira winawake pa dzanja.

Chodala ndi chimango
Cha mitima yathu mu chikondi;
Chiyanjano cha apaubale
Chonga chija chakumwamba.

Ku mpando wa Atate
Titsanulira pemphero;
Mantha, ziyembekezo, zolinga nzimodzi,
Zitonthozo ndi zosamalira.

Pamene tisiyana,
Zimatipatsa kuwawa;
Koma tikhala amodzi mu mtima,
Kuyembekeza kudzakomanso.

Kodi inu mukukondana wina ndi mzake? Ana aang'ono, zikondanani wina ndi mzake.

Mpaka tidzakomane, mpaka tidzakomane,
Tidzakomane pa mapazi a Yesu;
Mpaka tidzakomane, mpaka tidzakomane,
Mulungu akhale nanu mpaka tidzakomanenso.

²⁹⁰ Inu mukumukonda Iye? Kodi Iye si wodabwitsa? Inu mukukondana wina ndi mzake? Fikirani pozungulira, nenani chinachake kwa wina ndi mzake. Kuti, “Mulungu akudalitseni inu, M'bale. Akudalitseni inu, Mlongo.”

²⁹¹ Iwo akumvetsera kwa ife usikuuno kuwoloka mtsinje kutaliko, Mlongo Wilson. Ine ndikukhoza kumuwona M'bale Seward wachikulire akuyenda pabwalopo, akuwomba manja ake. Ine ndinamuwona m'bale wathu kumbuyo uko ali ndi ndevu pa nkhope yake akukweza mmwamba manja ake, akuthokoza Mulungu; ine ndinaganiza za M'bale Ryan, momwe iye anakondera kukhala apo pomwe mu kachisi wakaleyo ali ndi ndevu zake zazitali zonga choncho. Iye akumvetsera usikuuno kudutsa ku makonde a Ulemerero, wokonedwa woyera wakale. Kodi Iye si wodabwitsa?

Tenga Dzina la Yesu nawe,
Mwana wa chisoni ndi tsoka;
Likusangalatsa ndi kutonthoza,
Litenge kulikonse upita.


Dzina lofunika, kukoma kwake!
Chiyembekezo cha padziko chisangalalo cha
Kumwamba,
Dzina lofunika, kukoma kwake!
Chiyembekezo cha padziko chisangalalo cha
Kumwamba.

Tsopano, inu tengani Dzina la Yesu nanu. (Nla chiani?)
Chishango ku misampha. (Chimachitika ndi chiani?)
Pamene mayesero akuzingani,
Pumani dzinalo mwa pemphero.

Dzina lofunika, kukoma kwake!
 Chiyembekezo cha padziko chisangalalo cha
 Kumwamba,
 Dzina lofunika, kukoma kwake!
 Chiyembekezo cha padziko chisangalalo cha
 Kumwamba.

[M'bale Branham ayankhula ndi winawake mwa onsonkhana—Mkonzi.]

²⁹² Pa zoyankhulana: Billy anati muwonane naye iye pakati pa pakali pano ndi Lachitatu pofuna zoyankhulana kapena kuyambira Lachitatu kupitirira mpakana Loweluka pa zoyankhulana zimene zikubwerapo, kaya . . . Ngati ife sitikhala nayo misonkhano pambuyo pa Lachitatu, fufuzani ndi iyeyo, inu amene muli nazo zoyankhulana. Ena a inu, iye sakudziwa momwe iye angakupezereni inu. Kotero iye anga . . . Onse amene akufuna kuyankhulana tsopano, fufuzani ndi Billy.

²⁹³ Inu mukumukonda Iye? Chabwino. Tsopano, mpaka tidzakomane, Mulungu akudalitseni inu. Ife tikufuna kuti tiweramitse mitu yathu; ndipo ine ndimufunsa mzanga wabwino, womvera, amene akupita kuwoloka nyanja tsopano, kutali komwe mu Afrika, kumene ine kamodzi ndinakachita umishonare kumeneko mu Dzina la Ambuye, M'bale Sidney Jackson, iye ndi mkazi wake . . . Ife takhala okondwa kwambiri kukhala tiri nawo iwo ndi ife pa misonkhano ingapo yapitayi. Momwe Mulungu wamudalitsira iye. Ndipo ine ndikuti ndimufunse M'bale Sidney Jackson ngati iye angawabalalitse omvetsera awa mwa pemphero. M'bale Jackson, ngati inu mungalolere. 

Khalidwe Dongosolo ndi Chiphunzitso cha Mpingo, Bukhu Lachiwiri
(Conduct, Order And Doctrine Of The Church, Volume Two)

Mauthenga awa a M'bale William Marrion Branham olalikidwa ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., anatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito ndipo anadindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingelezi. Ndipo kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice of God Recordings.

CHICHEWA

©2009 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org